

KUKUZA MAONEDWE

A

ZINTHU MALINGANA NDI BAIBULO

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe ntchito Ka bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira limodzi Pagulu.....	4
Mau oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	5
1. Pachiyambi.....	6
2. Dziko Logawanika.....	17
3. Kuona Zinthu Mmene Mulungu Amazionera.....	23
4. Maonedwe A Dziko Lapansi Mu Chuipangano Chakale.....	30
5. Dziko Mu Mau a Mulungu: Chipangano Chatsopano.....	48
6. Mpingo Mu Dziko Lapansi.....	60
7. Dziko Loyembekeza	76
8. Kukhala Nkhristu Wa Dziko Lonse.....	88
9. Opembedzera Dziko Lonse.....	102
10. Kugawana Ndi Ena Maonedwe a Dziko Malingana Ndi Baibulo.....	115
11. Chimaliziro Chidzabwera.....	132
12. Mayankho amafunso odziyesa nokha.....	141

KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogololera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: Ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

PHUNZIRO: KUKUZA KAONEDWE KAZINTHU MALINGANA NDI BAIBULO.

MAU OYAMBA

Phunziro ili ndi phunziro loyamba mu maphunziro a gawo lachitatu la Harvestime International Institute. Gawo loyamba limakamba za masomphenya a kholora lauzimu. Maphunziro a gawo lachitatu amene phunziro ili likupezeka, limafotokoza mmene mungaphunzitsire antchito akholora lauzimu amene akhonza kukaphunzitsa anthu ena:

Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (Timoteo 2:2)

Ndondomeko yopitilira pophunzitsa anthu ena imatchedwa “kuchulukitsa” chifukwa imachulukitsa antchito akholora lauzimu.

Kuona zinthu Malinga ndi Baibulo ndi nsanamira yakuchulukitsa. Kukhala ndi ndi maonedwe azinthu malingana ndi Baibulo zimatanthauza kuliona dziko malingana ndi zimene za bvumbulutsidwa mu Baibulo. Zinthu simumazona ngati mmene amazonera anthu andale, a geni kapena anthu a zamaphunziro. Simumaona zinthu malingana ndi chikhalidwe chanu, koma zinthu zimaonedwa malingana ndi mmene Mulungu amaonera zinthu kapena mmene amaonera dziko lapansi. Kukuza kumatanthauza kuonjezera zinthu mu gawo lina Lake. Kotero phunziro ili likuza chidziwitso chanu chadziko limene mumakhala ndi cholinga chofuna kuchulutsa atchito ogwira tchito yauzimu.

Buku ili likufotokoza maonedwe azinthu amene abvumbulutsidwa mu Baibulo, mau a Mulungu olembedwa. Ndipo likufotokoza zankhaniyi kuchokera Buku la Genesis mpaka la Chibvumbulutso. Likufotoza cholinga cha Mulungu pa mayiko a dziko lapansi kuchokera pachiyambi ndi chimaliziro cha nthawi. Phunziro ili likufotokozanso za udindo wa anthu okhulupilira pa mayiko a dziko lapansi pofotokozera mfundo yakukhala okhulupilira wa dziko lonse lapansi.

Maphunziro amene ali mubukuli akukamba mmene zinthu zililiri kumoyo wauzimu dziko lonse lapansi, ndipo akutsindika kufunika kolalika uthenga Wabwino mwamachawi kwa anthu amene sanafikilidwe pa dziko lapansi. Phunziroli likutsindikanso za udindo wa mpingo pano pa dziko lapansi komanso kuti ife tione zinthu mmene Mulungu amazionera. Chikhulupiliro chopanda ntchito chili chabe (Yakobo 2:26) chifukwa cha ichi, kuziona zinthu malingana ndi Baibulo kukhoza kukhala kopanga ntchito ngati inuyo simutengapo mbali. Maphunziro amenewa akusunthani inu kuchoka munthu ongopenyelera ndikukhala otengapo mbali pazimene Mulungu akuchita.

ZOLINGA ZAMAPHUNZIROWA

Pamene mudzamalize maphunziro awa muyenera kukwalitsa zinthu izi:

- Kuliona dziko lapansi mmene Mulungu amalionera
- Kudziwa mwachidule zimene Baibulo limaphunzitsa za dziko lapansi.
- Kuonetsa kuti mwamvetsa zolinga za Mulungu pa mayiko a dziko lapansi
- Kutenga udindo wanu pofalitsa uthenga waufumu wa Mulungu pa dziko lonse lapansi.
- Kukhala okhulupilira wa dziko lonse lapansi.
- Kutumikira kudzera kupembedzera dziko lonse lapansi.
- Kugawana ndi ena maonedwe azinthu malingana ndi Baibulo.

CHAPUTALA 1

PACHIYAMBI

ZOLINGA:

- Pamapeto pamaphunziro awa muyenera kukwanitsa zinthu izi:
- Kulemba vesi yotsogolera kuchokera pamtima.
- Kuzindikira Mmlengi wa dziko lapansi ndi anthu onse.
- Kupereka zifukwa zopangitsa nkhani zosiyanasiyana za chiyamabi cha zinthu zolengedwa.
- Kufotokoza chifukwa chimene anthu ena amakanira kuvomeleza zimene Baibulo limaphunzitsa pa zakulengedwa kwa zinthu.
- Kufotozoza tanthauzo la “kuona zinthu malingana ndi Baibulo”
- Kufotokoza mmene Mulungu analengera zinthu mumasiku asanu ndi awiri akulenga.
- Kufotokoza malo ake enieni amunthu komanso cholinga chimene analengedwera
- Kufotokoza mwachidule “zakugwa kwa munthu”
- Kufotokoza za zotsatira za kugwa kwa munthu.
- Kupeza ndime zofotokoza malingaliro a Mulungu ndi dziko lapansi.
- Kupeza magawo awiri amoyo amene anthu onse amakhala.

VESI YOTSOGOLERA

PACIYAMBI Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi. (Genesis 1:1)

MAU OYAMBA

Kaonedwe kazinthu kapena kadziko ka anthu ambiri ndikoperewera. Ambiri amangokhudzika ndi zochitikaka zinthu zokhudza mudzi wao okha, kapena dziko lawo lokha. Iwo samazindikira kuti dera limene amakhala ndi gawo lalingo’no la dziko lapansi. Samadziwa dongosolo la

Mulungu lokhudza dziko lonse lapansi, anthu amitundu yonse, komanso zikhalidwe ndi zilakhulo zonse.

Chaputala ichi chiyamba kufotokoza chiyambi cha dziko limene timakhala, komanso chikuyamba kufotokoza za kulengedwa kwa dziko kenako kwa munthu amene amakhala mudzikolo. Ndipo chaputala chawiri chimafotokoza za mmene dziko lapansi limagawanikira ndikukhala ndi mayiko ndi zilakhuro.

NTHANO ZOKHUDZA CHIYAMBI CHA DZIKO

Chikhalidwe chilichonse chili ndi zikhulupiliro zosiyanasiyana zokhudza kulengedwa kwa dziko lapansi. Anthu akhala akuyesayesa kufuna kufotozo zachiyambi cha munthu komanso dziko lapansi. Kotero anthu azikhalidwe zosiyanasiyana anapeka nthano zao pofuna kufotokoza za chiyambi chachilengedwe. Nthano zimenezi zimapekedwa pazifukwa izi:

1. Anthu samadziwa zoonza zenizeni zokhudza chilengedwe kapena
2. Anthu anasankha kusakhulupilira zoonza zake za chilengedwe angakhare anauzidwa.

Za Mulungu Mlengi.

Nkhani yeniyeni yakulengedwa kwa zinthu zonse imapezeka Buku la Genesis 1:1 akufotokoza za nkhani yonse imene ikupezeka muchaputapara choyambachi.

Pachiyambi Mulungu analenga dziko lapansi ndi lakumwamba (Genesis 1:1)

Mulungu amene akukambidwa apa ndi Mulungu yekhayo owonadi. Baibulo ndi mau a Mulungu olembedwa komanso zimene iye anachita. Pamene tikukamba zakukhala ndi maonedwe a zinthu malingana ndi Baibulo, tikutanthauza kaonedwe kathu kazinthu kamatsamira pa zimene zabvulumbulitsidw mu Baibulo.

Anthu ena amasankha kusakhulupilira choonadi chimene Baibulo limafotokoza chifukwa izi zimatanthauza kuti ayenera kubvomeleza kuti Mulungu alipo. Ngati anthu angabvomeleze kuti Mulungu alipo, amayenera kulolera kuti Iye alamulire iwo. Koma chifukwa chakusafuna kusintha makhalidwe, anthu amatha kusankha kusakhulupilira zimene Baibulo limafotokoza pa zakulengedwa kwa munthu ndi dziko lapansi komanso kuti Mulungu alipo.

Anthu enanso amanena kuti zimene Baibulo limafotokoza ndizosemphana ndi zimene akatswiri a science anapeza. Inde ndi zoonadi kuti Baibulo limasemphana ndi zimene akafukufuku wa science amafotokoza, koma zina zimene akatswiri a science amakhulupilira ndi zinthu zimene iwo amangoganizira pofuna kufotokozera zinthu. Ndipo zina mwazinthu zimene amakhulupilira zimakhala zopanda umboni ogwirika. Koma kafukufuku wambiri wa akatswiri a science wakhala akuonetsera kuti zimene Baibulo limafotokoza pa za kulengedwa kwa zinthu ndi zoonadi ndithu,

KULENGEDWA KWA DZIKO LAPANSI

Buku la Genesis limafotokoza mmene dziko lapansi linaliri Mulungu asanayambe kulenga.

Dziko lapansi ndipo linali lopanda kanthu; ndipo mdima unali pamwamba pa nyanja; (Genesis 1:2)

Mavesi ali munsiwa amafotokoza mmene dziko lapansi linalengedwera:

Tsiku loyamba: kuwala ndi mdima (vesi 3-5).

Tsiku lachiwiri: Thambo (Kumwamba) kulekanitsa madzi ndi madzi (verses 6-8).

Tsiku lachitatu: Nthaka ndi zomera (vesi 9-13).

Tsiku lachinayi: zonse zamulengalenga; dzuwa, mwezi, nyenyezi (vesi 14-19).

Tsiku lachisanu: zolengedwa za mmadzi ndi mlengalenga (vesi 20-23).

Tsiku lachisanu ndi chimodzi: Nyama zonse zapanthaka ndi munthu (vesi 24-25)

Baibulo limafotokoza za kulenga kwa Mulungu pofuna kuonetsa kuti ...

Pakuti mwa iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa iye ndi kwa iye. Ndipo iye ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa iye. (Akolose 1:16-17)

KULENGEDWA KWA MUNTHU

Patsiku lachisanu ndi chimodzi Mulungu analenga cholengedwa choposa zolengedwa zonse. Analenga munthu muchifanizo chake.

Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'cifanizo cathu, monga mwa cikhalidwe cathu: alamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa ng'ombe, ndi pa dziko lonse lapansi, ndi pa zokwawa zonse zakukwawa pa dziko lapansi. Mulungu ndipo adalenga munthu m'cifanizo cace, m'cifanizo ca Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi. (Genesis 1:26-27)

Mulungu analenga munthu oyamba, Adamu kuchokera ku fumbi ndipo anamuuzira iye mpweya kuti akhale ndi moyo. Mulungu analengaso mzimayi oyamba kuchokera kwa Adamu. Werengani kulengedwa kwa Hava pa Genesis 2: 18-25.

CHOLINGA CHA MULUNGU POMULENGA MUNTHU.

Masiku akalero, mafumu amasema zifananifani za iwo eni makamaka mu madera amene iwo samakwanitsa kupezekako. Munthu analengedwa muchifaniziro cha Mulungu nayikidwa padziko lapansi kuti akhale Kazembe wa Mulungu. Ndipo ngati Kazembe wa Mulungu, munthu anapatsidwa ulamuliro pa zonse zomera ndi zinyama zadziko lapansi.

Munthu anapatsidwa udindo wapaderadera. Iye amayenera kuti ali dzare dziko ndi anthu ena amene amayera kuonetsera chifanizo cha Mulungu mwa iwo.

Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, Mubalane, mucuruke, mudzaze dziko lapansi, muligonjetse: mulamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakukwawa pa dziko lapansi. (Genesis 1:28)

Munthu ndi cholengedwa choposa zolengedwa zonse ndipo analengedwa muchifanizo cha Mulungu, ali ndi moyo wa muyaya umene nyama sizimakhala nao. Alinso ndi mzimu ndi maganizo zimene zimampangitsa kutha kulakhula ndi Mulungu komanso kudziwa za Iye. Mzimu wa Mulungu umatsika ndi kumalakhula ndi munthu uja m'munda wa Eden umene munthu amakhalamo. (Genesis 3:8)

Chifukwa cha udindo wapaderadera umene munthu anapatsidwa, munthu amayenera kuti aonetsere Mulungu amene anamulenga iye muchifanizo chake. Munthu amayenera kulemekeza komanso kumalakhula ndi Mulungu:

Yense wochedwa dzina langa, amene ndinamlenga cifukwa ca ulemerero wanga; ndinamuumba iye; inde, ndinampanga iye. Iwe sunanditengere Ine zoweta zazing'ono za nsembe zopsereza zako; kapena kundilemekeza ndi nsembe zako. Sindinakutumikiritsa ndi nsembe zaufa, kapena kukutopetsa ndi zonunkhira. (Yesaya 43:7,23)

KUGWA KWA MUNTHU

Chaputala 3 cha Genesis chimafotokoza nkhani yokhumudwitsa kwambiri. Chaputara ichi chimafotokoza za “Kugwa kwa munthu.” Munthu analengedwa m’chifanizo cha Mulungu. Mwachitsanzo, Mulungu ali ndi ufulu opanga chiganizo chimene akufuna, chomwechonso munthu ali ndi ufulu opanga chiganizo chimene akufuna.

M’ munda wa Eden umene Adamu ndi Hava amakhala, munali mitengo yambiri. Koma panali mitengo iwiri yapaderadera. Umodzi mwa mitengo imeneyi umatchedwa mtengo wa moyo (Genesis 3:22). Kotero kuti Adamu anakadya mtengo umeneu, anakakhara ndi moyo kwa muyaya, sakanafanso ndithu.

Mtengo wina unali mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa. (Genesis 2:17) Mulungu anachenjeza Adamu ndi Hava kuti asadye Chipatso cha mtengo umeneu chifukwa Iye sanafune iwo kuti akumane ndi zowawa zodza chifukwa cha uchimo. Mulungu anachenjezelatu kuti zotsatira zakudya chipatso cha mtengo umeneu ndi imfa.

Ngakhale Mulungu anachenjeza zotsatira zakudya chipatso cha mtengo umenewu, Munthu anasankha kusamvera chenjezo la Mulungu. Satani ndi mdani wake wa Mulungu amene pachiyambi anali mngelo wabwino wa Mulungu, koma iye anafuna kufanana ndi Mulungu. Satana anatsogolera kugalukira kwa angelo kumwamba. Mukhoza kuwelenga zambiri pa (Yesaya 14:12-17)

Satana sanafune kuti munthu atumikire Mulungu. Koyamba anadza kwa mkazi kenako kwa mamuna ndi cholinga chofuna kuwanamiza. Iye anawayesa iwo powapatsa malonjezano abodza. Koma iwo anagwa mmayeselo ndipo anachimwa pakudya chipatso cha mtengo wakudziwitsa chabwino ndi choipa.

Zotsatira za kugwa kwa munthu kunasintha dziko lonse lapansi. Zomera zinayamba kumelera pali ponse. Zinyama zinayamba kukhala zolusa komanso zoopsya. Angakhale nyengo imene inasinthanso pamene zinthu ngai kusefukila kwa madzi kunayamba kuoneka komanso ndi ngozi zina zogwa mwadzidzi.

Zinthu zonse zoyipa zapadziko lapansi kuyambira, mabvuto, ngozi kapena miliri yonse, ikudza chifukwa cha kuchimwa kwa munthu. Pamene uchimo umalowa dziko lapansi, unadzanso ndi mabvuto. Komanso chilango cha imfa chinapekedwa kwa munthu ngati mmene Mulungu anachenjezera. Chifukwa cha ichi anthu onse ayenera kufa kuthupi mpaka pachimaliziro cha nthawi.

Chotsatira chatchimo choopsya kwambiri ndiko kulekaninitsidwa kwa munthu ndi Mulungu. Chifanizo cha Mulungu mwa munthu chinasokonekera. Chifukwa cha tchimo munthu anaphwanya ubale umene unali pakati pa iye ndi Mulungu.

LONJEZANO LALIKULU

Munyengo yopanda chiyembekezo mumbiri ya munthu, Mulungu anapereka lonjezo lalikulu. Mulungu anati kwa Satana:

ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace. (Genesis 3:15)

Ili linali bvumbulutso lapaderadera lachikonzero cha Mulungu. Izi zinabvumbulutsa kuti udani pakati pa satana ndi munthu udzakhala ukupitilirabe kwa zaka zambiri. Koma mukupita kwa nthawi, Mulungu anatuma wina kuti agonjetse mdani wa munthu ndikumbwezeletsa ubale wa munthu ndi Mulungu. Ndipo winawakeyo ndiye Yesu Khristu. Muphonzira zambiri zadongosolo la Mulungu pa anthu onse pamene mupitiliza kuphonzira phunziroli.

MAYIKO AWIRI

Genesis 3:15 akubvumbulutsa mfundo yina yofunika kwambiri, anthu onse amakhala mayiko awiri. Munthu amakhala mu magawo awiri. Gawo loyamba ndi lakuthupi limene limaoneka ndi maso komanso munthu amakhala dziko lauzimu losaoneka ndi maso. Ngakhare kuti silioneka, koma ili ndi dziko lenileni limene munthu amakhalamonso ngati mmene akhalira kudziko lakuthupi

Munthu wina aliyese ali ndi nthupi limene limakhala kudziko lakuthupi, koma mukuyenera kukumbukira kuti Munthu analengedwa ndi mzimu komanso moyo. Choncho, moyo ndi mzimu ndi zimene zipanga dziko lauzimu.

Pa Genesis 3:15, mau oti kulalira akuonetsera nkondi yaikulu mudzio lauzimu ndipo iyi ndi nkondo yolimbilana mzimu, moyo, maganizo ndi mtima wa munthu. Ndipo pa nkondo imeneyi, anthu onse ali ku mbali ziwiri zotsutsana. Yesu analakhura nati:

Palibe munthu, atayatsa nyali, aiika m'cipinda capansi, kapena pansu pa muyeso, koma pa coikapo cace, kuti iwo akulowamo aone kuunika. (Luka 11:33)

Kuti mukunze maonedwe azinthu malingana ndi Baibulo muyenera kumvetisa mfundo izi:

1. Muyenera kuzindikira kuti anthu onse amakhala kudziko lakuthupi komanso lauzimu.
2. Nkhondo imene imachitika kudziko lauzimu imakhudzanso dziko lakuthupi limene timakhala. Satana amakangalika kugwira nchito kudziko lauzimu ndipo izi zimaonekera kuthupi kudzera mu zinthu zoyipa zimene anthu amachita.
3. Pankhondo imeneyi palibe amene amakhala pakatikati. Mukhoza kukhala mbali ya Yesu Khristu kapena otsutsana naye. Ndipo ngati tili mbali ya yesu ndiye kuti ife timakhulupilira zimene mau a Mulungu amaphunzitsa komanso timachita zinthu malingana ndi Malemba. Ngati sitikhulupilira mau a Mulungu komanso kupanga zimene thupi lathu likufuna, ndiye kuti ifeyo tikupanga motsutsana ndi Mulungu.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera ya muchaputara ichi

2. Kodi analenga dziko lapansi ndi munthu ndi ndani?

3. Perekani zifukwa ziwiri zopangitsa kuti pakhale nthano zosiyanasiya zofotokozera chiyambi cha chilengedwe.

4. Ndichifukwa chani anthu ena amakana kubvomeleza zimene Baibulo limafotokoza zokhuzda chiyambi cha zolengedwa?

5. Kodi mau akuti “kuona zinthu malingana ndi mau a Mulungu” amanthauza chani?

6. Fotokozani mwachidule mmene Mulungu analengera zinthu kwa masiku asanu ndi limodzi

Tsiku loyamba: _____

Tsiku lachiwiri: _____

Tsiku lachitatu: _____

Tsiku lachinayi _____

Tsiku lachisanu: _____

Tsiku lachisanu ndi chimodzi: _____

7. Kodi chimamusiyantsa munthu ndi zolengedwa zina ndi chani?

8. Fotokozani mwachidule nkhani ya kugwa kwa munthu.

9. Kodi zotsatira za kuchimwa kwa munthu zinali chani?

10. Tchulani magawo awiri amene munthu amakhala

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Mukhonza kuphunzira zambiri zokhudza chiyambi cha dziko komanso Mulungu ngati olenga powerenga ndime izi za mu Baibulo.

MULUNGU ANALENGA DZIKO LAPANSI:

Genesis 1:1-32; 2:3-4; 5:1-2

Yeremiya 9:6

Yobu 38:1-41

Masalimo 74:17; 89:11; 104:1-35; 115:15; 121:2; 124:8; 134:3; 136:6; 148:5

Miyambo 8:23-31

Mlaliki 3:11

Yesaya 40:28; 42:5; 43:1,7; 44:24; 45:8,12,18; 48:13; 54:16; 65:17

Yeremiya 10:12; 27:5; 31:22; 32:17; 51:15

Ezekiyele 28:13, 15

Amosi 4:13

Zakaliya 12:1

Malaki 2:10

Yohane 1:3

Machitidwe 4:24; 17:24

Aroma 1:20

Aefeso 2:10; 3:9; 4:24

Chibvumbutso 10:6

MULUNGU AMASUNGA DZIKO NDI MPHAMVU YAKE.

Masalimo 75:3; 95:4

Akolose 1:16-17

Aheberi 1:3; 6:7

II Petro 3:4

Chibvumbulutso 4:11

CHAPUTALA 2

DZIKO LOGAWANIKANA

ZOLINGA:

Pamapeto pa chaputara ichi, muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yoloweza yotsogolera
- Kufotokoza mmene dziko linagawanikira ndi zilankhulo zosiyanasiyana.
- Kufotoza mmene kusiyana kwa zilankhulo kunapangitsira chiyambi cha ma gulu a anthu osiyanasiyana.
- Fotokozani mmene magulu a anthu apangira mayiko adziko lapansi

MA VESI OTSOGOLERA

Ndipo onse ali naco cinenedwe cao cimodzi; ndipo ici ayamba kucita: ndipo tsopano palibe kanthu kakuletsedwa nao kamene akafuna kucita. Tiyeni, titsike, pomwepo tisokoneze cinenedwe cao, kuti wina asamvere cinenedwe ca mnzace.

(Genesis 11:6-7)

MAU OYAMBA

Mu chaputala changopitacho, munaphunzira za kulengedwa kwa dziko lapansi ndi munthu. Komanso munaphunzira za kuchimwa kwa munthu. Pamene Adam ndi Hava anayamba kubeleka, ana amene amabadwao, naonso amabadwa ndi chikhalidwe cha uchimo. Munthu sanalinsu wabwino ngati mmene analengedwela pachiyambi. Maganizo ndi ntchito za munthu zinayamba kukhala zauchimo. Pachiyambi, azimayi ndi azibambo amakhala banja limodzi lalikulu. Koma pakupita kwa nthawi, dziko lapansi linagawikana potengera zilankhulo, mayiko komanso mitundu ya anthu.

Mu chaputala changopitachi, munaphunzira za magowo awili adziko amene ali dziko lakuthupi ndi dziko lauzimu. Koma padziko lapansi ma gawo angapo amene amapezekanso.

Mwachitsanzo, dziko lapansi lagawidwa malingana ndi mayiko, zikhalidwe komanso zinenero zosiyanasiyana. Baibulo limafotokoza mmene kugawikana kumeneku kunabwelera

KUFALIKIRA KWA TCHIMO

Genesis 4:1-6:4 amafotokoza za kufalikira kwa tchimo pa dziko lapansi. Musanapitilire ndi phunziroli, muyenera kuwerenga ndime zimenezi mu Baibulo. Ndipo mu ndime zimenezi timapezamo kuphana koyamba, bodza loyamba komanso mmene kuyipa mtima kwa munthu kunafalikira ma gawo onse amunthu mpaka kufikira dziko lonse lapansi linagwidwanso ndi uchimo kufikira kuti Mulungu...

Ndipo anaona Yehova kuti kuipa kwa anthu kunali kwakukuru pa dziko lapansi, ndiponso kuti ndingaliro zonse za maganizo a mitima yao zinali zoipabe zokhazokha. Ndipo Yehova anamva cisoni cifukwa anapanga munthu pa dziko lapansi, ndipo anabvutika m'mtima mwace. (Genesis 6:5-6)

Chifukwa chakufalikira mwa changu kwa tchimo kudziko lapansi, Mulungu anaganiza kuti awononge dziko lapansi ndi madzi. koma Mulungu anapulumutsa Nowa ndi banja lake ku chigumula chimenechi. Welengani nkhani ya Nowa ndi chigumula yopezeka pa Genesis 6:8-9:17. Koma chitatha chigumula chija, Nowa ndi banja lake anayamba kubelekana komabe uchimo unapitilirabe.

NSANJA YA BABULO

Kufikilabe nthawi imeneyi, anthu okhala padziko amakhalabe ngati banja limodzi lalikulu.

Ndipo dziko lapansi linali la cinenedwe cimodzi ndi cilankhulidwe cimodzi. (Genesis 11:1)

Panalibe kusiyana kwa zinenelo kapena chikhalidwe pakati pa anthu adziko lapansi. Mayiko nthawi imeyo anali ndi chiyakhulo chimodzi komanso chikhalidwe chofanana. Ndipo anthu amenewa anapangana kuti amange nsanja yokwera mwamba ndi cholinga choti amufikire Mulungu. Iwo cholinga chao chinali kufuna kutchuka. Mukhoza kuwelenga nkhani imeneyi pa Genesis 11:1-9

Mulungu anadziwa za mpamvu ya chilakhulo ndi chikhalidwe chimodzi ndi chifukwa Mulngu anangosankha kusokoneza chilankhulo chao.

Ndipo Yehova anati, Taonani, anthu ali amodzi, ndipo onse ali naco cinenedwe cao cimodzi; ndipo ici ayamba kucita: ndipo tsopano palibe kanthu kakuletsedwa nao kamene akafuna kucita. Tiyeni, titsike, pomwepo tisokoneze cinenedwe cao, kuti wina asamvere cinenedwe ca mnzace. (Genesis 11:6-7)

Ichi chinali chiyambi cha kugawanika kwa zinenelo za dziko lapansi ndipo chifukwa chakuti anthu samvana zokamba zao, dongosolo lonse lomangamanga linathera panjira.

Ndipo Yehova anabalalitsa iwo pa dziko lonse lapansi, ndipo analeka kumanga mudzi. (Genesis 11:8)

Anthu amene amamvana chinenele anayamba kubwela pamodzi. Kotero kuti mitundu ya anthu olakhula chinenele chimodzi inayamba. Pamene mitundu ya anthu imeyi imakula, anthu anayamba kufalikira madera osiyanasiyana adziko lapansi. Chifukwa cha ichi, anthu ayakhalanso osiyana osati chifukwa cha chinenele chakha komanso ma dera amene anthuwa amakhala. Anthu amakhala olekanitsidwa ndi mapili akuluakulu komanso Nyanja zazikulu.

Mukupita kwa nthawi, chifukwa chakulekana kwa mitundu ya anthu, zikhalidwe ndi kachitidwe ka zinthu mosiyana zinayamba kuoneka. Komanso zipembedzo ndi kupembedza milungu yosiyansiya zinayamba kuonekera.

Patadutsa nthawi yayiyali, magulu a anthu akula ndipo izi zinapangitsa kuti mayiko ayambe kubadwa. Ndipo mayikowa anayamba kukhazikitsa malire, malamulo oyendetsera dziko, boma komanso anthu. Umu ndi mmene dziko lapansi linagawanikira nakhala ndi zilakhulo komanso zinenelo zosiyansiya.

MMENE DZIKO LILI LERO LINO

Lero lino dziko ndi logawikana malingana ndi nthaka imene imalekanitsidwa ndi madzi. Ena mwa magulu amayiko ndi Africa, America komanso Australia kungotchulapo ochepa. Ndipo dziko lililonse limene limapezeka mu magulu amayiko lili ndi malamulo ake osiyana ndi mayiko ena.

Angakhale mudziko limene mukhalanso zigawo zosiyanasiyana. Mwachitsanzo, madera osiyansiysana amakhara ndi mitundu komanso zikhalidwe zosiyansiya. Koma anthu ambiri opezeka mayiko osiyansiya sanamvebe Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Samadziwa za Mulungu mmodzi weniweni komanso ena alibe mau a Mulungu olembedwa muchinenelo chawo.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yoloweza yotsogolera

2. Fotokozani mmene dziko lapansi linagawanikila kukhala ndi anthu azinenelo zosiyanasiyana.

3. Fotokozani mmene kusiyana zinenelo kunabweletsera mitundu ya anthu.

4. Kodi kubwela kwa mitundu ya anthu kunapangitsa bwanji kuti mayiko ayambe?

ZOPHUNZIRA ZOONJEZERA

Mulungu analenga dziko lapansi

|

Anthu onse amakhala mu gawo awiri

Dziko lakuthupi ndi dziko lauzimu

|

Dziko lakuthupi → munthu ← dziko lauzimu

Dziko lakuthupi ndi lauzimu zimayendelana kapena zochitika mbali imodzi zimakhudza mabali inayi

|

Dziko lakuthupi limagawidwa malingana ndi chilakhulo, chikhalidwe komanso malire a panthaka

|

Dziko lauzimu limagawidwa mu ma gawo awiri a anthu

Okhulupilira Yesu komanso amene sakhulupilira iye

|

Dziko lauzimu

|

Okana Khristu

|

ake a Khristu

CHAPUTALA 3

KUONA ZINTHU (DZIKO) MMENE MULUNGU AMAONERA

ZOLINGA

Pamapeto pa maphunziro awa, muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- kulemba Vesi yapamtima Yotsogolera
- Kupeza chifungulo cholowa paliponse mu Baiburo
- Kufotokoza mfundo ziwiri za chifungulo cholowa paliponse mu Baibulo
- Pezani ma vesi awiri ofotokoza cholinga cha Mulungu ndi dziko lapansi.
- Gwilitsani ntchito zitsanzo zakuthupi pofuna kuonetsera mmene Mulungu amalionera. Dziko lapansi.

VESI YOTSOGOLERA

Ndipo anawatsegulira mitima yao, kuti adziwitse malembo; ndipo anati kwa iwo, 8 Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacityatu; ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luka 24:45-47)

MAU OYAMBA

Mu phunziro lapitalo, taona kuti okhulupirira ayenera kuona zinthu ngati mmene Mulungu amazionera. Koma masomphenya amenewa akhoza kukwanilitsidwa pokhapokha mutadziwa zimene mau a Mulungu amaphunzitsa. Koma chaputala ichi chifotokozeraz za chinsisi chothandiza kuti mumvetse kaonedwe ka zinthu ngati mmene Mulungu amazionera, cholinga cha Mulungu ndi dziko lapansi komanso mu ndime imeneyi, tiona zitsanzo za kuthupi zoonetsera mmene Mulungu amaonera dziko lapansi. Phunziro ili limapitilirabe mu chaputala cha 4 ndi 5 mmene tidzaone mmene mau a Mulungu amafotokozeraz zokhudza dziko lapansi.

CHIFUNGULO CHOLOWA PALIPONSE

Mu Baibulo muli ma buku okwana 66 ndipo buku lililonse lili ndi vesi yotsogolera. Vesi imeneyi imagwira ntchito ngati mmene chifunguro chigwilira ntchito kudziko lakuthupi. Chifungulo chakuthupi chitsekula chitseko chomwechonso, vesi yotsogolera kuti timvetsetse mitu ikuluikulu mu Baibulo.

Baibulo nalo lili ndi chifunguro cholowa paliponse, chifungulochi imakhara vesi imene imathandiza kuti timvetse bwino lomwe mau onse a Mulungu. Ndipo chifungulo chimenechi ndi ichi:

Ndipo anawatsegulira mitima yao, kuti adziwitse malembo; ndipo anati kwa iwo, 8 Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lachitatu; ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi kukhulukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luke 24:45-47)

Mau akuti anatekula maso awo kuti akamvetsetse mau a Mulungu akutanthauza kuti Yesu khristu anapereka chifungulo cholowa paliponse chowathandiza kuti akamvetse mau a Mulungu. Ndipo Yesu akupeleka mfundo ziwili zothandiza kuti amvetse mau a Mulungu kotere kuti ngati munthu sangamvetse mfundo zimenezi, ndiye kuti sangamvetsenso mau a Mulungu.

MFUNDO YOYAMBA, Kotere kwalembedwa kuti Khristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lachitatu”

Mau akuti kodi kwalembedwa akutanthauza kuti Khristu amayenera amve zowawa ndi cholinga choti munthu ochimwa uja ayanjanitsidwe ndi Mulungu. Ichi ndi mfundo yayikulu mu Baiburo lonse

Mulungu ananena kuti mphoto ya uchimo ndi imfa yakhupi keneko yamuyaya.

Koma mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa, usadye umenewo; cifukwa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu. (Genesis 2:17)

Pakuti mphotoho yace ya ucimo ndi imfa; koma mphotoho yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu. (Aroma 6:23)

Yesu Khristu anachoka kumwamba nasandulika kuthupi kuti akafere munthu wochimwayo:

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. (Yohane 3:16)

Mulungu akaliona dziko lapansi, Iye amaona munthu ochimwa amene akufunika mpulumutsi:

Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu; (Aroma 3:23)

Kudzera mukulapa machimo mwa Khristu Yesu, munthu anayanjanitsidwa ndi Mulungu ndipo analandira mphoto ya Moyo osatha.

MFUNDO YACHIWIRI: kulapa ndi chikhululukiro cha machimo zilalikidwe”

Chifungulo chachiwiri kuti tikamvetse malemba ndiko kulalikira za kulapa komanso chikhulukiro cha machimo kwa anthu onse adziko lapansi. Izi zikutathauza kuti anthu onse okhulupirira ali ndi udindo ofunika kwambiri pa mfundo imeneyi.

Ndikanena kwa woipa, Udzafa ndithu, koma iwe osamcengeza, wosanena kumcengeza woipayo aleke njira yace yoipa, kumsunga ndi moyo, woipa yemweyo adzafa mu mphulupulu yace; koma mwazi wace ndidzaufuna pa dzanja lako. (Ezekieli 3:18)

Angakhale kuti Yesu anafera anthu onse, izi sizitanthauza kuti anthu onse anapulumutsidwa kutchimo. Munthu wina aliyense payekha ayenera kupanga chisankho cholapa kapena ayi. Koma kuti munthu alandire chikhuluko, pakuyenera kukhala chidziwitso kuti Yesu ndi ndani kapena munthu ayenera kudziwa za Yesu Khristu.

Pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka. Ndipo iwo adzaitana bwanji pa iye amene sanamkhulupirira? Ndipo adzakhulupirira bwanji iye amene sanamva za iye? ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? (Aroma 10:13-14 Romans 10:13-14)

Pamene tilalika za kulapa komanso kukhululukidwa kwa machimo ndiye kuti tikufalitsa Uthenga wabwino. Nkhani yofalitsa uthenga wabwino unali mutu umene Yesu Khristu amakonda

kukambirana ndi ophunzira ake atauka kwa kufa. Mukhoza kuona izi mmabuku awa (Yohane 20:21, 21:15-17; Mateyu 28:18-20, Marko 16:15; Luka 24:44-48) Nthawi zambiri ukakhara kuti ukukambirana ndi munthu komaliza, pamakhala kutsindika mfundo zofunika chimodzimodzinso Yesu Khristu anatsindika zakulalika uthenga wabwino kwa ophunzira ake*.

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

MMENE MULUNGU AMAONERA DZIKO LAPANSI

Timaphunzira mmene Mulungu amalionera dziko lapansi kuchokera ku chifungulo cha Baibulo. Mulungu samaona dziko lapansi malingana ndi ndale, chikhalidwe kapena ma boma a dziko lapansi. Iye amaona anthu ochimwa amene ayenera kuyanjanitsidwa ndi Mulungu kudzera mwa Khristu Yesu kotero kuti Iye amaona dziko lapansi limene liyenera kulandira uthenga wachipulumutso.

Mulungu amaona dziko lapansi malingana ndi dongosolo limene anakhazikitsa pachiyambi pomwe

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. Aefeso 1:9-10)

Monga mwa citsimikizo mtima ca nthawi za nthawi, cimene anacita mwa Kristu Yesu Ambuye wathu: (Aefeso 3:11)

Harvestime International Institute imapeleka phunziro lina lotchedwa "*maziko achikhulupiliro*," limene limafotokoza mwa dongosole nkhani ya kulapa ndi kukhulukidwa kwa machimo

Cholinga cha Mulungu kuchokera pachiyambi pomwe ndiko kusonkhanitsa anthu onse ochimwa pamodzi kudzera mwa Khristu Yesu. Koma kudzera mu mau a Mulungu koma ichi pachiyambi chinali chinsisi chobisika kwa dzaka zochulukira.

Zitsanzo zakuthupi za mmene Mulungu amaonera dziko lapansi

Baibulo limagwiritsa ntchito zitsanzo zakuthupi pofuna kufotokoza mfundo zauzimu. Chinthu chakuthupi ndi chimene tikhoza kuchiona ndi maso anthu. Zinthu zimenezi tikhoza kuzimva kapena kuzionika. Pamene zinthu zauzimu ndi zimene sitingazione ndi maso anthu. Choncho pofuna kuphunzitsa zinthu zimene sitingamvetse ku thupi lauzimu, Mulungu amagwiritsa ntchito zitsanzo zakuthupi pofuna kuonetsera mmene Mulungu amaonera dziko lapansi kapena mmene amaonera zinthu. Mwachitsanzo, Yesu khristu anagwilitsa nthchito chitsanzo cha kuthupi pofuma kuonetsa mmene Mulungu amaonera dziko lapansi. Yesu Khristu anati kwa ophunzira ake:

Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta. (Yohane 4:35)

Yesu khristu sikuti apa amafotokoza za kholora la munda wakuthupi. Ndipo Yesu Khristu amakamba za choonadi chazimu pofuna kuonetsera masomphenya auzimu a dziko lapansi Nthawi ina Yesu khristu anafotokozera ophunzira ake kuti:

Ndipo munda ndiwo dziko lapansi; Mateyu 13:38)

Kuyambira ku Africa, kumpoto kwa America, kumwera kwa America, ku Ulaya ndi Zilumba zonse za dziko lapansi, Mulungu amaona madera onsewa ngati ngati munda wakholora lauzimu chifukwa cha ichi, Mulungu amaona za chosowa chachikulu mumayiko atchulidwawa chimene chili:

. . . Pomwepo ananena kwa ophunzira ace, Zotuta zicurukadi koma anchito (Mateyu 9:37) ali owerengeka.

Mulungu amaona kholola lambirio loti likololedwe koma bvuto ndi lakuti ogwira ntchito achepa.

‡

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lemabani Vesi yapamtima yotsogolera

2. Kodi ndi Vesi iti mu Baibulo ndi chifungulo cha Baibulo lonse?

3. Fotokozani mfundo ziwiri zopezeka mu vesi ya chifunguro cha Baibulo

4. Pelekani vesi imene imaonetsera cholinga cha Mulungu ndi dziko lapansi.

5. Kodi cholinga cha Mulungu mu vesi imeneyi ndi chiani?

6. Kodi ndi chitsanzo chiti chakuthupi chopeza mu Baibulo chimene chimafotokoza mmene Mulungu amaonera dziko lapansi?

‡ Muphunzira zambiri zokhudza za chosowa cha ogwira ntchito ambiri pamene mupitiriza ndi maphunziro awa.

ZOONJEZER POPHUNZIRA

Muphunziro ili mwaphunzira mmene Yesu Khristu amagwiritsira ntchito zitsanzo zakuthupi pofuna kuonetsera choonadi chazimu. Pitolirizanani kuphunzira poonetsera chimene ndime zili munsimu zikuphunzitsa pa nkhani ya kholora.

Mateyu 13:3-39

Marko 4:3-32

Luka8:5-15

Luka 10:2

Yohane4:35

Yohane 12:24

I Akorinto 3:6-8

II Akorinto 9:6

Agalatiya 6:7-8

CHAPUTALA 4

MAONEDWE A DZIKO LAPANSI MU CHIPANGANO CHAKALE

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziro ili, muyenera kukwanitsa zinthu:

- Kulemba vesi yotsogolera ya pamtima.
- kupeza pa mtima pa mau a Mulungu mu Baibulo
- Kufotokoza mwachidule mmene mabuku a chilamulo mu Chipangano Chakale amanonezera zinthu.
- Kufotokoza mwachidule mmene mabuku a mbiri muchipangano chakale amaonera zinthu.
- Fotokozani mwachidule mmene ma buku a ndakatulo muchipangano chakale amaonera zinthu.
- Fotokozani mwachidule mmene ma buku a ndakatulo amaonera zinthu mu chipangano chakale.

VESI YOTSOGOLERA

Pakuti kuyambira koturukira dzuwa kufikira kolowera kwace dzina langa lidzakhala lalikuru mwa amitundu; ndipo m'malo monse adzaperekera dzina langa cofukiza ndi copereka coona; pakuti dzina langa lidzakhala lalikuru mwa amitundu, ati Yehova wa makamu. (Malaki 1:11)

MAU OYAMBA

Chaputala ichi komanso chaputala 5 chipitiriza kuona Maonedwe a Zinthu Malingana ndi Mau a Mulungu pogwiritsa ntchito ma vesi angapo mu Baiburo. Mbuyomu, taona kale mmene Mulungu analengera dziko lapansi, kugwa kwa munthu komanso mmene dziko lapansi linagawanikirana kukhala ndi mayiko ndi zinenelo zosiyanasiyana. Koma mu chaputala ichi, muphunzira zimenezi

malingana ndi zimene Chipangano Chakale chimafotokoza zokhudza dziko lapansi. Kenako, chaputala cha patsogolo chidzafotokoza za nkhani yomweyi malingana ndi Chipangano chakale.

Anthu ambiri samazindikira za chikonzero cha Mulungu chirichikhalire. Izi zikugwirizana ndi mau akuti anthu anga akuonengeka chifukwa chakusadziwa (Hoseya 4:6). Mundime imeneyi sikuti Mulungu amakamba za chidziwitso chimene anthu amachipeza akaphunzira ku sukulu. Mulungu akukamba za chidziwitso chauzimu chimene chimathandiza ife kuti timvetse malingaliro a Mulungu pa dziko lapansi komanso ndikutengapo mbali mu ndosolo limeneli pano padziko lapansi.

BUKU LOKHALA NDI UTHENGA UMODZI

Baibulo si buku limene limafotokoza nzeru za anthu zokhudza Mulungu koma ndi uthenga ochokera kwa Mulungu. Ndipo cholinga cha uthengawu ndi kuti munthu akazindikire cholinga cha Mulungu pa munthu. Baibulo limafotokoza nkhani za anhtu a Mulungu anasankhidwa ndi Mulungu kuti akabvumbulutse mau ake kudziko lapansi.

Mu Baibulo mumapezeka malonjezano, ma uneneri, komanso mau otonthoza angakhaleenso olimbikitsa. Koma ngakhale izi zili chomwechi, uthenga wa Baibulo kuchokera pa chiyambi mpaka kumapeto ndi umodzi. Uthenga umene ndi wa kukhudzika kwa Mulungu ndi cholinga chofuna kupulumutsa munthu ochimwa.

Cholinga cha Mulungu kuchokera pachiyambi ndi.....

Kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:10)

Dongosolo kapena lofuna kupulumutsa munthu kudzera mwa khristu Yesu zinali mu dongosolo la Mulungu kuchokera pachiyambi pomwe.

CHIPANGANO CHAKALE

Chipangano chakale chili ndi mabuku okwana 39 ndip mabukuwa anagawidwa mu zigawo **zinayi zimene ndi izi:**

Chilamulo

Kuyambira Genesis mpaka Deteronome

Mbiri

kuyambira Yoswa mpaka Estere

Ndakatulo

Kuyambira Yobuu mpaka Nyimbo Ya Solomo

Uneneri Kuyambira

Yesaya mpakana Malaki

Munsimu muli kufootokoza mwachidule zimene ma gawo a Chipangano Chakale chimaphunzitsa zokhudza dongosolo la Mulungu pa dziko lapansi.

MABUKU A CHILAMULO

Kuyambira Genesis Mpaka Deteronome

Mabuku a Genesis mpaka Deteronome amatchedwa ma Buku a chilamulo chifukwa amafotokoza za malamulo oyambilira amene Mulungu anapereka kwa munthu komanso mnene anthu anachitira ndi malamulo amenewa.

CHIYAMBI

Mau akuti Genesis amatanthauza kuti chiyambi. Buku loyamba mu Baibulo limafotokoza za chiyambi cha dziko lapansi, munthu, tchimo komansi malingaliro a Mulungu pofuna kupulumutsa munthu ochimwa. Tinaphunzira kale kuti munthu analengedwa mu chifanizo cha Mulungu. Izi zikutanthauza kuti munthu ali ngati Mulungu m' ma gawo ena monga Mulungu ndi mzimu chomwechonso munthu ali ndi mzimu. Kugwa kwa munthu chifukwa cha tchimo kunapangitsa kuti munthu kufanana kwake ndi Mulungu kuchepe. Dongosolo la Mulungu loyamba lokhudza dziko lapansi likuperekedwa pa Genesis 3:15:

**Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace
(Genesis 3:15)**

Lonjezano linaperekedwa mobisika. Mbeu yanamwali ikuyimilira Yesu amene adzalalira mutu wa njoka imene ikuyimira satana amene anachimwitsa munthu. Ndipo Yesu Khristu adzapanga zimenezi pafera pa mtantand ndi cholinga choyajanitsa munthu ndi Mulungu.

Pali zinthu zisanu ndi chimodzi zimene vesi ikubvumbulutsa:

1. Mulungu ndi gwero la chipulumutso

2. Satana ndiye mdaniyo (udani pakati pa mbeu yamkazi ndi njoka)
3. Mpulumutsiyo ndi munthu ndithu chifukwa adzakhara ochokera ku (mbeu yamkazi)
4. Mpulumutsiyo adzazuzidwa (adzalalira chitende chake)
5. Mulungu adzagongetsa mdaniyu (adzalalira mutu wako)
6. Chipulumutso chidzakhala cha anthu onse (mbeu zonse) zamibado yonse

Nkhani yakufalikira kwa uchimo padzio lonse lapansi (Genesis 6) yakambidwa kale. Koma Mulungu anatumiza chigumura cha madzi ataona kuti kuipa kwa munthu kwakura. Komabe Mulungu anapelekabe dongosolo la chipulumutso cha munthu pa (Genesis 8-9)

Chombo chimene Nowa ndi banja lake anapulumukira chimayimilira chipulumutso chimene chidzabwere ndi Yesu Khristu. Yesu Khristu ndiye Chombo chauzimu chimene anthu onse akhoza kuthawiramo kuchokera kuchionengeko cha uchimo. Ngakhale kuti nkhani ya Nowa imaonetsa kuti dziko lapansi ndi lochimwa kotere kuti liyenera kuonongwedwa, Mulungu yemweyu amaona dziko lapansi ndi chifundo choncho wapereka dongosolo lothawira chilango cha tchimo.

Chifundo ndi chiweruzo cha Mulungu chimaonekera kwambiri mu chipangano. Munthu akachimwa, Mulungu amatumiza chiweruzo koma chifukwa chifundo chake, amaperekanso populumukiranso.

FUKO LOSANKHIKA/ LAPADERA

Mbuyomu taona mmene kuukila Mulungu pa nsanja ya Babulo kunabweletsera zinero zosiyanasiyana kenako izi zinabadwitsa mitundu ya anthu osiyanasiyana komanso mayiko. Kuchokera ku mafuko amene anadza chifukwa cha nsanja ya Babulo, Mulungu anasankha fuko la Israyeli ndi cholinga.

Fuko lonseli linachokera kwa munthu mmodzi amene ndi Abrahamu. Mukhoza kuwerenga nkhani ya Abrahamu makamaka malonjezano a Mulungu kwa iye ndi kukwaniritsidwa kwake pa Genesis 11:27-25:24. Mulungu anasakha Abrahamu kuti akakhare tate wa fuko la Israyeli komanso Mulungu anasankha Iye ndi cholinga cha paderadera.

ndipo ndidzakuyesa iwe mtundu waukuru, ndipo ndidzakudalitsa iwe, ndi kubukitsa dzina lako; nukhale iwe mdalitso; ndipo ndidzadalitsa amene akudalitsa iwe; ndi kutemberera iye amene akutemberera iwe; ndipo mwa iwe adzadalitsidwa mabanja onse a dziko lapansi, (Genesis 12:2-3)

Genesis 22:18 m'mbeu zako mitundu yonse ya dziko lapansi idzadalitsidwa: cifukwa wamvera mau anga.) (Werenganiso Genesis 26:4 and 28:14)

Kudzera mwa Abrahamu, Mulungu anadzutsa mtundu wa Israyeli. kudzera mwa Israyeli anthu onse adziko lapansi adzadalitsidwa pakumudziwa Mulungu weneweni. Ndipo mdalitso umenewu udzakhudza mtundu uli onse wa anthu.

Mulungu sanasankhe Israyeli chifukwa cha kupambana kwake kuyelekeza anthu amitundu ina. Koma Mulungu anasankha Israyeli ndi cholinga chapaderadera. Mulungu anasankha mtundu waung'on wa anthu ndi cholinga choti ukatumikire mitundu ya mbiri ya anthu. Komanso Mulungu anasankha Israyeli ngati njira imodzi yofuna kudzibvumbulutsa yekha kwa anthu ake makamaka kudzera mwa mwana wake Yesu Khristu amene anali ochokera ku fuko la Israyeli. (Mateyu 2:2; John 4:22). Israyeli ndi fuko limene Mulungu analakhura mau ake olembedwa kwa anthu onse a dziko lapansi. (Salimo 147:19; Aroma 3:1,2; 9:4).

Amitundu onse asonkhane pamodzi, ndi anthu aunjikane; ndani mwa iwo anganene ici ndi kuonetsa ife zinthu zakale? Atenge mboni zao, kuti abvomerezeke ndi olungama; Pena amve, nanene zoonadi. Inu ndinu mboni zanga, ati Yehova, ndi mtumiki wanga, amene ndakusankha; kuti mundidziwe, ndi kundikhulupirira Ine, ndi kuzindikira, kuti Ine ndine; ndisanakhale Ine, panalibe Mulungu wolengedwa, ngakhale pambuyo panga sipadzakhala wina. Ine, Inetu ndine Yehova; ndipo palibe Mpulumutsi, koma Ine ndekha. Ine ndalalikira, ndipo ndikupulumutsa ndi kumvetsa, ndipo panalibe Mulungu wacilendo pakati pa inu; cifukwa cace inu ndinu mboni zanga, ati Yehova, ndipo Ine ndine Mulungu. (Yesaya 43:9-12)

Mulungu anakhazikitsa ubale ndi Israyeli kudzera mu pangano. Pangano limeneli ndi ngwirizano osonyeza kuti iwo ndi anthu a Mulungu komanso Iye ndi Mulungu wao.

**Koteronso cikho, citatha cakudya, ndi kuti, Cikho ici ndi pangano latsopano
m'mwazi wanga; citani ici, nthawi zonse mukamwa, cikhale cikumbukilo canga
(I 1 Akorinto 11:25)**

OLOWA M'NYUMBA A ABRAHAMU

Malingana ndi Chipangano chatsopano, ife ndife mbumba ya Abrahamu kapena kuti olowa m'nyumba. Olowa nyumba ndi munthu amene amatenga chuma cha munthu amene wamwalira. Chimodzimodzi ndi Abrahamu, ife taitanidwa kuti tikakhale mdalitso ku dziko lapansi. Koma maiko kapena kuti mafuko a dziko lapansi adzadalitsidwa pokhapokha ngati tingawagawire Uthenga Wabwino. Pamene Mulungu anaitana Abrahamu, Anamuza Iye kuti achoke ku dziko la makolo ake ndi kupita ku dziko limene Mulungu adzamuonetsera. (Machitidwe 11:31). Ndipo Abrahamu anatenga banja lake lonse ndi kupita kukhala ku Harani (Genesis 11:31)

Pamene Abrahamu amayitanidwa, Mulungu anauza Abrahama kuti ochoke dziko lake la Ur ndikupita ku dziko limene Mulungu adzamulozera. Ndipo Abrahamu anamvera zimenezi nakakhazikiza atafika ku Harani (Genesis 11:31)

Mulungu akuyitana munthu okhulupirira wina aliyense m'dziko lina lilironse lauzimu limene limalepheretsa kukwanilitsa cholinga cha Mulungu. Nthawi zina okhulupirira akhoza kuyitanidwa ndi Mulugu kuti asiye dziko lao ndi kukatumikira anthu a mayiko ena. Tikhoza kufotokoza kuti okhulupirira wina aliyense ali ndi malo otchedwa “Harani” amane pomvera Mulungu amayera kusamukilako. Koma ukafika malo amenewa sipamakhara kubweleranso mbuyo ngati mmene anachitira Abrahamu.

CHIYAMBI CHA ISRAYELI

Ili munsimu ndi Mbiri ya Abrahamu mu buku la Genesis, ndipo mbiri ndi kukula kwa fuko la Israyeli kukupezeza mu mabuku ena achilamulo

Mulungu anagwiritsa ntchito Israyeli pofuna kubvumbulutsa chikonzero chake ndi dziko lapansi.

Genesis 50:20: Ali ku Ayiguputu, Mulungu anasankha Yosefe ndi cholinga fuko la Israyeli likapitirire.

Ekisodo 8:22: Mulungu anatulutsa Israyeli kuchoka ku Ayiguputo ndi cholinga chofuna kuonetsera kuti ndi Mulungu wa dziko lonse lapansi.

Ekisodo: 9:29: Miliri imene Mulungu anatumiza kwa anthu aku Ayiguputo inali yofuna kuonetsera mphamvu Yake.

Ekisodo 33:16: Kupezeka kwa Mulungu pakati pa Israyeli kunali kufuna kuonetsa kuti iye alipodi kwa anthu adziko lapansi.

Ekisodo 34:10 Mulungu anapitilirabe kugwira ntchito pakati pa ana a Israyeli pofuna kuti onse akaone ntchito ya Mulungu.

Levitiko 20: 23: Israyeli amayenera kukhara chitsanzo cha bwin kwa anthu ena amitundu ina osati kutsata ntchito zao zoyipa.

Levitiko 19:24: Israyeli amayera kuonetsera chikondi cha Mulungu kwa anthu amitundu ina.

Numeri 14:21 Choling cha Mulungu chinali chakuti dziko lapansi lonse lionetsere ulemelero wake.

Mulungu anasankha Israyeli kuti akakhale mboni yake, koma chifukwa chakuchimwa, Mulungu anabalalitsa iwo ndikuwapereka m' manja mwa adani awo.

Deuteronomo 18:9; 30:19: Mulungu anachenjeza Israyeli kuti asatsate njira za anthu amitundu ina koma kuti akasankhe njira yapatsa Moyo.

Deuteronomo 28:9-10: Chokhumba cha Mulungu chinali kuti anthu onse adziko lapansi akazindikie mphamvu ya Mulungu kudzera mwa Israyeli.

Kwa anthu ena apadziko lapansi, mtundu wa Isreyeli sumaonedwa ngati ofunika kwambiri, koma izi ndi zosiyana ndi m'mene Baibulo limaonera zinthu. Ma buku a Mbiri mu Chipangano Chakale. Amafotokoza zinthu zimene Israyeli amakumana nazo pa udindo umene anapatsidwa ndi Mulungu.

Pamene Israyeli amvera, Mulungu amachitapo kanthu ndikuwalanditsa mmanja mwa adani awo. Ndipo izi zimachira umboni za mphamvu ya Mulungu. (Werengani Masalimo 66:1-7; Yesaya 52:10). Pamene Israyeli wachimwa, chiweruzo chimene Mulungu amapereka chinali chizindikiro

kuti iye alipo (Salimo 145:17). Kaya ndi chikondi kapena chiweruzo kwa Israyeli kuchokera kwa Mulungu, Mulungu mwini amapitiriza kudzionetserabe kwa anthu onse adziko lonse lapansi.

Zina mwa ndime zochokera ku ma buku a mbiri amene akhoza kukuthandizan kumvetsa chikonzero cha Mulungu ndi dziko lapansi ndi awa:

Yoswa 2:11; 3:11: Mulungu ndi Mbuye wa dziko lonse lapansi.

Yoswa 4:23-24: Mulungu anaumitsa mtsinje wa Yolodani kuti nathu onse a dziko lapansi akazindikire mphamvu yake.

Yoswa 23:3, 9, 12, 13: Mulungu anachenjeza Israyeli kuti akapatuke kwa anthu osakhulupirira ndikukatamikira ngati mboni pakati pa anthu amenewa.

Mulungu anayesa Israyeli kuti aone ngati atsate malamuro Ake ndipo buku la Oweruza limanetsera kulempera kwa Israyeli mobwerelezabwereleza.

Rute 1:16: Mulungu wa Ayuda anakhala Mulungu wa anthu Amitundu.

I Samuyeli 17:46: Pamene Davite anakumana ndi Goliata, analumbira chigonjeztso kuti anthu onse akadziwe kuti kuli Mulungu wa Israyeli.

II Sameuli 22:50-51: Davide anatamanda Mulungu ndi cholinga choti anthu a dziko lonse atamande Mulungu.

I Mafumu 8:23, 43: Pamene Ufumu wa Israeli unakhazikitsidwa, Mfumu Solomo inapempha kuti anthu onse a dziko lapansi adzina la Yehova.

I Mafumu 8:43, 53, 60: Ma vesi awa akuonetsera cholinga cha Mulungu kuti dziko lonse lapansi lonse lidziwe Yehova.

II Mafumu 19:15-19: Cholinga cha chipulumutso ndi chakuti dziko lapansi lonse lidziwe Mulungu

I Mbiri 16:23-24, 31: Ulemelero wa Mulungu kumayenera kulengezedwa dziko lonse lapansi

I Mbiri 16:35: Kulanditsidwa kwa anthu achikunja kumabweretsa ulemelero wa Mulungu.

II Mbiri 6:32-33: Adziko lapansi ayenera kukhala ndi mwai ozindikira Mulungu.

II Mbiri 6:14; 20:6; Mulungu amalemekezedwa ngati Mulungu mmodzi owona yekhayo.

II Mbiri 16:9: Mulungu amaona dziko lapansi ndi cholinga chapaderadera mkati mwake.

Ezara 1:2; 5:11: Koresi amayenera kumanga kachisi ku Yerusalemu kuti akalemekeze Mulungu pamaso pa antu onse a dziko lapansi

Nehemiya 6:16: Cholinga chenicheni cha Nehemiya sichinali kungomanga malinga amphamvu chabe, koma chinali kufuna kuonetsa mphamvu Ya Mulungu komanso kuti zolinga za Mulungu zimakhara za kale lomwe.

Nehemiya 9:6-7: Mulungu akulengezedwa ngati Mbuye wa dziko lonse lapansi.

Estere 4:14: Estere anakuzidwa ndi cholinga chapadera choti akapulmutse Israyeli ku chionongeko chimene Satana anakonza.

MA BUKU A CHILAMULO

Kuyambira buku la Yobu mpaka la Nyombo ya Solomo

Ma buku a Yobu, Masalimo, Miyambo, Mlaliki ndi Nyimbo ya Solomo amatchedwa ma buku a ndakaturu chifukwa chakuti analembedwa mwa ndakaturu. Mutu waukulu umene mabuku amenewa amakamba ndi dziko lapansi.

Mu buku la Masalimo, mau oti mafuko kapena maiko onse a dziko lapansi amatchulidwa kokwana ka 200. Ndipo pali mau osiyanasiyana monga, “dziko lapansi lonse”, “anthu onse” “thupi lonse”, “chirichonse chopuma”, “maso a onse” ndi amitundu onse amatchulidwa kawirikawiri.

Buku la Salimo limaonetsera dziko lapansi ngati la Mulungu ndipo kuti chilichonse chili pansu pa ulamuliro wake (Salimo 24:1). Mulungu akulemekezedwa ngati wamkulu pa onse (Salimo 38:10, 97:9). Mulungu akuonetseredwa ngati oweruza wadziko lapansi (149:7), ngakhale Mulungu yemweyo akupereka Chipulumutso mwachifundo chake (119:64). Uchimo wamaiko kapena wamafuko onse ukufotokozeredwa pa Salimo 2. Malingana ndi chaputala 67, chiyembekezo cha chipulumutso chikuperekedwa kwa mafuko onse.

Gawo la zoonjezera likupereka zambiri zokhudza dziko lapansi mu buku la Salimo.

Ma vesi ena otsogolera kuchokera ku mabuku ena a ndakatulo:

Yobu 1 ndi 2. Fotokozani nkondo imene ikuyenda mumtima, mmaganizo, ndi mmoyo wa munthu.

Yobu 9:24; 12:23; 38:1-41: Ngakhale kuti dziko lapansi pakadali pano ndi lauchimo, koma Mulungu akulamulirabe dziko lapansi.

Miyambo 2:22; 10:30; 11:31: Akufotokoza kuipa kwa dziko lapansi pakadali pano

Miyambo 14:34: Maiko agwirowo ndi ochimwa akusiyansidwa.

Miyambi 3:19; 8:23-31: Imalemekeza Mulungu ngati olenga dziko lapansi ndi lakumwamba.

Mlaliki 1:4; 3:11: Imaonetsera Mbuye ngati olenga dziko lapansi ndi lakumwamba.

Mlaliki 7:20; 8:14; 10:7: Amaonetsera nyengo ya munthu wa dziko lapansi akutsamo.

Mlaliki 12:7: Amaonetsera moyo wamuyaya wa mzimu wa munthu.

Mlaliki 3:14: Amatsindikika zakukhazikika kwa chikonzero cha Mulungu.

Ma vesi alembedwawa akuonetsera chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi malingana ndi mmene zakambiridwa mma buku amenewa. Werengani gawo la zoonjezera pophunzira kuti muone zina zimene mabuku a ndakatulo akukamba zokhudza dziko lapansi.

MA BUKU A UNENERI

Kuyambira buku la Yesaya kufikira buku la Malaki, Mabuku onsewa amatchedwa ma buku a uneneri. Ma bukuwa analemba za mauneneri amene aperekedwa ndi Mulungu kudzera mwa anthu odzodzedwa a Israeli. Ma buku amanewa akufotokoza zinthu zamtsogolo malingana ndi chikonzero cha Mulungu. Kudzera mu mabuku amenewa, ntchito ya mpulumutsi ya dziko lonse lapansi ikutsindikizidwa. Mabuku amenewa sakungoonetsera Yesu ngati Mpulumutsi wa Israeli yekha, koma ngati mpulumutsi wa anthu onse.

Utumiki wa maiko osiyanasiyana

Awiri mwa aneneri amenewa ndi Danieli ndi Yesaya anatumikira maiko ena.

Danieli anachitira umboni za Mulungu pamene amatumikira ku nyumba ya chifumu ku Babulo. Mulungu anapulumsa Danieli ku imfa pofuna kumuonetsera iye kuti ngati Mulungu wadziko lapansi (Danieli 6:27). Buku la Danieli liri ndi mavumbulutso ambiri amene amaonetsera tsogolo la dziko lapansi. Buku limeneli limagwirizana ndi Buku la Chivumbulutso mu Chipangano chatsopano limene limapereka zinthu zina zoonjezera zokhudza chikinzero cha Mulungu ndi maiko a dziko lapansi.

Zolinga za chikonzero cha Mulungu zafotokozeredwa mwachidule pa ndime iyi:

Ndipo anampatsa ulamuliro, ndi ulemerero, ndi ufumu, kuti anthu onse, ndi mitundu yonse ya anthu, ndi a manenedwe onse, amtumikire; ulamuliro Wace ndi ulamuliro wosatha wosapitirira, ndi ufumu wace sudzaonongeka. (Danieli 7:14)

Yona anali mtumwi wachiyuda amene anatumidwa kuti akalalike za chipulumutso kwa amitundu oipa aku Nenevi. Iye anakwaniritsa cholinga cha utumiki wake ngakhale amkazengereza. Buku la Yona ndi lofunika chifukwa chakuti limaonetsera cholinga cha Mulungu chofuna kubweretsa chipulumutso kwa anthu amafuko onse, osati fuko la Israeli lonse.

Anthu aku Israeli anali ndi udani waukulu ndi Nenevi. Chifukwa cha ichi, pachiyambi Yona anakana kukalalikira uthenga Wabwino. Koma atakumana ndi Mulungu, Iye anapita ndi kukalalikira za Uthenga wakulapa. Ngakhale kuti Iye sanapereke chitsogozo cha mmene amayenera kuchitira, koma anadziwa okha chimene amayenera kuchita ndipo izi zikuonekera mu zimene amfumu analamula kuti zichitike. (Yona 3: 8-9)

Mmalo moti Yona akondwere ndi kutembenuka mtima kwa anthu amenewa, iye anadandaura ndi kuyamba kufusa mafuso Mulungu (Yona 4:9). Mau omaliriza amene Yona analemba m'bukuli ndi akuti: ndikuyenera kupsa mtima kufikira imfa" (Yona 4:9) Buku la Yona liribe mathereo ankhani ndi mafunso omaliza alibe mayankho (Yona 4:9-11). Bukuli kuimira pamene Yona akudikira Mulungu kuti mwina ayamba kuziona ngati mmene iye amazionera. Mulungu akudikira chikhamu cha anthu amenene ali ngati Yona. Anthu amenewa samusunthika ndi kanthu, amakanika kuti amvetsetse komanso kuti atengepo gawo pa chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi.

BUKU LA YESAYA:

Buku la Yesaya ndi chitsanzo chabwino cha chikonzero cha Mulungu chokhudza dziko lonse lapansi:

Yesaya 17:12-13; 24:5-6; Akufotokoza mnene dziko lapansi liliri pamaso pa Mulungu.

Yesaya 40:12; 42:5; 44:24; 45:8, 12, 18; 48:13: Akulemekeza Mulungu Iye ngati olenga kumwamba ndi dziko lapansi.

Yesaya 14:12: Akuonetsera Satana ngati mdani wamaiko.

Yesaya 37:20, 64:4: Akutsindika cholinga ndi kukula kwa chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi

Yesaya 65:17; 66:22: Akuonetsera dongosolo la Mulungu lokhudza tsogolo.

Yesaya 40:15: Mmene Mulungu amalionera dziko lapansi.

Yesaya 45:22; 51:6: Kudandaulira kukupira ku maiko kuti afunefune chipulumutso kwa Mulungu.

Yesaya 43:8-12: Israeli anali mboni ya Mulungu pa maiko onse.

Yesaya 52:13-15: Mtumiki amene akutchulidwa apayu ndi Yesu. Iye adzazuzidwa chifukwa cha dziko lapansi mafumu a anthu amitundu adzaumva Uthenga Wabwino. Imfa ya Khristu Yesu inali ya anthu onse adziko lapansi. Uthenga wake umayenera kulalikiridwa ku dzipembedzo zonse za dziko lapansi.

Yesaya 54:1-5: Mau oti mbeu akuimilira mbeu yauzimu Ya Israeli komanso okhukupirira onse amitundu amene anamuzindikira Yesu Khristu. Mau oti kukuza malo okhalamo akutanthauza kukuza malo oti alandire ana a Mulungu ochokera pakati pa anthu a mitundu.

Yesaya 54:1-5: Mulungu adzachita mwachifundo ndi anthu amitundu. Iye sadzasiya kufikira onse atalandira uthenga Wabwino. Vesi 6 imafotokoza za mpulumutsi amene adzabweretsa anthu onse adziko lapansi pamodzi.

Yesaya 49:6-12: Kubwezeretsedwa kwa Israeli chinali chinthu chaching'ono kuyelekeza ndi chikonzero cha Mulungu cha dziko lonse lapansi. Iye Cholinga chake ndi chakuti dziko lonse lapansi lizindikire iye ndi kumupembedza iye mu chi mzimu ndi choonadi.

Yesaya 56:7: Nyumba ya Mulungu imeyenera kukhala nyumba yamapemphero ya mafuko onse.

Yesaya 59:16 - 60:5: Ndime imeneyi ikufotokoza kuti ngakhale kuti mdima unakuta dziko lapansi lonse chifukwa cha tchimo, koma Yesu anabwera ndi machiritso komansi kuunika pa dziko lapansi. Ndipo kuwala kumeneku kudzaonekera dziko lonse lapansi ndipo anthu onse amitundu adzazindikira zakuwala kumeneku.

Yesaya 2:4,19,21; 5:26; 11:4; 13:11,13; 24:1,19,21; 25:7; 26:21; 34:2; 64:2: Ma vesi onsewa amalosera za chiweruzo cha Mulungu maiko onse.

Yesaya2:2; 6:3; 11:9; 52:10; 55:5; 60:2; 61:11; 66:1, 18: Ma vesi awa amalankhuka za nthawi imene dziko lonse lapansi lidzadzala ndi chidziwitso cha Mulungu.

ANENERI ENA:

Zina mwa ndime zikulu zikulu kuchokera mmabuku aneneri ndi izi:

Yeremiya 1:5: Yeremiya anaitanidwa kukhala mneneneri kwa anthu amitundu

Yeremiya 9:24: Mulungu amaonetsera chifundo, chikondi, chiweruzo ndi ugwirowo pa dziko lapansi.

Yeremiya 23:5: Ulosi okhudza chiweruzo ndi chilungano chidzaperekedwa pa dziko lapansi lonse.

Yeremiya 18:7-10: Chisankho chikuperekedwa akwa anthu amitundu yonse

Yeremiya 27:5; 32:17; 51:15: Akulemekeza Mulungu ngati olenga dziko lapansi

Mulungu akulemekezedwa pakati pa anthu amitundu.

Yeremiya 4:2; 33:9: Maiko onse adzalemekeza Mulungu.

Yeremiya 5:9; 6:19; 7:28; 9:9; 10:10,11,25; 12:17; 23:5; 25:14,31; 51:25: Amalankhula za chiweruzo cha Mulungu pa maiko onse a dziko lapansi

Yeremiya 16:19-21: Cholinga cha Mulungu pa anthu amitundu chidzakwaniritsidwa kudzera mwa Israeli.

Yeremiya 33:9: Maiko onse a dziko lapansi adzamva za dzina la Mulungu

Maliro 3:37-39: Mulungu adzalanga munthu chifukwa cha ntchimo. .

Maliro 4:20: Ngakhale tikhala pakati pa anthu amitundu, koma tili pansu pa nthunzi wa Mulungu.

Ezekere 20:41; 36:23; 38:23; 39:7, 21: Ndime zonsezi zikuonetsera chifuniro cha Mulungu chofuna kuti dzina lake lidziwike dziko Inse lapansi.

Hoseya 1:10; 2:23Malo onse amene Mulungu samamudziwa, Iye adzavumbulutsidwa.

Yoweri 1:15: Yoweri anachenjeza za tsiku la ambuye limene ndi tsiku limene ndi nthawi yachiweruzo chiweruzo cha maiko onse.

Yoweri 2:28-32; 3:9-12: Ngakhale kuti maiko onse adzaweruzidwa ndi Mulungu, komanso iwo adzakumana ndi mphatso ya Mzimu Woyera komanso mtendere udzawatsata.

Yoweri 3:14: Amafotokoza chikhamu cha anthu adziko lapansi amene sadziwa Mulungu.

Amosi 4:13: Amosi ndi ananeri ena akulunge za Mulungu ngati Mbuye wa dziko lonse lapansi.

Amosi 9:11-12: Mulungu adzadzutsa maiko onse adziko lapansi otchedwa mudzina lake.

Obadaya 1:1: Mulungu watumiza anthenga pakati mafuko onse.

Obadaya 1:15: Tsiku lachiweruzo lidzabwera pa dziko lapansi.

Mika 4:1-3; 5:15; 7:16: Mulungu adzaweruzo maiko onse adziko lapansi

Nahumu 1:5: Dziko lonse lapansi lidzakhala pansu pa ulumuliro wa Mulungu.

Habakkuku 15; 3:12: Mulungu adzachita zinthu zodabwitsa pofuna kudzionetsera yekha padziko lapansi.

Habakkuku 2:4: Mfundo kulungamitsidwa mwachikhulupiriro ikukhazikitsidwa.

Habakkuku 2:14; 3:3: Akuloseza za tsiku limene dziko lapansi lidzadzadzidwe ndi ulemelero wa Ambuye.

Zefanaya 3:6, 8: Mulungu adzaweruza maiko onse oipa.

Hagayi 2:7, 21, 22: Mulungu adzagwedeza maiko onse ndi kuitanira iwo kwa iye.

Zekaliya 12:1: Mulungu akuonetseredwa ngati mlengi wa mzimu wa munthu.

Zekaliya 4:10: Chidwi cha Mulungu chili pa dziko lapansi.

Zekaliya 12:10; 13:1, 6, 7: Ulosi wa imfa ya Yesu chifukwa cha machimo a dziko lapansi.

Zekaliya 14:8-9: Mulungu adzakhala mfumu ya dziko lonse lapansi.

Malachi 1:11: dzina la Mulungu lidzalemekezedw pakati pa anthu onse amitundu

Kuchokera mu ndime zonsezi mukhoza kuoma kuti ndi zosatheka kuunikira ndime ina iliyonse mu zolemba za aneneri imene ikukamba za chikonzero cha Mulungu pa maiko onse adziko lapansi. Mu gawo la zoonjezera pophunzira tipeza ndime zokhudza dziko lapansi Pakato pa aneneri a Chipangano Chakale. Izi zikuthandizani kuti mumalizitse phunziro limeneri

KULUMIKIZANA NDI CHIPANGANO CHATSOPANO

Chipangano chakale chimamaliza ndi buku la Malaki. Pamene Chipangano chatsopano chimayamba ndi buku la Mateyu. Mu chaputala chikubwerachi tiona mmene Chipangano Chatsopano chimafotokozer a dziko lapansi.

Mu Chipangano Chakale Mulungu anagwiritsa ntchito Israeli ndi cholinga chofuna kuitanira anthu amitundi kwa Iye. Pokhala moyo owopa Mulungu, izi zimayenera kukopa anthu ku mzinda wa Yerusalemu ndi kwa Mulungu.

Israeli atakana Yesu Khristu, Mulungu akudzutsa gulu la antu mu Chipangano chatsopano. Gulu la anthu limeneri ndi mpingo umene anthu ake ndi onse amene ndi obadadwa mwatsopano. Kudzera mu mpingo, Mulungu akugwira ntchito ndi cholinga chofuna kudzionetsera Yekha kwa anthu onse a dziko lapansi. Mu Chipangano Chatsopano, Mulungu akutumiza Mpingo kuchokera ku Yerusalemu ndi kufikira maiko kapena mafuko onse.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Kodi mfundo yaikulu ya mau a Mulungu ndi chiani?

3. Fotokozerani mmene dziko lapansi likufotokozeredwa malingana ndi ma buku a chilamuro a Chipangano Chakale.

4. Fotokozerani mmene dziko lapansi likufotokozeredwa malinga ndi ma buku a mbiri a chipangao chakale.

5. Fotokozani mmene ma buku a ndakatulo amafotokozerera dziko lapansi.

6. Fotokozerani mwachidule mmene ma buku a uneneri mu Chipangano Chatsopano amafotokozerera dziko lapansi.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa Buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Gwiritsani ntchito ndime zili munsimuzi kuti mupitirize kuphunzira kaonedwe ka dziko lapaansi maligana ndi Chipangano Chakale. Mavesi amenewa akukamba za dziko lapansi, mafuko, ndi anthu amitundu amene ali anthu ena alionse amene si Ayuda.

Genesis: 6:5-7,11-13,17; 8:17,22; 9:1-2,11-17; 10:32; 11:1,8,9; 12:2,3; 13:16; 14:19,22; 17:4-6, 16, 20; 18:18; 21:13, 18; 22:18; 26:4; 28:14; 46:3

Eksodo: 8:22; 9:14, 16, 29; 19:5, 6; 32:10; 33:16; 34:10

Levitiko: 20:23

Numeri: 14:21

Deuteronome: 3:24; 4:27,39; 7:6; 9:4; 10:14; 14:2; 15:6; 18:9; 26:19; 28:1,10; 30:19

Yoswa: 2:11; 3:11; 4:24; 23:3, 9, 12, 23

Oweruza: 2:21-23

I Samueli: 8:5

II Samueli: 7:23; 22:50

I Mafumu: 8:23, 43, 53, 60; 11:2

II Mafumu: 5:15; 17:11, 15; 19:15, 19

I Mbiri: 16:14, 23, 24, 30, 31, 35; 17:21; 29:11

II Mbiri: 6:14, 33; 16:9; 20:6; 32:13

Nehemiya: 1:8; 5:9; 6:16; 9:6

Yobu: 9:24; 12:23; 19:25; 37:6, 12; 38:4

Masalimo: 2:1,2,8; 8:1,9; 9:5,8,15,17,19,20; 10:16,18; 18:7,43,49; 19:4; 22:27-29; 24:1; 25:13; 33:5,8,10,12,14; 34:16; 37:9,11,22; 44:2,11,14; 46:2,6,8-10; 47:2,3,7-9; 48:2,10; 49:1; 50:1,4,12; 57:5,9,11; 58:11; 59:5,8,13; 65:5,9; 66:4,7; 67:2,4,6,7; 68:8,32; 69:34; 72:8,11,17,19; 73:12,25;

74:12,17,20; 75:3,8; 76:8,9,12; 77:18; 78:55,69; 79:6,10; 80:8; 82:8; 83:4,18; 86:9; 89:11; 90:2;
93:1; 94:10; 95:4; 96:1; 99:1; 102:15,19,25; 104:5,9,13,14,24,30,32,35;
105:7;106:27,34,35,41,47; 108:3,5; 110:6; 111:6; 112:2; 113:4; 114:7; 115:2,15,16; 117:1;
Miyambo: 2:22; 3:19; 8:23, 26, 29, 31; 10:30; 11:31; 14:34
Mlaliki: 1:4; 3:11; 5:2,9; 7:20; 8:14,16; 10:7; 11:2; 12:7
Yesaya: 2:2,4,19,21; 5:26; 6:3; 11:4,9,12; 12:5; 13:11,13; 14:12,26; 17:12,13; 23:9; 24:1,4-6,19-
21; 25:7,8; 26:2,9,21; 34:2; 37:16,20; 40:12,15,17,21,28; 41:9; 42:4,5,10; 44:24; 45:8,12,18,22;
48:13; 49:6; 51:6,13,16; 52:10; 54:5; 55:5,9; 60:2; 61:11; 64:2,4; 65:1,17; 66:1,18,22
Yeremiya: 1:5; 4:2; 5:9; 6:19; 7:28; 9:9,24; 10:2,10-12,25; 12:17; 16:19; 18:7-9; 22:29; 23:5,24;
25:14,15,17,31,32; 27:5; 29:14; 31:7,10; 32:17; 33:9; 36:2; 46:28; 49:14; 51:15,20,25
Maliro: 4:20
Ezekieli: 5:5-8; 16:14; 20:41; 36:24; 38:23; 39:7,21; 43:2
Danieli: 4:35; 6:27
Hosea: 2:23; 6:3; 9:17
Yoweri: 2:17, 19, 30; 3:2, 11, 12
Amosi: 4:13; 9:8, 9, 12
Obadiya: 1:1, 15
Mika: 1:2,3; 4:2,3,7; 5:4,15; 6:2; 7:16
Nahumu: 1:5
Habakkuk: 1:5; 2:14, 20; 3:3, 6, 12
Zefaniya: 2:3, 11; 3:6, 8, 20
Hagayi: 2:7, 14, 21, 22
Zakariya: 1:10,11,15; 2:8,11; 4:10; 12:1,3,9; 14:2,3,9,16
Malaki 1:11

CHAPUTALA 5

DZIKO MU MAU A MULUNGU: CHIPANGANO CHATSOPANO

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi, muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi Yotsogelera osaonera.
- Kufotokoza mmene chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi chikuonetseredwa kudzera mu uthenga wakubadwa kwa Yesu.
- Kufotokoza mmene Yesu amaonera zinthu malingana ndi khalidwe Lake.
- Fotozani zimene Yesu anaphunzitsa zokhudza dziko lapansi ndi Utumiki wake wa dziko lapansi.
- Kufotokozera kufunika kwa mtanda wa Yesu Khristu mu chikonzero cha Mulungu cha dziko lapansi.

VESI YOTSOGOLERA

Ine ndalemekeza Inu pa dziko lapansi, m'mene ndinatsiriza nchito imene munandipatsa ndicite. (Yohane 17:4)

MAU OYAMBA

Chaputala ichi chipitiriza phunziro la dziko lapansi malingana ndi mmene limafotokozeredwa mu mau a Mulungu. Tifotokoza mmene Baibulo limaonera dziko lapansi. Kuchokera kubadwa kwa Yesu, imfa yake, ndi chiukitso chake, Baibulo limatsindika za dziko lapansi.

Kutsindika kwa mfundo ya dziko lapansi kukupitirirabe ngakhale Yesu atakwera kumwamba pamene mpingo unatuluka ndi kulalikira uthenga Wabwino.

KULENGEZEDWA KWA KUBADWA KWA YESU

Kulengezedwa koyamba Kwa kubadwa Kwa Yesu kumene kunalembidwa muchipangano Chatsopano kunalengezedwa ndi Angelo Kwa Mariya. Werengani nkhani imeneyi pa Luka

Kubwera kwa Yesu kunali kukwaniritsidwa kwa uneneri umene unaperekedwa mu Chipangano Chakale. Mariya anati mpulumutsi akubwera.

Monga analankhula kwa makolo athu) Kwa Abrahamu ndi kwa mbeu yace ku nthawi yonse. (Luka 1:55 8)

Werengani kulengezedwa kwa kubadwa kwa Yesu ndi mngelo pa Luke 2:10-14. “Onani, ndikuuzani inu uthenga wabwino wa cikondwero cacikuru, cimene cidzakhala kwa anthu onse” (vesi 10). Mau oti anthu onse akutanthauza kuti anthu onse a dziko lapansi. Kulengezedwa kwa kubadwa kwa Yesu kukuonetsera kuti iye anabwelera anthu onse a dziko lapansi.

Kunakakhala kuti panalibe umboni wina mu chipangano Chatsopano choonetsera kuti Yesu anabwelera anthu onse, ndime imeneyi ikakhala yokwana kuchitira umboni kuti Yesu anabwelera anthu onse.

KUEPEREKEDWA KWA YESU KHRISTU KU KACHISI

Cimene munakonza pamaso pa anthu onse, Kuunika kukhale cibvumbulutso ca kwa anthu a mitundu, Ndi ulemerero wa anthu anu Israyeli. (Luka 2:31-32).

Uneneri wina mu Chipangano Chatsopano okhudzana ndi Utumiki wa Yesu Khristu ku dziko lapansi unanenedwa ndi Kayafa, amene anali wamkulu wansembe wachiyuda. Iye anati:

kapena simuganiza kuti nkokoma kwa inu kuti munthu mmodzi afere anthu, ndi kuti mtundu wonse usaonongeke, Koma ici sananena kwa iye yekha; koma pokhala mkulu wa ansembe caka comweco ananenera kuti Yesu akadzafera mtunduwo; ndipo si cifukwa ca mtunduwo wokha ai, koma kuti akasonkhanitse pamodzi ana a Mulungu akubalalikawo. (Yohane 11:50-52)

YOHANE M'BATIZI

Yohane m'batizi anali munthu amene anasankhidwa ndi Mulungu ndi cholinga choti akonzekeretse anthu zakubwera kwa Yesu. Werengani za kubadwa kwa Yesu ndi chikonzero cha Mulungu pa moyo wake Luka1.

Yohane anatchula Yesu Khristu ngati “mwana wankhosa amene achotsa tchimo la dziko lapansi”

M'mawa mwace anaona Yesu alinkudza kwa iye, nanena, Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene acotsa cimo lace la dziko lapasi! (Yohane 1:29)

Mu chipangano Chakale, nkhusa zimawiritsidwa ntchito ngati nsembe yochotsa machimo kotere kuti Yesu Khristu amayenera kukhala nsembe ya uchimo. Iye ndi nsembe yagwiro yomaliza. Chifukwa chaichi, panalibenso chifukwa chopitirizira kupereka nsembe yamagazi anyama ndi cholinga choti munthu apeze chikhulupiriro.

Yohane anamutcha Yesu ngati “kuunika kwa dziko lapansi”

Uku ndiko kuunika kweni kweni, kumene kuunikira anthu onse akulowa m'dziko lapansi. Anali m'dziko lapansi, ndi dziko linalengedwa ndi iye, koma dziko silinamzindikira iye. (Yohane 1:9-10)

MACHITIDWE A YESU

Yesu anaonetsera chikondi chake cha dziko lapansi kudzera mu machitidwe ake pamene amatumikira padziko lapansi. Werengani nkhani ya kudyetsa anthu zikwi zisanu pa Mateyu 14:13-21. Kwa ophunzira iwo anaone chikhamu cha anthu ngati chinthu chosowetsa mtendendere. Koma Yesu Khristu anaona chinthu ichi ngati mwai waukulu kuti aonetsera chikondi chachikulu cha Mulungu.

Werengani nkhani yokhudza Yesu ndi mzimayi waku Samariya pa Yohane 4:142. Chitsanzo chimene chimaonetsera kuti palibe kusiyana pakati pa anthu amitundu yosiyana, komanso izi zikuonetsera chikonzero cha chipulumutso ku tchimo. Ndipo anthu aku Samariya anati:

Ndipo ananena kwa mkazi, kuti, Tsopano sitikhulupira cifukwa ca kulankhula kwako: pakuti tamva tokha, ndipo tidziwa kuti Mpulumutsi wa dziko lapansi ndi Iyeyu ndithu. (Yohane 4:42)

Iyi inali nthawi imene Yesu anagawana ndi ophunzira ake masomphenye ake a kholola lauzimu la dziko lonse lapansi. Iye anati:

Kodi simunena inu, kuti, Yatsala miyezi inai, ndipo kudza kumweta? Onani ndinena kwa inu, Kwezani maso anu, nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta. (Yohane 4:35)

Iye anauza ophunzira kuti:

Ndipo popita Yesu kucokera kumeneko, anamtsata Iye anthu awiri akhungu, opfuula ndi kuti, Muticitire ife cifundo, mwana wa Davide. (Mateyu 9:27)

Werengani Marko 14:1-9 pamene amafotokoza mmene Mariya anadzodzera Yesu. Anthu ena anadzudzula mkaziyu chifukwa chagwiritsa ntchito mafuta odula podzodza Yesu. Koma Yesu anati:

. . . Ponse pamene padzalalikidwa uthenga wabwino ku dziko lonse lapansi, ichinso chimene anachita mkazi uyu chidzanenedwa chikhale chonkumbira nacho.

(Marko 14:9)

Mau amene analankhula Yesu akuwonetsera kuti ndi cholinga cha Yesu kuti uthenga ufalikire ku dziko lonse lapansi.

Werengani nkhani yakuyeretsa kachisi pa Marko 11:15-17. Ndipo Yesu Khristu akutsindik za mfundo ya dziko lapansi.

Sicilembedwa kodi, Nyumba yanga idzachedwa nyumba yakupempheramo anthu a mitundu yonse? koma inu mwaiyesa phanga la acifwamba. (Marko 11:17)

lero lino malo ambiri opembedzera akusemphana ndi cholinga cha Mulungu. Ndikoyenera kuti tiyeretsedwe ndi Yesu ndi cholinga choti tikwaniritse cholinga cha Yesu:

Naonso ndidzanka nao ku phiri langa lopatulika, ndi kuwasangalatsa m'nyumba yanga yopemphereramo; zopereka zao zopsereza ndi nsembe zao zidzalandiridwa pa guwa la nsembe langa; pakuti nyumba yanga idzachedwa nyumba yopemphereramo anthu onse. (Yesaya 56:7)

CHIPHUNZITSO CHA YESU

Chiphunzitso cha Yesu Khristu komanso ndi machitidwe ake amatsindika chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi.

Werengani ndime zili munsimuzi:

Mateyu 5:13-16: Otsatira a Yesu Khristu amayenera kukhala mchere ndi kuunikwa kwa dziko lapansi.

Mateyu 6:10 imachitira umboni kuti Mulungu ali ndi chikozero choti chikwaniritsidwe pa dziko.

Mateyu 6:19; 16:26; Mark 8:36; Luka 12:22-32; Yohane 12:25: Sitikuyera kukhudzika ndi zinthu zadziko lapansi koma tikuyera kukhazikika pa zinthu za muyaya.

Mateyu 9:6; Marko 2:10; Luka 5:24: Yesu ali ndi mphamvu yokhululukira machimo.

Mateyu 13:35: Yesu avumbulutsa zinthu zokhudza chikonzero cha Mulungu ku dziko lapansi zimene zinali zobisika kuchokera pachiyemba.

Mateyu 21:43: Yesu akuloserera zakufalikira kwa uthenga Wabwino kwa anthu amitundu.

Luka 4:18-19: Onani kukhudzika kwa Yesu ndi zosowa za anthu pa dziko lapansi

Luka 12:49-51; Yohane 9:39; 12:31: Yesu anabwera ndi cholinga chofuna kubweretsa chiweruzo pakati pa tchimo ndi ugwiro kapena kuti kusiyinitsa pakati pa ugwiro ndi tchimo.

Luka 13:28-29: Yesu anaphunzitsa za kusunghanitsidwa kwa anthu onse a dziko lapansi pamapeto pa nthawi.

Yohane 3:16-18; 12:47; 17:6; 18:37: Ma vesi awa akufotokozera cholinga chake chobwelera padziko lapansi.

Yohane 6:33-51: Yesu anafotokoza kuti iye ndi mkate wa moyo kwa munthu wina aliyense ndipo kuti iye adzapereka thupi lake kuti apereke moyo ku dziko lapansi.

Yohane 7:7: Yesu analankhula za uchimo wa dziko lapansi.

Yohane 8:12: Yesu anadzionetsera yekha ngati kuunika kwa dziko lapansi. (Onaniso 9:5 ndi 12:46).

Yohane 8:23, 26: Yesu analankhula kuti iye siwapadziko lapansi koma iye anadza kudziko kuti afalitse uthenga wa Mulungu.

Yohane 12:47: Yesu anafotokoza anabwera kudzapulukutsa dziko lapansi.

Yohane 10:1-16: Ndime imeneyi imaloseza zakufaritsidwa kwa uthenga wabwino anthu amitundu “: nkhosa” chilichonse chorekanitsa kapakati pa Israeli ndi amitundu zidzachotsedwa

Yohane 12:20-36: Yesu anafotokoza kuti adzasonkanitsa anthu onse kwa Iye pakuferu machimo a dziko lapansi, iye adzabweretsa anthu onse adziko lapansi pamodzi.

Yohane 15:18-19; 16:33; 17:14-16: Otsatira ake a Yesu adzakanidwa chimodzimidzi mmene Yesu anakanidwira ndi dziko lapansi.

Yohane 16:8: Pamene mzimu woyera adzafika, iye atsutsa dziko lapansi tchimo.

MAFANIZO A YESU

Yesu anagwiritsa ntchito mafanizo pa utumiki wake. Mafanizo ndi zitsanzo zakuthupi zimene zimafotokozera choonadi chauzimu. Izi ndi nkhani zapadziko lapansi zimene zimakhala ndi tanthauzo la kumwamba. Mu mafanizo ake, Iye anaonetsera chikonzero cha Mulungu cha dziko lapansi.

FANIZO LA MSAMARIYA WABWINO (LUKA 10)

Anthu a Israeli sanali paubale wabwino ndi Asamariya. Funso lakuti kodi nansi wanga ndi ndani? Linali funso limene limakambidwa pakati pa atsogoleri achipembedzo. Nkhaniyi ikuonetsera maonedwe oyenera amene tikuyenera kukhala nao pa anthu achikhalidwe china.

FANIZO LA MWANA OLOWELERA (LUKA 15)

Khalidwe la mwana wamkulu mu nkhaniyi silikusiyana ndi khalidwe la atsogoleri achipembedzo a Israeli mu nthawi ya Yesu. Iwo samafuna kuti chikondi cha Mulungu chifalikire ku maiko kapena kumafuko ena. Iwo anali kutsutsana ndi ganizo loti anthu amaiko ena azindikire Mulungu.

Ngati tingafune kudzudzula Israeli, tiyenera kudziwa kuti pali anthu ambira mu mpingo walero amene ali ndi khalidwe lofanana ndi Isreali. Nthawi zambiri timakhala okhutitsidwa ndi madalitso a uthenga wabwino koma sitimakhudzika ndi anthu amene ali mu mdima chifukwa chopanda Yesu.

MPHWANDO LALIKULU (LUKA 14:16-24)

Nkhani imeneyi imaonetsera kuti Isreali anali oyamba kuitanidwa kulowa mu ufumu wa Mulungu, koma iye anaukana mwai umeneu. Chifukwa cha ichi, anthu amene anali kunja kwa ufumu wa Mulungu anaitanidwa mu ufumu umeneu.

FANIZO LA OLIMA MUNDA WAMPHESA :(MATEYU 21:34-44)

Yesu anaonetsera kuti Israeli amayenera kukhala osamala munda wamphesa, koma iye analephelera udindo wake.

TIRIGU NDI NANSONGOLE (MATEYU 13:36-43)

Munda mu fanizo limeneli ukuimira dziko lapansi. Mau a Mulungu amayenera kufalikira dziko lapansi lonse. Pamapeto pa zonse, Mulungu kholora lonse lauzimu lidzakoloredwa ndi Mulungu.

FANIZO LA OFESA (MARKO 4)

Mbeu imene ndi mau a Mulungu ikuyenera kufalikira pa dziko lonse lapansi. Mbeuyi idzagwera pa dothi lauzimu losiyanasiyana ndipo chifukwa chaichi zokolora kapena zotsatira zake zidzakhal zosiyanasiyana.

KUFALIKIRA KWA UFUMU WA MULUNGU (MATEYU 13)

Yesu anagwiritsa ntchito zitsanzo zosiyanasiyana pofuna kuonetsera mmene uthenga Wabwino udzafalikire pa dziko lonse lapansi. Werengani nkhani ya mbeu ya mpiru, ya chotupitsa, ya nyali, chuma chobisila ndi ukonde (Mateyu 13).

KUKANIDWA KWA YESU KHRISTU.

Chifukwa chakuti Israeli anakana uthenga umene Yesu anabwera nawo, Iye anagwiritsa ntchito zitsanzo zosiyanasiyana pofuna kuonetsera kukula kwa nkhanayi.

AKHATE KHUMI (Luka 17:12-19)

Mu nkhani imeneyi, wakhate mmodzi waku Samariya anabwelera ndi kudzathokoza ngakhale kuti akhate ena onse amene anali ochokera ku Israeli sanabwere kudzathokoza. Yesu anatsindika mfundo yoti anthu aku Samariya anali othokoza Mulungu pamene Ayuda amatenga kukonderedwa kwao pamaso pa Mulungu mwachizorowezi. Nkhami imeneyi ikusiyanyitsa kalandiridwe kwa uthenga pakati pa Israeli ndi anthu amitundu.

MZIMAYI WAKU SUROFONIKA (Mateyu 15:21-28)

Yankho loyamba limene Yesu anapereka limaoneka ngati lankhaza, koma Iye anali ndi cholinga chapadera. Yesu amafuna kuti chikhulupiriro chaka chachikulu kuti chionekere ndikukhala ngati chidzudzulo chachikulu kwa Israeli. Poyankha pempho lake ndi chizindikiro kuti chifundo cha Mulungu sichiona malire a fuko.

KAPOLO WA KENTURIYO (Mateyu 8:5-12)

Munthu ameneyu anali msirikari wachi Roma, koma Chifundo cha Mulungu chinamukhudza pamene kapolo wake anachiritsidwa. Yesu anati kwa iye nati:

Ndipo pakumva ici, Yesu anazizwa, nati kwa iwo akumtsata, Indetu ndinena kwa inu, ngakhale mwa Israyeli, sindinapeza cikhulupiriro coteri. (Mateyu 8:10)

Umboni wa Yesu pa vesi 11 ukounetsera kuti Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu ndi wa anthu onse:

Ndipo ndinena ndi inu, kuti ambiri a kum'mawa ndi a kumadzulo adzafika, nadzakhala pamodzi ndi Abrahamu, ndi Isake, ndi Yakobo, mu Ufumu wa Kumwamba; (Mateyu 8:11)

MTANDA NDI DZIKO LAPANSI

Imfa ya Yesu pamtanda paja inali chikonzero cha Mulungu cha dziko lapansi. Imfa Yake ndi maziko achipulumutso cha dziko lapansi. Uwu ndi uthenga waukulu wa Baibulo. Yesu nthawi zambiri amafotokozera za mphamvu ya mtanda kudziko lonse.

Mateyu 20:28 Iye anapereka moyo wake ngati nsembe yopulumutsa anthu onse a dziko lapansi.

Mateyu: 26:28 Baibulo limafotokoza kuti mwazi wake unaperekedwa ngati chikhulukiro cha machimo a anthu onse.

Yohane: 3:14-17. Yesu anaonetsera chikondi cha Mulungu pa dziko lapansi popereka mwana wake yekha ndi cholinga choti chofera machimo a dziko lonse lapansi.

Yohane 6: 51: imaanetsa kuti Iye adzapereka moyo wake ku dziko lapansi.

Yohane 12:32: Yesua anafotokoza kuti iye adzasonkhanitsa anthu onse kwa iye.

Mtanda ndi mutu waukulu mu zolembe za Paulo amene akufotokoza zolinga za mtanda pa dziko lonse lapansi.

Aroma 5:12-21: Chifukwa cha tchimo la Adamu, chilango chimaperekedw pa anthu onse a dziko lapansi. Chimodzimodzinso, kudzera mu imfa ya Yesu pamtanda, chiyero chinadza pa anthu onse.

II Akorinto 5:14-19: Yesu anafera anthu onse ndipo Mulungu kudzera mwa Yesu anadziyanjanitsa Yekha ndi dziko lonse lapansi.

Agalatiya 1:4 Yesu anadzipereka mwachifuniro chake chifukwa cha machimo athu.

Aefeso 3:6-11. Mafuko achikunja analandira zotsatira za imfa ya Yesu.

Akolose: 1:20. Mtendere ndi kuyanjanitsidwa ndi Mulungu kunabwera kudzera mu imfa Ya Yesu.

I Timoteo 1:15 Yesu anabwera kudzapulumutsa anthu ochimwa.

I Timoteo 2: 5-6 Pali nkhalak pakati mmodzi yekha amene anthu onse adziko lapansi akhoza kudza pamaso pa Mulungu yekhayo weniweni.

Ahaberi 9:11-12: Yesu anazunzidwa chifukwa chamachimo a anhtu onse.

I Yohane 4:9, 14 Yohane akufotokoza za mphamvu pa dziko lonse lapansi. Iye anabwera pa dziko lapansi ndi cholinga choti apulumutse dziko lonse lapansi.

NTCHITO YOMALIZA KALE

Pamene ifa inatsala pafupo pamtanda paja, Yesu anati:

Pamenepo Pilato anati kwa iye, Nanga kodi ndiwe Mfumu? Yesu anayankha, Munena kuti ndine Mfumu. Ndinabadwira ici Ine, ndipo ndinadzera ici kudza ku dziko lapansi, kuti ndikacite umboni ndi coonadi. Yense wakukhala mwa coonadi amva mau anga. (Yohane 18:37)

Kudzera mu imfa yake pa mtanda paja, Yesu analengeza za chikonzero cha Mulungu cha dziko lapansi kuti chakwaniritsidwa. Yesu anati:

Ine ndalemekeza Inu pa dziko lapansi, m'mene ndinatsiriza nchito imene munandipatsa ndicite. (Yohane 17:4)

KUTUMIDWA KWAKUKULU.

Patadutsa masiku atatu, Yesu Khristu anauka (Mateyu) Yesu anaonekera kwa ophunzira ake ataukitsidwa ndi asanabwelere kumwamba. Nthawi ina iliyonse imene amakumana nawo amatsindika kufunika kofalitsa uthenga Wabwino kudziko lonse lapansi. Iye anawapatsa ntchito yoti achite imene imachedwa kutumidwa kwakukulu. Muchaputala chamunsimu tiona mmene ophunzira ake anakwaniritsira kutumidwa kumeneku.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera osaonera

2. Fotokozerani mmene dongosolo la Mulungu linaonetseredwa kudzera mu kulengeza zakubadwa kwa Yesu.

3. Fotokozani mmene kaonedwe ka zinthu ka Baibulo kanaonetseredwa kudzera mu zochita za Yesu.

4. Fotokozani zimene Yesu anaphunzitsa zokhudza dziko lapansi ndi cholinga cha utumiki wake.

5. Fotokozani kufunika kwa mtanda wa Yesu mu dongosolo la Mulungu la dziko lapansi.

6. Kodi Yesu amatanthauza chiyani pamene amati wamaliza ntchito Ya Mulungu?

(Mayankho amafunso amenewa ali kumapeto kwa Buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Pitirizanibe kuphunzira zokhudza dziko lapansi powerenga ndime izi. Ndime zonsezi zimakamba za dziko lapansi malingana ndi Uthenga Wabwino.

Mateyu: 5:5,13,14; 6:19; 9:6; 10:34; 13:35,38-40,49; 16:19,26; 18:18,19; 21:43;

24:3, 7, 9, 14, 30, 35; 25:32, 34; 28:18-20

Marko: 2:10; 4:5,19; 8:36; 10:30; 11:17; 13:8,10,27,31; 14:9; 16:15

Luka: 1:70; 5:24; 11:50; 12:30, 49, 51; 18:30; 21:10, 25, 26, 33, 35; 24:47

Yohane: 1:9,10,29; 3:16,17,19,31; 4:42; 6:33,51; 7:7; 8:12,23,26; 9:5,39; 11:51,52;

12:19,25,31,32,46,47; 14:17,19,31; 15:18,19; 16:11,21, 28,33; 17:4,6,11,14-16,18,21,23;18:20,36,37; 21:25.

CHAPUTALA 6

MPINGO MU DZIKO LAPANSI

Pamepeto pa chaputala ichi muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza za Kutumidwa kwa Kukulu
- Kupereka umboni wa m'Baibulo wa kutumidwa kwakulu.
- Kufotokoza tanthauzo la Mpingo.
- Kufotokoza mmene mpingo unayambira.
- Kuzindikira mphavu zimene mpingo zili nazo.
- Kufotokoza chikonzero cha Mulungu cha kayendetsedwe ka mpingo.
- Kufotokoza Cholinga cha Mpingo.
- Kufotokozani nsanamira za uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu.

VESI YOTSOLERA:

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

MAU OYAMBA

Mu Chipangano Chakale Mulungu anadzutsa mtundu wa ana a Israeli ngati anthu amene akhoza kugwiritsa ntchito pofuna kuonetsera chikonzero chake chofun kupulumutsa dziko lapansi. Israeli atamkana Yesu, Mulungu anadzutsa gulu lina la anthu limene adzaligwiritse ntchito pa dziko lapansi. Ndipo gulu limeneli ndi mpingo. Mpingi uli ndi cholinga chapadera chimene Mulungu ali nacho ndi dziko lapansi. Phunziro ili lifotokoza za udindo wa mpingo mu dziko.

KUITANIDWA KWAKUKULU

Yesu atauka kwakufa, Iye anaonekera kwa ophunzira ake kangapo. Nthawi ina iliyonse imene amaonekera, iye amatsindika za udindo wao oti afalitse uthenga Wabwino padziko lonse lapansi. Ntchito imeneyi imene Yesu anapereka kwa ophunzira ake imatchedwa kuitana kwakukulu. Umeneu ndi udindo ofalitsa Uthenga Wabwino kwa cholengedwa chinachilichonse kapene kuti kwa munthu wina aliyense.

Ndime zili munsimuzi zikuonetsa kuitana kwakukulu kumene kunaperekedwa ndi Yesu Khristu.

Yohane 20:21-13:

Yesu anauza ophunzira ake kuti” Atate anga andituma ine chomwechonso ndi kutumani inu”. Mukhoza kuoma kuti kutuma kwakukulu kunayamba ndi Mulungu. Mu nthawi ya mnbuyomu Mulungu amatuma anthenga ake, ndi aneneri ndi cholinga chofuna kuitanira anthu kwa iye. Koma anthenga amenewa nthawi zambiri amakanidwa. Pamapeto pake Mulungu anatuma mwana wake, Yesu Khristu.

Chinachilichonse chimene Mulungu amkafuna kwa Yesu ngati otumidwa, amayembekezeranso zimenezi kwa ife chifukwa choti ife ndife otumidwa. Kodi ndi chiani chimene Yesu amayemebekezedwa kuchita?

- Iye anabwera pa dziko lapansi ndi cholinga cha umulungu.
- Iye anasiya zonse ndi kubwera.
- Iye anali okonzeka kukhala limodzi ndi munthu ochimwa.
- Iye anali okonzeka kufa pofuna kukwaniritsa cholinga chake.
- Iye anakwaniritsa cholinga chake pakulengeza ndi kuonetsera.
- Iye anamaliza ntchito imene Mulungu anamutuma kuti achite.

Luka 24: 45-59:

Taona kale ndime imeneyi mu chaputala chapitachi ngati vesi yotsogolera. Ndimeyi imaonetsera chikonzero cha Mulungu pa imfa ndi chiukitso cha Yesu. Ndipo ndimeneyinso ikuitanira tonse za kulalika Uthenga Wabwino kudziko lomse lapansi.

Sizokwanira kuti Yesu anafera machimo anthu chifukwa cha anthu amene ali osakhika samapulimutsidwa okha. Ndi kofunika kuti kulalikira uthenga Wabwino ndi cholinga choti anthu abwere kwa Mulungu. Chilango cha tchimo ndi Imfa (Aroma 6: 23) Chifukwa cha tchimo, muntu wina aliyense ndi wakumoto. Koma ndi okhawo amene analandira Yesu amene adzapulumutsidwa atakhululukidwa.

Ndicholinga cha Mulungu kuti munthu akapulumsidwe:

Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengerezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa. (2 Petro 3:9)

Palibe kukaika a kuti ndi cholinga cha Mulungu kuti munthu wina aliyense akapulumuke:

Pakuti, amene aliyense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka. (Aroma 10:13)

Koma...

Ndipo iwo adzaitana bwanji pa iye amene sanamkhulupirira? Ndipo adzakhulupirira bwanji iye amene sanamva za iye? Ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? (Aroma 10:14)

Mulungu akufuna kuti munthu wina aliyense apulumutsidwe, koma izi zikhoza kuchitika pokhapokha ngati wina atalalikira uthenga Wabwino.

MARKO 16:14-16:

Lamulo limene likuperekedwa apa ndi lakuti tipite kapena kuti “Mukani.” Kumene tikuyenera kupita mu dziko lapansi. Uthenga Wabwino ukuyenera kularikidwa ku cholengedwa china chili chonse. Yesu analonjeza kuti adzakhala ndiwo amene adzatuluka kukalalika powapatsa mphamvu ya zodabwitsa. Anthu ena amafuna zodabwitsa mu utumiki pamene sakukwaniritsa lamuro loti timuke ndi kukalalika Uthenga Wabwino kotere kuti amakhala odabwa pamene zizindikiro ndi zodabwitsa sizikuchitika.

YOHANE 15:16

Yesu anasankha ndikudzodza ife kuti tikabale zipatso. Werengani chaputala chonsechi chimene chikukamba za kubala zipatso. Muphonzira za Yesu ngati mphesa ndipo ife ngati nthambi. Ndi moyo wa Yesu osefukira mwa ife umene umabweretsa kholora lauzimu.

MATEYU 28:16-20:

Yesu anati “phamvu ndi ulamuliro zonse zaperekedwa kwa ine.” Chifukwa cha ichi Yesu anali ndi ulamuliro otumiza ophonzira ake kuti alalikire uthenga Wabwino dziko lonse lapansi.

Onanani zinthu izi mu ndime zimenezi:

Anthu: Yesu akutuma anthu ndipo anthu amenewa ndi okhulupilira onse.

Mphamvu: “Mphamvu zonse” Izi ndi mphamvu zimene Mulungu amapereka polimbikitsa nthenga kuti zitukuke ndikulalika Uthenga Wabwino. Imeneyi ndi mphamvu ya Mzimu Woyera osati mphamvu ya munthu kapena njira za umuthu.

Chinthu chofunika komanso choyamba: “Mukani” ndi kulamuliridwa kumene kukupezeka mu ndime imeneyi. Izi zikuonetsa kuti Kufalitsa uthenga Wabwino chikuyenera kukhala chithu chofunikwa kwambiri pamoyo wanthu komanso kuti ndi zinthu zimene sitingasankhe kusachita.

Chikonzero: kuphonzitsa ndi kulalikira ndi njira zimene ziyenera kugwiritsa ntchito.

Choling: cholinga ndi kupanga ophonzira dziko lonse lapansi. Izi zikuonetsera kukula kwa kutumidwa kumeneku.

Anthu: Anthu amene ayenera kufikiridwa ndi anthu onse amitundu yonse. Kukula kwa kutumidwa kumeneku ndi kwa dziko lonse lapansi.

Kupezeka: Amene ali nafe ndi Yesu amene ndi mnthenga wamkulu. Iye amapereka chitsogozo kudzera mwa Mzimu Woyera pamene kukukwaniritsa kutumidwa kumeneku.

Zophonzitsa: mfundop zoti anthu aphonzitsidwe ndi Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu.

Mateyu 24:14 Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikiwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu h mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Matthew 24:14)

Uthenga umeneu umatchedwa Uthenga wa Mulungu (I Atesalonika 2:9) Uthenga wa Kristu (I Atesalonika 3:2). Uthenga wa Paulo (Aroma2:6). Izi zikutanthauza kuti pali kutsatana kwina kuli konse pamene tikuti Uthenga wa Paulo chifukwa chakuti Mulungu ndiye mwini Uthenga Wabwino. Yesu anakwaniritsa chikonzero cha Mulungu. Anthu ngati Paulo anangolandira chabe Uthenga Wabwino komanso anali mnthenga wa Uthenga Wabwino.

Uthenga umalandiridwa kudzera mu vumbulutso la Mulungu, si chiphunzitso cha munthu ayi:

Pakuti ndikudziwitsani inu, abale, za Uthenga Wabwinowo wolalikidwa ndi ine, kuti suli monga mwa anthu. Pakutitu sindinaulandira kwa munthu, kapena sindinauphunzira, komatu unadza mwa bvumbulutso la Yesu Kristu. (Agalatiya 1:11-12)

Pa 1 Akorinto 15:1-11, choonadi cha uthenga Wabwino chafotokozeredwa mwachidule. Nsanamira ya uthenga umeneu ndi Yesu, utumiki wake, imfa yake yofera machimo kumanso kuonekera kwakwe atauka kwa kufa. Uthenga Wabwino ndi wachisomo komanso chikhulupiriro.

Uthenga Wabwino ndi choonadi cha Mulungu:

Cifukwa ca ciyembekezo cosungikira kwa inu m'Mwamba, cimene mudacimva kale m'mau a coonadi ca Uthenga Wabwino, (Akolose 1:5)

Uthenga Wabwino ndi mphamvu ya Mulungu yobweretsa chipulumutsu.

Pakuti Uthenga Wabwino sundicititsa manyazi; pakuti uti mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira; kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene. (Aroma 1:16)

MPINGO

Kutumidwa kwakukulu kunaperekedwa ku mpingo ndi Yesu. Mpingo umatumikira chimodzimodzi mmene Israeli amatumikira mu Chipangano Chakale. Mpingo ndi gulu la anthu limene Mulungu amagwiritsa ntchito pofuna kudzionetsera yekha ku dziko lapansi.

Ndi zofunika kufotokoza tanthauzo la mpingo. Mpingo umene ukutchulidwa apa sichinyumba ayi komanso mpingo sichipembedzo. Tikhoza kufotokoza mpingo mu magawo awa.

DZIKO LONSE LAPANSI:

Mpingo umapangidwa ndi anthu onse okhulupirira Yesu Khristu. Ndi chiyanjano cha anthu onse okhulupirira amene anabadwa mwatsopano komanso amene amamvera Mulungu.

Mau oti mpingo amatanthauza kuti “kuitana” kapena “oitaniidwa” Mpingo umapangidwa ndi anthu amene anaitanidwa kuchokera ku Ufumu wa satana ndi kupita ku ufumu wa Mulungu. Awa ndi anthu amitundu yonse, chikhalidwe chinachilichonse komanso anthu a chinenero chinachilichose amene anamulandira Yesu ngati mbuye.

Mpingo ukutchedwa thupi la khristu Yesu. Izi zikutanthauza kuti mpingo ndi gulu la anthu okhawo amene abadwa mwatsopano.

MIPINGO YAM'MADERA:

Ndi cholinga chofuna kulalikirira uthenga Wabwino, ndi kuchita chiyanjano okhulupirira amakumana m'mdadera ndi kuchita chiyanjano. Umu ndi mmene zinthu zimachitikira mu Chipangano Chatsopano.

CHIKHALIDWE CHA MPINGO

Baibulo limagwiritsa ntchito zizindikiro zimene zimafotokoza chikhalidwe, ntchito komanso malo enieni a mpingo.

Mu ndimene zili munsimuzi, mpingo ukutchedwa zinthu izi:

Munthu watsopano: Aefeso 2:14-15

Thupi la Khristu: Aefeso 1:22-23; 5:30; I Corinthians 12:27

Kachisi wa Mulungu Aefeso 2:21-22; I Corinthians 3:9,16; I Timothy 3:15; I Peter 2:5

A ufumu Osankhika: I Petro 2:5,9; Chivumbulutso 1:6; 5:10

Mkwati wa Yesu: II Akorinto 11:2

Nyumba ya Mulungu: Aefeso2:19

NKhosha za Mulungu: Yohane 10:1-29; I Petro5:3-4; Ahebri 13:20; Machitidwe20:28

Mpingo wa Mulungu: Machitidwe 20:28; I Akorinto 1:2; 10:32; 11:22; 15:9; I Timoteo 3:5; I Atesalonika 2:14

Mpingo wa Mulungu wa Moyo: I Timoteo 3:15

Mpingo wa Khristu: Aroma 16:16

CHOLINGA CHA MPINGO

Mpingo uli ndi zolinga zingapo zimene zili zofunika, ndipo zina mwa zolinga zimenezi ndi izi: kupembedzera, chiyanjano, kutumikira zosowa za munthu. Koma cholinga chenicheni cha mpingo ndi Kufalitsa Uthenga Wabwino kapena kuti cholinga cha mpingo ndi kukwaniritsa Kutumidwa kwakukulu.

Satana analimbana ndi cholinga cha mpingo oyamba mu njira zambiri. Iye anayesayesa kulepheletsa kufalitsa Uthenga Wabwino kudzera mu chizuzo, ziphunziztso zonyenga komanso ntchimo. Koma izi ndi njira zimene Satana akugwiritsabe ntchito lero lino. Palinso chinthu china cholepheleretsa kuti mpingo ukwanitse cholinga chake: chinthu chimenechi ndi kutengeka kwa atsogoleri ndi kuchita ntchito zabwino, chimene ndi chinthu chopangitsa kuti mpingo uchoke pa cholinga chake ngati mmene Yesu anakonzera. Werengani Machitidwe chaputala 4. Pa ndime imeneyi, panali ntchito zambiri zabwino zimene zimachitika koma atsogoleri amene amachita izi amasokonekera chifukwa chakuti amayiwara kufunika kwa nthawi kumva mau a Mulungu kapena kupemphera.

Zosowa za anthu ndi zambiri koma Yesu anakamba kuti tidzakhala ndi osauka pakati panthu nthawi zonse. Mpingo ukhoza kukumana ndi zosowa za anthu ngati mmene zimachitikira mu mpingo woyamba mu nthawi ya Chipangano Chatsapano. Koma cholinga chenicheni cha mpingo sikuthandiza anthu ku zinthu zawo zakuthupi, cholinga chenicheni ndi Kulalikira uthenga Wabwino. Mpingo ukhoza kutumikira ku zinthu izi koma pamene izi zikuchitika, uthenga Wabwino uyenera kulalikidwa.

Chitsanzo chabwino tikuchipeza pa Aroma 9 ndi 10. Mtumwi Paulo amazindikira zosowa zakuthupi za Ayuda. Iye akuzindikira chizuzo chimene Ayuda amakumana nacho, koma ngakhale izi zinali choncho iye chimene chimamukhudza kwambiri chinali zosowa zauzimu za anthu. Khumbo lake pa Israeli linali loti Israeli apulumutsidwe (Aroma 10:1). Cholinga chenicheni cha mpingo ndi kufalitsa Uthenga Wabwino ndi cholinga choti anthu akatumikire Mulungu.

NTHAMBI YOTUMIZA

Njira imene Mulungu anagwiritsa ntchito ndi yotumiza. Chifukwa chachikondi Mulungu Tate anatumiza mwana wake”

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Yohane 3:16)

Yesu amatuma ife kuti tifalitse Uthenga Wabwino. Chifukwa cha ichi, mpingo wina ulionse uyenera kukhala mpingo otumiza anthu kufalitsa Uthenga Wabwino. Mpingo uyenera kutuluka chifukwa chachikondi kuti akafalitse Uthenga Wabwino. Mulungu anadzutsa mpingo ndi Cholinga kotere kuti mpingo sunangopatsidwa mwai wapadera koma iwo unapatsidwa udindo ndi cholinga. Tikuyenera kutsata chitsanzom cha Yesu pofalitsa Uthenga Wabwino.

Mpingo wina uli onse wazunguliridw ndi guru la anthu ambiri amene alibe Mulungu komanso opanda chiyembekezo. Uwu ndiye udindo wathu wathu waukulu komanso oyamba. Izi zikugwirizana ndi Mau a Paulo amene akupezeka pa (Afilipi 2:12-16) ndipo mau omwewa akulankhuridwanso ku mipingo yaku Aefeso, Akorinto, Tesalonika ndi ku Kolosse. Koma uthenga omweu ukuperekedwanso ku mpingo wa lero.

Ku Efeso, Paulo akutsindika cholinga cha Mpingo:

Ndi kuwalitsira onse adziwe makonzedwe a cinsinsico, cimene cinabisika ku yambira kale kale mwa Mulungu wolenga zonse; kuti mu Eklesia azindikiritse tsopano kwa akulu ndi maulamuliro m'zakumwamba nzeru ya mitundu mitundu ya

Mulungu, monga mwa citsimikizo mtima ca nthawi za nthawi, cimene anacita mwa Kristu Yesu Ambuye wathu: Lord. (Aefeso 3:9-11)

MPINGO OBADWA NDI MPHAMVU

Yesu anasiira ophunzira ake ntchito yaikulu imene inali kulalikira Uthenga Wabwino dziko lonse lapansi. Koma Iye sanangowapatsa udindo opanda kupawapatsa mphamvu. Iye anawapatsa mphamvu zapadera ndi cholinga choti akwaniritse ntchito imeneyi.

Yesu anauza ophunzira ake kuti adzalandira mphamvu kudzera mwa Mzimu Woyera.

Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko. (Macitidwe 1:8)

Anthu okwana khumi ndi mmodzi anapatsidwa ntchito yowoneka ngati yosatheka. Koma iwo sanapange komiti yoti iyendetse dongosolo lonse la kumene apaite. Iwo sanatenga chopereka kuti athe kuona kuti awone kumene angathe kupita. Iwo sanachite kuvota kuti atsate zotsatira za masankhowo. Anthu amenewa anali pa chipinda chapamwamba ndikudzipereka ku pemphero. Izi zikuonetsa kuti mpingo unabadwa kudzera muchionetsero cha mphamvu yaikulu.

Machitidwe 2 amaonetsera zimene zinachitika pa tsiku limene Mzimu Woyera anadza.

Mphamvu ya Mzimu imene inaperekedwa inali ndi cholinga chapadera. Cholinga chimenechi chinali kuti akafalitse Uthenga Wabwini dziko lonse lapansi. (Machitidwe 1:8). Machitidwe chaputala 2 amaonetsera chiyambi cha mpingo oyamba. Pamene Mzimu Woyera anaperekedwa, Petro analalika ndipo anthu okwana zikwi zitatu anatembenuka mtima. Anthu awa ndi amene anapangsa mpingo woyamba. Mbiri yakuchuluka kwao komanso utumiki wao ikuonetseredwa mu buku lonse la Machitidwe.

KAYENDETSEDWA KA MPINGO

Kuti mpingo ukwanitse cholinga chake, Mulungu wakhazikitsa dongosolo komanso mfundo zakayendetsedwe ka zinthu mu mpingo. Anthu amu mpingo amakhala pa ubale wa munthu ndi mlonga wake mwa uzimu. Anthuwa amakhala thupi la Khristu Yesu limene Iye ali mutu wa thupi limeneli. Chifukwa cha ichi, mpingo uyenera kugwira ntchito ndi umodzi ngati mmene thupi limapangira. Mpingo ukuyenera kugwira ntchito panso pa ulamuliro wa Yesu Khristu.

Mulungu amakhazikitsa ma udindo apadera mu mpingo ndipo ena mwa adindo amenewa ndi aphunzitsa, aneneri ndi atumwi. Koma Mulungu aperekanso mphatso zosiyanasiyana za Mzimu Woyera kwa okkhulupirira ndi cholinga choti zigwire ntchito yautumiki.

UTUMIKI WA MPINGO OYAMBA

Buku la Machitidwe mu Chipangano Chatsopano ndi nkhani ya mmene mpingo unakwaniritsira kutumidwa kwa kukulu kolalika Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi. Anthu zikwi zikwi anapulumsidwa mu masabata ochepa okha zinthu zimene zalembedwa pa Machitidwe 2 zitangochitika. Pakudutsa kwa nthawi, chiwerengero cha anthu okhulupirira chinachuluka mu mzinda wa Yerusalemu.

Mulungu analora chizuzo kuti chiwagwere okhulupirira oyamba ndi cholinga choti uthenga ufalikire. Iwo anafalikira mu Yudeya monse ndi ku Samariya.

Ndipo Saulo analikubvomerezana nao pa imfa yace. Ndipo tsikulo kunayamba kuzunza kwakukuru pa Mpingo unali m'Yerusalemu; ndipo anabalalitsidwa onse m'maiko a Yudeya ndi samariya, koma osati atumwi ai. Pamenepo ndipo iwo akubalalitsidwa anapitapita nalalikira mauwo. (Machitidwe 8:1,4)

Mmodzi mwa okhulupirira amene anapita ku Samariya kukalalikira anali Filipino. Uwu unali utumiki oyamba otumikira anthu achikhalidwe china chosiyana (Machitidwe 8). Pa Machitidwe 9, Mulungu akudzutsa mtumwi Paulo kuti afalitse Uthenga Wabwino Kwa anthu amitundu komanso kuti akhale mntenga ku mafuko onse a dziko lonse lapansi.

Pa Machitidwe 13, dongosolo lenileni lofaritsa uthenga Wabwino ku dziko lapansi lonse ikukhazikitsidwa. Paulo ndi Barnanana anaitanidwa ku utumiki wa kwa anthu azikhalidwe

zosiyanasiyana. Iwo amayenera kukafaritsa uthenga kwa anthu achikhalidwe china osati Israeli yekha.

Ndipo pakumva ici amitundu anakondwera, nalemekeza mau a Mulungu; ndipo anakhulupira onse amene anaikidwiratu ku moyo wosatha. Ndipo mau a Ambuye anabukitsidwa m'dziko lonse. (Macitidwe 13:48-49)

Mpingo oyambilira unakwaniritsa kutumidwa kwakukulu kotere kuti chifukwa cha izi, iwo anatembunuza zinthu kwambiri (Machitidwe 17:6). Cholinga cha Mulungu chinakwaniritsa pamene anthu amitundu yosiyana anapangidwa kukhala amodzi chifukwa cha mwazi wa Yesu:

Ndipo ndi mmodzi analenga mitundu yonse ya anthu, kuti akhale ponse pa nkhope ya dziko lapansi, atapangiratu nyengo zao, ndi malekezero a pokhala pao; (Macitidwe 17:26)

Koma m'mitundu yonse, wakumuopa iye ndi wakucita cilungamo alandiridwa naye. (Macitidwe 10:35)

UMBONI OCHOKERA MA GAWO ENA A CHIPANGANO CHATSOPANO

Phunziro ili latsindika kwambiri za udindo wa mpingo pa dziko makamaka mu Buku la Machitidwe. Chipangano chanse Chatsopano chinalembedwa kwa okhulupirira oyamba komanso chinalembedwa ndi okhulupirira amanewa motsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo mu gawo limeneli muli ma vesi a chikonzero cha Mulungu cha dziko lapansi.

Mu gawo la zoonjezera pophunzira liri ndi mavesi amene akuthandizeni kuti muphunzire zambiri zokhudza dziko lapansi. Wonetsetsani kuti mwakwaniritsa gawo limeneli kutui mukuze chidziwitso chanu cha kaonedwe kwa dziko lapansi malingana ndi Baibulo.

Chinthu chimodzi chofunikwa kwambiri pamene mukuwerenga gawo la zoonjezera pophunzira gawo lokhudza Chipangano Chakale. Pa Aroma 4, Paulo akutchula za malonjezano amene anaperekedwa kwa Abrahamu. Limodzi mwa malonjezano amenewa ndi lakuti Iye adzakhala mdalitso kudziko lonse lapansi. Malingana ndi Chipangano Chatsopano, okhulupirira ndi mbumba ya Abrahamu (Agalatiya 3). Izi zikutanthauza kuti madalitso onse Abrahamu aperekedwa kwa okhulupirira. ife ndi gawo limodzo lodalitisa anthu onse a dziko lapansi.

MPINGO MU DZIKO LAPANSI

Kuchokera mukuphunzira kwa Chipangano Chakale, ntchito ya Mpingo pa dzikolapansi ikhoza kufotokozeredwa mwachidule motere:

1. Mpingo ukuyenera kufalitsa za yesu ngati mpulumutsi kwa anthu komanso kudziko lonse lapansi, iye ayenera kuonetseredwa ngati Mbuye wa ulamuliro onse wa dziko lapansi amene adzaweruze anthu onse.
2. Mpingo ukuyenera kutsogolera anthu kuti akhale paubale wabwino ndi Yesu khristu ndi cholinga choti akumane ndi chikhukululukiro cha machimo awo ndi kukhala moyo watsopano.
3. Kudzera mu ubatizo wa madzi, kuphunzitsa ndi kulalikira, mpingo ukuyenera kukhazikitsa okhulupirira mu chiphunzitso ndi chikhaliidwe chachi Kristu. Mpingo ukuyenera kuphunzitsa anthu kuti amvere zinthu zonse zimene zalamuliridwa mu Baibulo.
4. Mpingo ukuyenera kubweretsa anthu onse okhulupirira kuti akhale pa mpingo wamdere umene ndi wamphamvu komanso umene ukakwaniritsa kutumidwa kwakukulu.
5. Mpingo wina uli onse wamdera ukuyenera kulandira mphamvu ya Mzimu Woyera ndi kutha kudzutsa gulu lina la anthu okhulupirira.

Mpingo ukuyenera kutuluka kudziko lapansi ndi kulalikira Uthenga Wabwino. Chaputala chikubwerachi chikufotokoza za dziko limene likudikira kulandira Uthenga Wabwino, dziko limene mpingo waitaniridwa kuti ukatumikire.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Fotokozani tanthauzo la kutumidwa kwakukulu

3. Perekani ndime zitatu zofotokozera kutumidwa kwakukulu

4. Kodi mau oti mpingo amatanthauza chinai malinga ndi Baibulo?

5. Kodi mpingo unayamba bwanji?

6. Kodi ndi mphavu iti imene imathandiza mpingo kuti ukwanitse cholinga chake pa dziko lapansi?

7. Fotokozerani chikonzero cha Mulungu pakayendetsedwe ka mpingo

8. Fotokozerani cholinga cha mpingo mu chikonzero cha Mulungu

9. Kodi mfundo zazikulu kapena nsanamira za Uthenga Wabwino ndi Chiani?

(Mayankho amafunso amenewa ali kumapeto kwa buku ili)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Ngati muli ndi chidwi choti mudziwe mmene Uthenga unafalikira ku dziko lonse lapansi makamaka Baibulo litamalizidwa kulembedwa, mukhoza kupeza buku lotchedwa “*From Jerusalem to Iryiani Jaya*” Bukuli linalembedwa ndi Rute Tucker. ndipo linasindikizidwa ndi Zondervan Publishing House, Michigan USA.

Malingana ndi bukuli, Kufalitsa Uthenga Wabwino ku mafuko onse kwa gawidwa mu zigawo zitatu chiyambireni Chipangano Chatsopano.

GAWO LOYAMBA

Kufalikira kwa uthenga wabwino ku madera ozungulidwa ndi madzi a dziko lonse lapansi. Izi zinachitika chifukwa cha munthu otchedwa William Carely.

GAWO LACHIWIRI

Kufarikira kwa Uthenga Wabwino kumadera a pantunda a dziko lapansi ndipo ntchito imeneyi inakwaniritsidwa ndi munthu otchedwa Hudson Taylor.

GAWO LACHITATU

Izi zinakhazikitsidwa ndi munthu otchedwa Townsend ndipo zikupitilira kufikira lero lino. Cholinga chenicheni ndi kufikira anthu amene sanafikiridwe ndi uthenga Wabwino.

2. Mu chaputala chomaliza, munaona ndime mu chipangano chatsopano za ma buku a Mateyu, marko, ndi Yohane. Ndime zili pansizi ndi ndime zimene zikutchula za dziko lapansi kuchokera buku la Machitidwe kufikira Buku la Yuda Muchipangano Chatsopano.

Machitidwe: 1:8; 2:5; 3:25; 4:24,26; 10:28,35; 13:47; 14:15,16; 15:18; 17:6,24,26,31

Aroma: 1:5,8,20; 3:19; 4:13,17,18; 5:12,13; 9:17,28; 10:18; 11:12,15; 12:2; 16:25,26

I Akorinto: 1:20,21,27,28; 2:6-8,12; 3:18,19; 8:4,5; 10:11,26,28; 11:32; 15:47-49

II Akorinto: 4:4; 5:19; 7:10

Agalatiya: 1:4, 16; 2:9; 3:8; 4:3

Aefeso: 1:4, 10, 21; 2:2, 12; 3:9, 21; 6:12

Afilipo: 2:10, 15; 3:19

Akolose: 1:16, 20; 2:8, 20; 3:2, 5

I Timoteo: 1:15; 3:16; 6:7, 17 II Timoteo: 1:9; 4:10

Tito: 1:2; 2:12

Ahebri: 6:7; 9:26; 11:7; 12:25, 26

Yakobo: 2:5

I Petro: 1:20 II Peter: 2:5; 3:6, 7

I Yohane: 2:2, 15-17; 3:1; 4:3, 4, 9, 14, 17; 5:4, 5, 19 II John: 1:7

CHAPUTALA 7

DZIKO LOYEMBEKEZA

Pamapeto pa phunziro ili mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi Yotsogolera osaonera.
- Kufotokozero mmene Uthenga Wabwino ukufarikira pa dziko lapansi.
- Kufotokozero tanthauza la guru losafikiridwa.
- Kufotokokoza tanthauzo la anthu ofikiridwa.
- Kuzindikira magulu asanu a anthu osafikiridwa.
- Kufotokoza tanthauzo la dziko lotsekeka.

VESI YOTSOGOLERA.

Zokolola ndizambiri koma antchito ndi ochepa. (Mateyu 9:37)

MAU OYAMBA

Mu chaputala ichi muphunzira zammene uzimu wa dziko lapansi uliri, dziko limene likudikira Uthenga Wabwino w ufumu wa Mulungu. Kumbukira chitsanzo cha kholora chimene yesu anagwiritsa ntchito pofuna kuonetsera zosowa zauzimu za dziko lapansi. Pamapeto pa chaputala ichi mumvetsetsa chifukwa chimene Yesu ananenera mau awa:

Pomwepo ananena kwa ophunzira ace, Zotuta zicurukadi koma anchito ali owerengeka. (Mateyu 9:37)

DZIKO LAPANSI LONSE

Yesu anauza ophunzira ake:

Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: (Mateyu 28:19)

Ndipo ananena nao, mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. (Marko 16:15)

ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhululukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luka 24:47)

Ndipo pamene anapita pambali pa Musiya, anatsikira ku Trowa. (Macitidwe 16:8)

MALO ENA ALIONSE

Pali miyandamiyanda ya anthu yopezeka mmamidzi osiyanasiyana kapena kuti malo osiyanasiyana amene sanamve uthenga Wabwino. Anthu amenewa ndi gawo limodzi la dziko lapansi. Chifukwa cha ichi, tikhoza kunena kuti sitinafikirebe dziko lonse lapansi.

KUZILANKHULO

Kufalitsa uthenga Wabwino kuzilankhulo zonse kukutanthauza kumasulira uthenga Wabwino kupita muzilankhulo zonse za dziko lapansi. Baibulo ndi uthenga Wabwino wa Mulungu kwa munthu. Ndipo njira yabwino yolumikizirana ndi anthu ndi kulankhula muchinenero chimene iwo amalankhula.

Pakadali pano pa zilankhulo pafupifupi zikwi zisanu ndi ziwiri zimene zimalankhulidwa ndi anthu dziko lonse lapansi. Anthu ambiri alibe Baibulo limene ndi lolembedwa mu chiyankhulo chawo. Anthu amenewa sanapeze mwai oti khoza kuwerenga Uthenga ochokera kwa Mulungu olembedwa. Chifukwa cha ichi, zilankhulo za dzikola lapansi sizinafikiridwebe.

CHIWERENGERO CHA DZIKO LAPANSI

Sitinakwanitse kufikira zilakhulo zonse za dziko lapansi, maiko onse a dziko lapansi komanso sitinakwanitse kufikira chiwerengero cha anthu onse a dziko lapansi. Mu nthawi ya Yesu, anthu amakhulupirira kuti kunali anthu okwana 250 miliyoni. Koma chiwerengero chimenechi chinakwera ndi kawiri pamene chimafika chaka cha 1600. Kuchokera mu nthawi ya Adamu kufikira chaka cha 1500 imene ndi nthawi imene Yesu anali atabadwa kale, chiwerengero cha anthu chinali chitafika anthu okwana 500 Miliyoni. Pamene chimafika chaka cha 1850, chiwerengero cha dziko lapansi chinali chitakula ndi kawiri. Ndipo pakadali pano pa dziko lapansi pali anthu okwana ma biliyoni.

Ngakhale mu mizinda ikuluikulu imene muli mipingo yambiri, pali anthu ambiri amene sanamvepo za Yesu Khristu. Chifukwa cha ichi, dziko lapansi silinafikiridwebe ndi Uthenga Wabwino chifukwa pali miyandamkiyanda ya anthu amene sanamve uthenga wabwino.

MAGULU A ANTHU

Tikati tiliwone dziko lapansi ngati maiko, tikhoza Kunena kuti maiko onse a dziko lapansi afikiridwa chifukwa chakuti dziko lina lilironse liri ndi mboni za Uthenga Wabwino. Pakadali pano mu dziko lina lilironse muli anthu kapena mipingo yokhazikika. Koma izi sizikutanthauza kuti mtundu wa anthu wina uli onse kapena kuti mutundu ya anthu yonse yafikiridwa ndi Uthenga Wabwino ngati mmene zimakambiridwa pa Chibvumbulutso 5:9.

Pamene Yesu amakamba za dziko lapansi, iye samangokamba za dziko limodzi lokha ayi. Mau amene Yesu anagwiritsa ntchito pofotokoza za dziko lapansi ndi mau a Chiheleni amene amatanthauza magulu a wanthu. Yesu amaliona dzikolapansi malinga ndi magulu a anthu.

Ndi kosavuta kuti tizindikire mmene Uthenga wafarikira pa dziko lapansi titati tirione dziko lapansi ngati gulu a anthu. Gulu la anthu likhoza kufotozedwa motere:

“Gulu lalikulu la anthu limene limakhala pa gwirizano waukulu wina ndi mzake. Gulu limeneli limakhala ndi zinthu zowanjanitsa monga chilankhulo, chikhalidwe chofanana, komanso anthuwa amakhala malo amodzi”

Mtundu wa anthu ndi gulu lalikulu limene uthenga ukhoza kufarikira osakumana ndi mavuto akumvetsetsa komanso kuvomereza Uthenga Wabwino. Chifukwa chakuti mtundu wa anthu umodzi umalankhula chilankhulo chimodzi komanso chikhalidwe chao ndi chimodzi, zolempheretsa zimakhala zosavuta kufalita Uthenga Wabwino. Izi zili chomwechi chifukwa chakuti zinthu zimene zimalepheleretsa kufalitsa uthenga makamaka chilankhulo sizimakhalanso vuto ayi.

Pali mitundu yambirimbiri ya anthu pa dziko lapansi imene azindikiridwa. Ina mwa mitundu imene ili ndi anthu ochepa chabe okwana ziukwi zitatatu (3000), pamene mitundu ina ili ndi anthu okwana 30 Miliyoni. Chigawo chilichonse cha dziko lapansi chimakhala ndi maiko komanso mitundu ya anthu yosiyanasiyana. Mwachitsanzo, chigawo cha maiko aku Africa kuli anthu amitundu yosiyanasiyana amenea ali ndi zilankhulo zosiyanasiyanso.

Dziko lina lilironse liri ndi mitundu ya anthu yosinasiyana. Mwachitsanzo, pamene tingazindikire kuti dziko ngati Nigeria liri ndi miyandamiyanda ya mitundu ya anthu izi zimathandiza kuti tizindikire kuti kugawikana ndi kwakulu chifukwa cha mitundu kusiyana ndi kugawikana chifukwa cha maiko.

Chitsanzo cha bwino cha gulu la anthu ndi gulu la anthu aku Somalia amene amapezela ku Kenya. Anthu amenewa ali ndi chikhalidwe chofanana, chilankhulo chofanana ngakhale mbiri yao ndi yofanana. Anthu amenewa samakhala malo amodzimodzi, chipembedzo chao ndi cha Chisilamu ndipo amakhala madera aku mudzi. Iwo ndi gawo lochepa chabe ya mitundu yambiri imene imapezeka ku Kenya.

Pali mau awiri amene ndi odziwika bwino konse.

Anthu amene sanafikiridwe ndi anthu ameme pakati pawo palibe gulu la anthu okhulupirira amena ali ndi kuthekera kofikira anthu awo ndi Uthenga Wabwino.

Anthu ofikiridwa: Ili ndi gulu la anthu limene pakati pawo pamakhala okhulupirira okwanira amene ali ndi kuthekera kofaritsa Uthenga Wabwino pakati anthu awo.

MAGULU A ANTHU OSAFIKIRIDWA:

Pali mitundu yambiri ya anthu imene pakati pawo palibe mpingo umene umakhala ukufaritsa Uthenga Wabwino. Pakati pa anthu amanewa, pali anthu miyandamiyanda amene sanamve uthenga Wabwino. Anthu amene sanafikikiridwe akhoza kuikidwa mu magawo asanu:

ANTHU AMITUNDU YOSIYANASIYANA:

Anthu amitundu yosiyanasiyana ali ndi zikhalidwe komanso zilakhulo zosiyanasiyana. Anthu ambiri amitundu yosiyanasiyana amapembedza zinthu zosiyanasiyana za mizimu zimene si Mulungu weniweni. Ina mwa mizimu imeneyi imakhala ziwanda, milungu yabodza imene imakhala miyala, mitengo kapena zitsulo zosemedwa.

ASILAMU

Asilamu ndi anthu amene amatsatira chipembedzo cha chisilamu komanso chiphunzitso cha Korani. Kwambiri a Silamu amapezeka mmadera awa: Chigawo chapakati chaku Asiya, ku Africa komanso maiko a Aruya. Koma chifukwa chakufarikira kwa chisilamu, pakadali pano a Silamu akupezeka gawo lina lirilonse la dziko lapansi:

A HINDU:

A Hindu ambiri amapezeka ku India, koma amapezekanso gawo linalironse la dziko lapansi. Anthu ambiri ali mu goli la chipembedzo chimenechi kuidzera mu makachitsi, mafano, miyambo ndi zinthu zambiri za chipembedzo zimenezi.

MA CHINISE

Ma Chinise ndi gulu limodzi la anthu lalikulu limene silinafikiridwe ndi uthenga Wabwino. Pali ma chinise ambiri amene afalikira dziko lonse lapansi kuonjzera ma gulu ama machineese amane ali ku China

ANTHU A CHIBUDA:

Gawo lachisanu la anthu amene sanafikiridwe ndi gulu la anthu a Chibuda. Pali kusiyana pakati pa anthu a Chibuda amene amapezeka ku mmawa kwa Asiya. Koma chinthu chimodzi

chodziwikiratu ndi chakuti anthu a Chibuda koma anthu onsewa amapembedza mizimu ndi ziwanda.

ATCHITO ALI KUTI?

Kodi ndi chifukwa chani anthu onsewa sanafikiridwe ndi uthenga Wabwino? Nanga a ntchito ali kuti?

Ogwira ntchito ambiri a Chikristu amafuna atamagwira ntchito mu mipingo ikuluikulu imene imakhala ndi chithandizo chambiri cha chuma. Ena samafuna kusiya mabanja awo kapena kumene amakhala ndi kukagwira ntchito ndi anthu ena azikhalidwe zina amene zinthu zimakhala zovuta. Pamene anthu ena sanazindikire kumene za masomphenya a Baibulo a dziko lonse lapansi.

Miyandamiyanda ya anthu yangoima pakatikati. Ali okonzeka kuti akoloredwe ndi uthenga wabwino. Mulungu akuti:

Ndipo ndinafunafuna munthu pakati pao wakumanganso linga, ndi kuimira dziko popasukira pamaso panga, kuti ndisaliononge; koma ndinapeza palibe. (Ezekieli 22:30)

Pamene mwamvetsa mmene Baibulo limaonera zinthu, mukhoza kuzindikira kuti Mulungu wakuitana kuti mukhale mulumikizitsi wa anthu amene ali ali kudikira Uthenga Wabwino. Awa ndi amitanidwe a anthu onse anthu amene ndi otembenuka mtina owonadi.

MAIKO OTSEKEKA

Chinthu chimodzi chimene chakhala chikulepheretsa kufalitsa Uthenga ndi chakuti Maiko ambiri akuletsa akhristu Kufalitsa Uthenga Wabwino pogwiritsa ntchito njira zodziwikiratu pofaritsa Uthenga Wabwino. Ndipo maiko amenewa alipo 60 pa 100 ena alionse. Pamene dziko ndi lotsekedwa zimatanthauza kuti dzikolo silimalora anthu ofaritsa Uthenga Wabwino alowe mu dzikolo. Nthawi zambiri maiko oterewa amakhazikitsa Malamulo oyendetsa chipembedzo cha anthu ake. Ena mwa maiko amenewa amaletsa kutembenuza anthu kuchipembedzo chao kupita ku Chipembedzo china.

Kodi ndi chifukwa chiani maiko amatseka makomo a Uthenga Wabwino? Izi zili chomwechi chifukwa chakuti Satana amapangitsa atsogoleri kuti apange zinthu izi:

- Potenga mfundo zachikunja zimene sizimavomereza kuti Mulungu alipo. Atsogoleri amaiko ngati amenewa samafuna kuti wina aliyense aphunzitse choonadi cha Mulungu weniweni.
- Amakhazikitsa chipembedzo cha dziko lonse. Atsogoleri a dziko ngati amenewa samafuna kuti anthu atembenuke mtima ndikutsata chikhristu. Iwo amafuna anthu kuti atsate chipembedzo cha dzikolo. Chifukwa cha ichi, iwo amakhazikitsa malamulo oletsa kufalitsa Uthenga Wabwino ngakhale kuletsa anthu ofalitsa uthenga kuti asalowe mu dziko lao.
- Iwo amakhazikitsa mfundo za ndale zimene zimakhala zosiyana ndi maiko ena amene amatumiza anthu ofalitsa Uthenga Wabwino. Satana ndiye amatsogolera mfundo zodzisala komanso zosagwirizana ndi maiko ena ndi cholionga choti Uthenga Wabwino Usafalikire.

MAKOMO OTSEKUKA

Ngakhale kuti maiko 60 mwa maiko 100 ena alionse amatengedwa ngati otsekeka pa nkhani yofaritsa Uthenga Wabwino, koma zoonza zake ndi zakuti palibe khomo limene ndo lotsekeka. Yesu amazindikira kuti padzakhala kulimbana ndi Uthengenga Wabwino. Iye anati pamene adzazuka inu mu mzinda wina pitani mzinda wina (Mateyu10:23)

Kwa okhulupirira, mfundo ya makomo otsekeka imaonetsera kulephera. Koma Yesu anaonetsera kuti pamene khomo linna latsekeka, khomo lina limatseguka. Nthawi zina Mulungu amagwiritsa ntchito makomo otsekeka ndi cholinga choti otitsolere ku minda yabala kwambiri. Izi zinamuchitikira Paulo ndi gulu lake lofarits Uthenga Wabwino:

Ndipo anapita pa dziko la Frugiya ndi Galatiya, atawaletsa Mzimu Woyera kuti asalalikire mau m'Asiya; pamene anafika kundunji kwa Musiya, anayesa kunka ku Bituniya; ndipo Mzimu wa Yesu sanawaloleza; ndipo pamene anapita pambali pa Musiya, anatsikira ku Trowa. (Macitidwe 16:6-8)

Kunali ku Troa kumene Paulo anamva kuti apite Ku Makedoni, limene linali dera lokokonzeka kulandira Uthenga Wabwino. Ndipo patadutsa nthawi, Paulo anaitanidwa kupia ku Asiya. Nthawi zina makomo amatsekedwa chifukwa chakuts kholora zilinache kapena kuti

silinakhwime. Chifukwa cha ichi, tikuyenera kusamaritsa kuti titsate chitogozo cha Mzimu Woyera.

Koma tingachite bwanji ndi maiko amene ndi otseka chifukwa zifukwa za ndale komansi chikhulupiriro choti kulibe Mulungu? Mpinga wakhala ukugonjetsedwa nsanga ndi nyengo zimenezi. Tikuyenera kuzindikira kuti pamene njira zanthawi zonse zofaritsira Uthenga Wabwino zagonjetsedwa, Mulungu amaonetsera njira zina zofaritsira Uthenga Wabwino mu dziko.

Mu maiko amene ndi zovuta kuti munthu akhoza kulowamo ngati ofaritsa Uthenga kapena ngati mtumiki, okhulupirira akhoza kulowa mu dzikolo ngati aphunzitsi, oyendetsa zinthu ndi ogwira ntchito zina. Anthu amanewa akhoza kukhala odzidalira okha pogwira ntchito zina zosakhala zauzimu, koma cholinga chao chenicheni ndi kufalitsa Uthenga Wabwino.

Baibulo limapereka chitsanzo cha Mfundo imeneyi. Paulo amapanga mahema ku maiko amene amapita ndi cholinga choti azithandize yekha. Yosefe ndi Daniele anali anthu wamba amene anali ndi maudindo akulu amene anawagwiritsa ntchito pofuna kuphunzitsa fuko lonse zokhudza Mulungu.

Ngakhale kuti zimaoneka kuti palibe njira ngakhale kuti zimaoneka kuti palibe njira yolowera mu dziko, koma dzikolo sikuti limakhala lotsekeka ku Uthenga Wabwino. Palibe dziko limene ndi lotsekeka ku mphamvu ya Mzimu Woyera kudzera mu pemphero. Pemphero ndi mphamvu ya Mzimu Woyera ikhoza kubooleza dziko lina lirilonse pasatengera kuti malamuro kapena kuti malire awo amaletsa uthenga Wabwino.

KODI ADZAKWANIRITSE NTCHITO IMENEYI NDI NDANI?

Tikaliona dziko lapansi ngati dziko liimene likudikira Uthenga Wabwino, timatha kuchita kakasi ndi kukula kwa ntchito imeneyi:

- Miyandamiyanda ya anthu amene alibe Khristu
- Zilankhulo za nkanikhani zimene zilibe Mau a Mulungu olembedwa.
- Magulu a anthu ambiri opanda anthu otumikira uthenga Wabwino pakati pawo.

Sikhala zothodwetsa pamene tiona miyandamiyanda ya anthu ku Tokyo, San Paulo ndi ku Hongkong. Koma anthu amenewa ndi akuti wina aliyense ayenera kumva Uthenga Wabwino kapena kuti kukhala ndi mwai ochitapo kanthu atamba Uthenga Wabwino.

Pamene tiona chikhamu cha anthu amene sanafikiridwe ndi Uthenga Wabwino, chikhumbokhumbo chathu chiyenera kukhala ngati cha mtumwi Paulo.

Ndipo coteru ndinaciyesa cinthu caulemu kulalikira Uthenga Wabwino, pa malopo Kristu asanachulldwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko a munthu wina. Koma monga kwalembedwa, Iwo amene uthenga wace sunawafikire, adzaona, Ndipo iwo amene sanamve, adzadziwitsa. (Aroma 15:20-21)

Tikhoza kukwaniritsa ntchito imeneyi ngati okhulupirira wina aliyense akhoza kukhala okhulupiriria wa dziko lapansi. Muphunzira zambiri zokhudza izi mu chaputala chikubwerachi.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Fotokozani mwachidule mmene uthenga Wabwino ukufalikira malingana ndi chilankhuro chiwerengero, komanso madera a dziko lapansi.

3. Fotokozani tanthauzo la mtundu wa anthu.

4. Fotokozera tanthauzo la anthu osafikiridwa?

5. Fotokozani tanthauzo la anthu ofikiridwa

6. Tchulani magulu asanu a anthu amene sanafikiridwe ndi Uthenga wabwino

7. Kodi mau oti dziko lotsekeka amatanthauza chiani?

8. Kodi ndi zoona kapena za bodza? Choonadi chake ndi chakuti palibe dziko lotsekeka

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku limeneri)

ZOONJEZERA POPHUNZITSA

1. Kuti midziwe zambiri zokhudza mmene uthenga Ukufalikira pa dziko lapansi, werengani Buku lotchedwa the world Christian Encyclopedia limene linalembedwa ndi David B. Barret.
2. Komanso onani tsamba la pa Internet lotchedwa US Center for Mission. Bugwe limeneli imatolera uthenga okhudza maiko amamene sanafikiridwe ndipo uthengawu umagawidwa kwa anthu amene ali ndi chidwi choti afikire anthu amene sanafikiridwe.
3. Ngati muli ndi chidwi choti mudziwe zambiri zokhudza anthu amene sanafikiridwe, (lemberani bungwe limeneri ndipo address yawo ndi Iyi: 160 Elizabeth St., Pasadena, California 91104, USA. Kapena mukhoza kolowa pa tsamba la internet la bungweli
4. Onaninso buku lotchedwa operations world limene limakhala ndi zinthu zofuna kupephelera zokhudza maiko osiyanasiyana.

CHAPUTALA 8

KUKHALA KHRISTU WA DZIKO LONSE

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziro ili muyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza tanthauzo la Khristu wa dziko lonse.
- Kukhala Khristu wa dziko lonse.
- Kufotokozero ndondomeko zimene mpingo oyamaba umagwiritsa ntchito pofuna kufaritsa Uthenga Wabwino.

VESI YOTSOGOLERA

Inu simunandisankha Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala cipatso, ndi kuti cipatso canu cikhale; kuti cimene ciri conse mukapempha Atate m'dzina langa akakupatseni inu. (Yohane 15:16)

Mu chaputala chapitachi, taona udindo umene mpingo uli nao pofikira dziko lonse lapansi ndi Uthenga Wabwino wa Yesu. Okhulupirira wina aliyense payekha payenkha ndi chiwalo cha thupi la Khristu Yesu limene ndi mpingo. Ngati mpingo ukukwaniritsa udindo wake pa dziko lapansi, ndiye kuti nanunso mukuyenera kuzindikira mbali yanu mu chikonzero cha Mulungu. Wina aliyense ali ndi udindo ku dziko lapansi. Koma udindo umene ndi waukulu kotere umaposa kungopereka ndalama kwa atumiki ofarita Uthenga Wabwino.

Chaputala ichi chikhazikika pa za udindo umene wina aliyense ali nawo pa dziko lapansi. Muphunzira mmene mungakhalire nkhristu wa dziko lapansi. Izi zikuthandizani kuchoka pakukhala munthu ongowonenera ndi kuyamba kuchitapo kanthu pa chikonzero cha Mulungu cha dziko lapansi.

MUNTHU WINA ALIYENSE NDI MLALIKI

Pamene Yesu anati mukani ku dziko lapansi ndi kulalikira Uthenga Wabwino ndipo inu mudzakhala mboni zanga. Apa Yesu amalankhula ku gulu la ophunzira ake. Koma monga mmene zimakhala ndi gulu linalirilonse, mguluro limapangidwa ndi anthu. Chifukwa cha ichi, pamene Yesu amanena kiuti mukani iye amanena izi kwa anthu munthu wina aliyense sikuti izi amakamba kwa gulu lokha ayi. Munthu wina aliyense amene ndi mbali imodzi ya gulu ali ndi udindo pa iye yekha. Ngati anthu pagulu angalephera ndiye kuti gulu lonse limakhala kuti lalephera.

Udindo omuka kupita ku dziko lapansi uli mmanja mwa mpingo. Koma mpingo umapangidwa ndi anthu kotere kuti ngati mpingo ungakwanitse kukwaniritsa Kutumidwa kwakukulu zitengera kudzipereka kwa munthu wina aliyense payekhapayenkha.

WINA ALIYENSE APHUNZITSE MUNTHU MMODZI

Malingana ndi mpingo oyamba, munthu wina aliyense amatenga udindo ofaritsa Uthenga Wabwino. Kufaritsa Uthenga Wabwino kwa anthu achikhalidwe kumachitiuka ndi anthu wamba amene sanali abusa kapena atsogoleri achipembedzo. Chifukwa cha ichi, anthu ena amene anafaritsa Uthenga Wabwino anali anthu wamba. Chaputala 6 ndi 7 cha Machitidwe ndi chitsanzo cha bwino cha anthu wamba akulalikira Uthenga Wabwino. Filipo ndi Stefano anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kufaritsa Uthenga mwamphamvu.

Pamene chizuzo chinabwera, mpingo waku Yerusalemu unabalalikirira ku Yudeya ndi ku Samariya. Baibulo limafotokoza kuti:

**Pamenepo ndipo iwo akubalalitsidwa anapitapita nalalikira mauwo.
(Macitidwe 8:4)**

Okhulupirira wina aliyense anatenga gawo pakuphunzitsa amayi ndi obambo okhulupirira amene naonso anaphunzitsa anthu ena okhulupirira:

And the things that thou hast heard of me among many witnesses, the same

Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo)

Kubala kwauzimu kopitilira kunabweretsanso kuchuluka kwa okhulupirira mopitiliranso.

KHOMO LINA LILONSE NDI GAWO LAKUBALA

Mfundo yonena kuti khomo linalironse ndi gawo limodzi lakubala si lachilendo. Kuchokera nthawi imene munthu anapatsidwa chilamuliro, Mulungu anakhazikitsa khomo ngati malo amene akhoza kukhala ophunzilira.

Ndipo mau awa ndikuuzanilero, azikhala pantima panu; ndipo muziwaphunzitsa mwacangu kwa ana anu, ndi kuwalankhula awa pokhala pansu m'nyumba zanu, ndi poyenda inu panjira, ndi pogona inu pansu, ndi pouka inu. Ndipo muziwalemba pa mphuthu za nyumba zanu, ndi pa zipata zanu. (Deuteronomo 6:6-7,9)

Malinga ndi mpingo oyamba, khomo lina lilironse lina malo ofalitsira uthenga wabwino. Okhulupirira samangophunzitsa Uthenga Wabwino mu kachisi, komanso pakhomo panali malo ophunzilira:

Ndipo masiku onse, m'Kacisi ndi m'nyumba, 2 sanaleka kuphunzitsa ndi kulalikira Kristu Yesu. (Macitidwe 5:42)

Kufaritsa Uthenga Wabwino kunali ndi maziko akulu kuchokera pa khomo ndi chifukwa cha ichi, pamene Paulo amalimbana ndi mpingo, iye amazindikira kuti ameyeneranso kulimbana ndi mipingo yammakomo osati kungolimbana ndi kachisi yekha. Iye amayenda khomo ndi khomo pofuna kuletsa kufarikira kwa Uthenga Wabwino:

Ndipo Saulo anapasula Mpingo, nalowa m'nyumba m'nyumba, nakokamo amuna ndi akazi, nawaika m'ndende. Macitidwe 8:3)

Masophenya a Mulungu oti uthenga ufarikire kwa anthu amitundu yonse anaperekedwa ku nyumba pamene Petro anali kupemphera pamwamba pa nyumba. (Machitidwe 10) Uthenga oyamba opita kwa anthu amitundu unalarikidwa kwa Koneriyo (Machitidwe 10)

Mlakiri wamkulu kwa anthu amitundu amene ndi Paulo anali ophunzira kapena otsatita wa Ananiya. Iye anaphunzitsidwa ku nyumba ya Ananiya (Machitidwe 9). Paulo anali kuphunzitsa khomo ndi khomo mu nthawi yautimiki wake komanso anatomikiranso ku gulu la anthu:

kuti sindinakubisirani zinthu zopindulira, osazilalikira kwa inu, ndi kukuphunzitsani inu pabwalo ndi m'nyumba m'nyumba, (Machitidwe 20:20)

Kumapeto kwa utumiki wake, Paulo amatumikira pa nyumba pamene anthu amabwera kudzamva uthenga kwa iye komanso ndi cholinga choti aphunzitsidwe:

Kuti sindinakubisirani zinthu zopindulira, osazilalikira kwa inu, ndi kukuphunzitsani inu pabwalo ndi m'nyumba m'nyumba, (Macitidwe 20:20)

Yesu anati nyumba yake imayenera kutchedwa nyumba ya mapemphero ya mafuko onse a dziko lapansi:

Ndipo pamene Yesu anamva ici, ananena nao, Akulimba safuna sing'anga, koma odwala ndiwo; sindinadza kudzaitana olungama, koma ocimwa. (Marko 2:17)

Mau akuti nyumba mu chiheleni amanthauza kuti malo okhalapo. Ndipo malowa akhoza kukhala nyumba yanu kapena ku kachisi.

Ndondomeko imene mpingo oyamba umagwiritsa ntchito pofuna kufaritsa Uthenga Wabwino inali yakuti okhulupirira wina aliyense amabara okhulupirira ena komanso khomo lina lilironse limakhala malo ofaritsira Uthenga Wabwino.

ZOTSATIRA

Kodi zotsatira za khomo kukhala malo ofaritsira Uthenga wabwino komanso munthu wina aliyense kutengapo gawo zinali zotani? Izi zinapangitsa kuti afikire dziko lonse lapansi ndi uthenga Wabwino. Ngakhale adani a mpingo amene analengeza nati:

Kodi zotsatira zikhoza kukhala zotani atati okhulupirira wina aliyense atsste ndondomeko imeneyi?

Werengani tchatu imene yalembedwa pansipayi. Malingana ndi tchatu imeneyi, ikuonetsera nthawi imene zimatenge kuti munthu athe kutembenuka mtima ndikuphunzitsidwa komanso kuti naye anayambe kuphunzitsa anthu ena kapena kubala zipatso. Zinthu zimenezi, zikhoza kuchitika kwa chaka chimodzi. Koma nthawi yeniyeni imene izi zimatengera anthu amene akufaritsa uthengawo. Koma ngati dziko munthu wina aliyense angapange ophunzira mmodzi pachaka

amene nayenso adzakwanitsa kupanga ophunzira wina. Izi zikho zikhoza kupangitsa kuti Uthenga ufukire dziko lonse lapansi lifikiridwe ndi Uthenga Wabwino.

Malingana ndi tchati ili munsiyi, munthu wina aliyense mu chaka chimodzo ayenera kupanga ophunzira mmodzi amene nayenso mu chaka chinacho adzapange ophunzira wina. Izi zikuthauza kuti pamapeto pa chaka ndekuti pali anthu awiri amene ndi okhulupirira. Oyamba ndi munthu amene wapanga ophunzira uka ndipo wachiwiri ndi amene waphunzitsidwa. Mu chaka chachiwiri ndiyi kuti anthu awiri amenewa naonso aphunzitsa anthu awiri zimene zikutanthauza kuti apamapeto pake pakhala anthu anayi amene ndi okhulupirira. Gawo lalikulu la dziko lapansi silinafikiridwe ndi Uthenga Wabwino. Koma Mulungu wapereka njira zimene ngati zingagwiritsidwe ntchito ndi okhulupirira wina aliyense ndiye kuti kufaritsa Uthenga Wabwino kukhoza kukwaniritsidwa kukwaniritsidwa mosavuta.

	Opanga ophunzira)	Opanga ophunzira	onse pamodzi	
Chaka 17	65,536	65,536	=	131,072
Chaka 16	32,768	32,768	=	65,536
Chaka 15	16,384	16,384	=	32,768
Chaka 14	8,192	8,192	=	16,384
Chaka 13	4,096	4,096	=	8,192
Chaka12	2,048	2,048	=	4,096
Chaka 11	1,024	1,024	=	2,048
Chaka10	512	512	=	1,024
Chaka 9	256	256	=	512
Chaka 8	128	128	=	256
Chaka 7	64	64	=	128
Chaka 6	32	32	=	64
Chaka 5	16	16	=	32

Chaka 4	8	8	=	16
Chaka3	4	4	=	8
Chaka 2	2	2	=	4
Chaka 1	1	1	=	2

NDONDOMEKO YA MULUNGU YA KACHULUKITISIDWE KA OPHUNZIRA AKHRISTU A DZIKO LONSE

Okhulupirira a dziko lapansi ndi ka gulu ka anthu kamena kakukula pa dziko lapansi. Gulu limeneli simpingo kapena bungwe ayi. Ili ndi gulu la anthu okhulupirira amene azindikira za uundo wao ofaritsa Uthenga Wabwino ku dziko lonse lapansi.

Anthu amenewa amachokera ku mitundu ya anthu yosiyanasiyana, zikhalidwe, zipembedzo komanso ndi ku mipingo yosiyana siyana. Koma chinthu chimodzi chimene chimawanjanitsa ndi kukhala okhulupirira wa dziko lonse. Khristu wa dziko lonse ndi:

- Amene amazindikira Mulungu amene waonetseredwa mu Baibulo ngati Mulungu yekhaya olondora kapena weniweni.
- Kuzindikira Baibulo ngati Mau a Mulungu olembedwa.
- Anavomereza chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso kudzera mwa Khristu Yesu.
- Maonede awo a zinthu ndi ogwirizana ndi Baibulo.
- Mwa iwo okha anavomereza kufunika kofaritsa Uthenga Wabwino ku dziko lonse lapansi.

Izi sizikutanthauza kuti kristu wa dziko lonse amachoka dziko lawo ndi kupita ku dziko lina kapena kukakhala pakati apa anthu a chikhalidwe china ngakhale kuti amakhala okozenzeka kutero ngati Mulungu ngawauze. Kukhala kristu wa dziko lonse kumatantauza kuti munthu ndi okonzeka kufaritsa Uthenga Wabwino kumalo kumene ali, kaya ndi kumudzi kapena ma matauni, iwo amakhala okonzeka. Iwo amakhalanso okonzeka kutumiza anthu ena kumadera kumene uthenga wabwino sunafike. Chinthu chimene chimakhala chofunika kwambiri kwa nkristu wa dziko lonse lapansi ndi kufaritsa Uthenga Wabwino.

KUDZIPEREKA KWA NKHRISTU WA DZIKO LONSE

Anthu amene adzipereka kukhala nkristu wa dziko lapansi amakhala adzipereka kwa Mulungu. Iwo amakhala kutu achita malonjezano awa:

“Mwachisomo cha Mulungu ndi ulemelero wake, ndikupereka moyo wanga kuti ndimvere kutimidwa kwakukulu pa Mateyu 28:18-20. Kwina kulikonse komanso ndi mwina mulimonse mmene Mulungu anganditsogolere ndidzadzzipereka kwa anthu amene sanafikiridwe (Aroma 15:20-21). Ndidzayesetsa kugawana masomphenya amenewa ndi anthu ena.”

KUKULA NGATI NKHRISTU WA DZIKO LONSE

Mu gawo la zoonjezera pophonzira la chaputala ichi, pali zolembedwa zina zapadera zimene zalembedwa kuti mukhoza kuwerenga ndi cholinga choti mukuze chidziwitso chanu cha nkristu wa dziko lonse lapansi. Zina mwa zinthu zina zimene mukhoza kuchita kuti mukhale gawo limodzi lokwaniritsa chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi ndi izi:

KONZEKERANI KUITANA KWA MULUNGU

1. Mudzipereke nokha ngati nsembe ya moyo kwa Ambuye (Aroma 12:1-2)
2. Onenetsetsani kuti palibe tchimo pakati panu limene likhoza kulepheretsa kuti musapenye kapene kumva zinthu mu dziko lauzimu (Aefeso 1:18; Akolose 1:9)
3. Muyenera kuchotsa maganizo anu onse amene munali nawo kale (Salimo 25:9)
4. Khazikitsani chikhalidwe chiwerenga Baibulo ndi kupemphera tsiku ndi tsiku (Yoswa 1:8, Salimo 77:12; 119:15,25,45)
5. Dikirani kwa Mulungu ndipo muyembekezera iye kuti akutsogozeni pa chinachilichonse chimene mumachita tsiku ndi tsiku. Iye adzakutsikimizirani za chifuniro chake ndi maitanidwe ake (Miyambo 3:6, Salimo 23:3; 32:8; 37:5, 7).

Zindindikirani kuti palibe nthawi imene imataika pamene munthu akudikira Mulungu kuti avumbulutse chikonzero chake pa moyo wanu. Yose anadikira mundende kwa dzaka ziwiri, koma pamapeto pake iye anapulumutsa fuko lake. Mose anadikira kwa dzaka makumi anayi mu chipululu, koma iye anatsogolera anthu ake kuchoka ku ukapolo ndi kuwapatsa Ufulu.

6. Pezani Buku phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa “Kuzindikira Kulankhula kwa Mulungu” pamene mukukonzekera kulandira maitanidwe anu kwa Mulungu kapena kuti kuvomera kuitanidwa kwanu.

YAMBANI KUMENE MULI

1. Mukuyenera kumvera Mulungu mu zinthu zazing’ono zimene mupanga tsiku ndi tsiku (Luka 19:17, I samueli 15:22) ngati simungakhulupirike ndi zinthu zazing’ono zome Mulungu wakupatsani kuti muchite kumene muli, sangakukhulupilireni ndi zinthu zazikulu pa UtumikiI (Mateyu 25:14-30). Yang’anani mudzi wani ndi maso auzimu. Ndipo pemphani Mulungu akupatseni akuonetsereni anthu amene akufinika Uthenga Wabwino. Phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa “kuunguza nyengo” Environmental Analysis ikuthandizani kuti mukwanitse kufikira anthu amene akufinika Uthenga Wabwino. Pali maphunziro enanso a Harvestime International ngati awa: ndindomeko zakuchulukitsa, ndi kufalitsa uthenga Wabwino akuthandizani kuti mukhale gawo limodzi la chikonzero cha Mulungu kumene inuyo muli.
2. Mukhale okonzeka kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu pena paliponse (Yohane 7:17) izi zikhoza kutanthauza kuchoka dera lanu ndikukhala pakati pa anthu a chikhalidwe china ndi cholinga chofalitsa uthenga Wabwino. Kapena izi zikhoza kutathauza kupiza mu mzinda wanu ndi cholinga chofalitsa Uthenga Wabwino.
3. Pitirizani kuphunzira zinthu zokhudza zosowa za dziko lapansi ndi cholinga choti mukuze masomphenya anu a dziko lapansi (Yohane 4:35) werengani ma buku okhudza muti umeneu ndipo pangani maulendo osatenga nthawi ndi cholinga choti muone mmene zinthu zimakhallira pokhala ndi anthu achikhalidwe china.
4. Pezani nthawi yopemphelera maiko a dziko ndi anthu onse amene akugwira ntchito yofaritsa Uthenga Wabwino. (Mateyu 9:37-38). Chaputala 10 cha phunziro ili chikupereka dongosolo la mmene mungachitire zinthu izi.
5. Yambani kugwiritsa ntchito mphatso zanu zauzimu “Utumiki wa Mzimu Woyera” wa Harvestime International institute ukuthandandizani kuti muzindikire mphatso yanu.

6. Lowani gulu la evangelism mu mpingo wanu ndipo palibe komiti kapena gulu la evangelism pa mpingo wanu, yambitsani gulu limeneli. Chaputala 10 cha phunziro limeli chikuthandizani kuti mukwaniritse zinthu zimenezi:
7. Lumikizanani ndi anthu amene akufaritsa Uthenga Wabwino maiko ena. lembarani atumiki a Uthenga Wabwino kapena kuti ma mishonare ndipo mukhoza kuwapempha kuti akhale mu dera lanu. Muyenera kuphunzira kuchokera mu zimene adutsamo. Mukhoza kupindura kwambira kuchokera pa ubale umeneu pamene akhale akugawana nanu nkhwana zawo, zosowa zawo komanso chigonjetso chawo.
8. Funani maphunziro apadera ndi cholinga choti mudzikonzekeretse nokha kuti mukafikire dziko lonse lapansi. Mukhaza kuyamba ndi kuwerenga maphuziro a Harvestime International Institute.
9. Gawanani ndi anthu ena zinthu zimene mwaphunzira. Lowani gulu la okhulupirira a dziko lonse ndi cholinga choti muphunzire zambiri zokhudza dziko lapansi komanso zinthu zimene inuyo mungachite kudzera kuzimene mwaphunzira. Chaputala 10 cha phunziro ili chikuthandizani kuti mukwanitise zinthu zimenezi.
10. Yambanipo kupereka ndalama zanu ndi cholinga chofaritsa uthenga Wabwino. Unikirani moyo wanu ndi cholinga choti mukhoza kusiya zinthu zina kuti ndi cholinga choti mupulumutse ndalama zina zimene zingathe kugwira ntchito yofaritsa Uthenga Wabwino.
11. Pezani chitupa chanu cha Passport mkutheka kuti Mulungu akufuna kukutumiza ku dziko lina.

ZINDIKIRANI KUITANA KWA MULUNGU:

Okhulupirira wina aliyense ali ndi Udindo ofaritsa Uthenga Wabwino ku malo kumene iye amakhala. Koma ena amalandira maitanidwe kuti akathe kutimikira Mulungu ngati ntchito ya nthawi zonse pamene amakhala akutumikira ngati abusa, alariki, ma Mishonare ndi ku ma utumiki ena. Pali mfundo zimene mukhoza kugwiritsa ntchito kuti muzindikire maitanidwe amene Mulungu akupatsana komanso dera limene Iye akufuna kuti mupite:

Mukuyenera kudzifunsa mafunso awa:

1. Kodi zimene mumakhumba zimagwirizana ndi chikonzero chimene Mulungu waika mmau ake. Kodi khumbo lanu ndi logwirizana ndi Baibulo ndipo kodi ganizo lanuro likuthandizira kufaritsa Uthenga Wabwino dziko lonse lapansi.
2. Kodi nyengo zimene mukudutsamo zikuonetsa kuti Mulungu I akukutsogolerani. Simukuyenera kungotsogozedwa ndi nyengo zokha ayi, koma mukuyenera kuunikira nyengo zanu malingana ndi maitanidwe amene Mulungu anakupatsani:
3. Kodi Mzimu Woyera amachitira Umboni ndi Mzimu wanu kuti ndi chifuniro cha Mulungu kusowa mtendere mkati mwa mzimu wanu ndi chizindikiro chakuti?
4. Kodi mumakhala kuti mwaitanidwabe pamene palibe china chilichonse choti muchite chokhudza maitanidwe anu chimene chikuoneka kuti ndi chachikulu? Kodi ngati mutanidwa kuti muchite ntchito imene ikuoneka yaing'ono, mukhoza kupitabe?
5. Kodi mwakonzeka kupereka dipo chifukwa cha maitanidwe anu? Dipu lake likhoza kutenga nthawi kuti muonjezere maphunziro anu kapena kufa kumene chifukwa cha chikhupiriro chanu. Likhoza kukhalanso kusiyana ndi abale anu, banja lanu komanso anasi. Kodi mwakonzeka kuchita zinthu zimenezi?

MULUNGU WAKUDZODZANI INU

Mulungu wakusankhani inu kuti mukhale gawo limodzi la chikonzero chake chofuna kufikira maiko onse a dziko lapansi. Iye wakudzodzani inu kuti mukabale chipatso chauzimu mu mmunda wakholora. Iye walonjeza kuti adzapereka zosowa zanthu zonse ndi cholinga choti mukwaniritse ntchito yanu:

Inu simunandisankha Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala cipatso, ndi kuti cipatso canu cikhale; kuti cimene ciri conse mukapempha Atate m'dzina langa akakupatseni inu. (Yohane 15:16)

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera

2. Kodi nkhiristu wa dziko lonse ndi ndani?

3. Fotozereni mwachidule ndondomeko zimen mpingo oyamba umagwiritsa ntchito ndi cholinga chofun kufikira dziko lonse lapansi ndi Uthenga Wabwino.

4. Mayeso akulu mu chaputala ichi ndi akuti mukhale nkhiristu wa dziko lonse. Werengani kudzipereka kumene kwalembedwa munsimu. Ngati mwamvetsa lonjezano limeneli ndipo mwakonzeka kukwaniritsa zimenezi mndi mphamvu zanu zonse, sainani pa mpata umene waperekedwa munsiu.

“Mwachisomo cha Mulungu ndi ulemelero wake, ndikupereka moyo wanga kuti ndimvere kutimidwa kwakukulu pa Mateyu 28:18-20. Kwina kulikonse komanso ndi mwina mulimonse mmene Mulungu anganditsogolere ndidzadzzipereka kwa anthu amene sanafikiridwe (Aroma 15:20-21). Ndidzayesetsa kugawana masomphenya amenewa ndi anthu ena.”

Kusaina _____ **Tsiku** _____

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Sankhani chinthu chimodzi chimene muokhoza kuthandizira.

Khristu oyamba wa dziko lonse anali Abrahamu, amene nkhani yake ikupezeka pa Genesis 11: -25. Abrahamu anali munthu oyamba amene Mulungu anamphatsa lonjezano lofuna kufikira dziko lonse lapansi. Iye anali munthu wamba amene amayenda ndi ng'ombe zake kwinaku akukwaniritsa cholinga cha Mulungu. Abrahamu anali ndi makhalidwe auzimu amene anamulora Iye kuti akwanitse kuitanidwa kwake ku maiko a dziko lapansi. Iye ngati okhulupirira a dziko lonse tikuyenera kutenga mfundo za Abrahamu mmoyo wanthu.

Abrahamu anazindikira maitanidwe ake: iye amazindikiranso udindo wake kumafuko a dziko lapansi. (Genesis 22: 18). Iye ngati mbumba ya Abrahamu, tili ndi udindo umene Iye anali nawo (Agalatiya 3:10)

- Iye anali otsikimizika pa cholinga chimene anali nacho: Romans 4:21
- Iye anali oyendayenda chifukwa cha Mulungu. Iye amakhala moyo osalira zambiri ndipo izi zimamulora kuti athe kuyenda chifukwa cha Mulungu. Iye amatha kusamuka mwachangu Mulungu akamulamura (Genesis 12).
- Iye samayang'ananso mbuyo ayi. Samasilira moyo wake wakale koma anali kuyembekezera zinthu zatsopano zimene Mulungu angamuchitire (Ahebri 11:6)
- Iye amagwira ntchito malinga ndi vumbulutso la Mulungu: Genesis 18:17.
- Iye sanayang'anire kuthekera kwakuthupi kumene anali nako: lonjezano ka fuko linaperekedwa kwa munthu amene tikhoza kuti anali wakufa (Ahebri 11:12).
- Abrahamu amatenga udindo wa anthu ena. Werengani nkhani ya Abrahamu ndi Loti pa Genesis 14.
- Iye anali munthu opereka: amapereka za khumi zake pa zinthu zonse zimene anali nazo (Genesis 14: 20).

- Iye anali omvera: Abrahamu anamvera malamuro a Mulungu ngakhale kuti zotsatira zake samazidziwa (Ahebri 11:8: Genesis 22:18)
- Iye anali okonzeka kukhala mdziko lachilendo: Ahebri 11:9.
- Iye anali lolera kulemekeza chikhalidwe cha anthu ena. Anawerama pamaso pa anthu ena chifukwa chinari chikhalidwe chawo (Genesis 23:12)
- Zinthu zimene amaziona kukhala zofunika zinali zakumwamba osati zakuthipi: Machitidwe 7:5
- Iye anali okonzeka kuima payekha: Yesaya 51: 2
- Anali munthu wa masompheny auzimu: Ahebri 11:10.
- Anali bwenzi la Mulungu (Yakob 2:23)
- Anali munthu wachiyembekezo: Aroma 4:18
- Anali ndi chikhulupiriro chachikulu Aroma 4: 20.
- Anali munthu wangwiro: Aroma 4: 22
- Anali munthu odzichepetsa: Aroma 4:20.
- Anali munthu okonda mtendere: Genesis 13.
- Abrahamu anali wamachawi pochita chifuniro cha Mulungu. ngakhala kuti chifuniro cha Mulungu chinali chovuta, iye amachitsa mwa machawi (Genesis 22)
- Amapereka ulemelero kwa Mulungu: Genesis 14:21-24.
- Iye anabala anthu odzipereka ngai iyeyo: iz zimaonekera mmoyo wa kapolo wake (Genesis 24)
- Anali odalitsika mu zonse: Genesis 24:1

CHAPUTALA 9

OPEMBEDZERA DZIKO LONSE

ZOLINGA

Pamapeto pa chaputala ichi muyenera kukwanitsa zinthu izi;

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokoza tanthauza la opembedzera wa dziko lonse.
- Kuzindikira kufunika kopembedzera dziko lonse.
- Kutsata dongosolo lakupembedzera maiko onse.
- Kukhala opembedzera wa dziko lonse.
- Kukhazikitsa dongosolo la kupembedzera dziko lonse.
- Kuphunzitsa ena kuti akhale opembedzera dziko lonse.

VESI YOTSOGOLERA:

.. Pakuti nyumba yanga idzachedwa nyumba yopemphereramo anthu onse. (Yesaya 56:7)

(Isaiah 56:7)

CHIYAMBI

Mu chaputala changopitachi, munapatsidwa ndondomeko zimene zikhoza kuti mutenga gawo pa chikonzero cha Mulungu cha dziko lonse lapansi. Njira imodzi imene mukhoza kukhala gawo la cholinga cha Mulungu chofuna kufikira dziko lonse ndi kudzera mumapephero. Koma chaputala ichi chiphunzitsa mmene mungachitire zinthu zimenezi. Muphunzira mmene mungakhalire opembedzera wa dziko lonse.

OPEMBEDZERA WA MULUNGU

Mulungu anapereka udindo opembedzera dziko lonse lapansi kwa okhulupirira onse. Pamene tikupembedzera timakhala tikufunafuna Mulungu mmalo mwa anthu ena. Timapereka nkhwawa kwa Mulungu mmalo mwa mafuko a dziko lapansi.

Mau oti dziko lonse amanthauza kuti mayiko onse. Ngati opembedzera wa dziko lonse lapansi, simungangopemphelera zinthu zanu zokha ayi. Pamene mukupephera, mukhala kuti mukuyenda muuzimu pakati pa maiko.

PHINDU LA KUPEMBEDZERA KWA DZIKO LONSE LAPANSI.

Ndondomeko yabwino komanso yoofunika pofikira dziko lonse lapansi ndi kupembedzera. Pali kufunika kutatu kwa utumiki umenewu:

KUPEMBEDZERA KUMAGWIRIZANA NDI BAIBULO

Mu chipangano Chakale chili ndi zitsanzo zambiri zimene zimaonetsera kusintha kwa zinthu chifukwa chakuti anthu anapembedzera. Kupembedzera kumene kumene Nehemiya anachita ndi chitsanzo chabwino. Pali ndime zambiri mu m'Baibulo zimene zimene zikufotokozeraz za kufunika kwa kupembedzera.

Pomwepo ananena kwa ophunzira ace, Zotuta zicurukadi koma anchito ali owerengeka. Cifukwa cace pempherani Mwini zotuta kuti akokose anchito kukututakwace. (Mateyu 9:37-38)

. . pakuti nyumba yanga idzachedwa nyumba yopemphereramo anthu onse. (Yesaya 56:7)

PEMPHERO NDI CHINTHU CHIMENE ANTHU ONSE AMADALIRA

Pemphero ndiye gwero lalikulu la mphamvu kwa munthu. Pemphero limabweretsa chitsitsimutso ndipo chitsitsimutso chimabweretsa njala yolalika uthenga Wabwino. Zotsatira zakulalika ndi kufalikira kwa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu. Madongosolo ofuna kularika ndi ofunika, koma chofunika kwambirinsu koma pemphero ndi gawo lofunika kwambiri. Pemphero ndi maziko amene amathandiza kuti utumiki upitilire.

KUPEMBEDZERA DZIKO LOPANSI KULIBE MALIRE

Palibe maiko otsekeka amene pemphero silingadutse, kapena malire amene silingadutse. Pemphero limafika kumapeto kwa dziko lapansi. Mwina singathe kuchoka mudera lanu, koma kudzera pemphera mukhoza mukhoza kuyenda dziko lonse lapansi mwauzimu. Pemphero limathandiza kuti kuti mukwaniritse zinthu opanda malire. Mtunda, chilankhulo kapena kupeza kwathu sichinthu chotchinga ku pemphero.

Pemphero ndi njira yopezekeratu kwa okhulupirira onse imene imapereka mwai kuti wina aliyense atengepo gawo pakufaritsa Uthenga Wabwino. Palibe munthu amene ndi wachichepere kwambiri kapena wamkulu kwambiri kuti sangachite utumiki. Palibe munthu amene anganene kuti ndi odalikwa kwambira kapena kuti ndi olumara kwambiri. Kupembedzera ndi kutenga mbali pa cholinga cha Mulungu pa dziko lapansi.

DONGOSOLO LA PEMPHERO

Dongosolo la kapempheleredwe likhoza kugwiritsidwa ntchito pa mapemphero a inu nokha ngati munthu kapena pagulu pamene. Dongosolo limathandiza kuti mupephere mwachindunji. Dongosolo limene ndi kupembedzera kwa ola limodzi. Koma musadzipatse nokha malire pa a nthawi yopemphera, ngati Mulungu akuuzanikuti mupemphera kwa nthawi yaitali mukuyera kutere. Kumbukirani kupemphera mu dzina la Yesu Khristu nthawi zonse ngati mmene iye anaphunzitsira. Mapemphero anu ayenera kukhala okhudza zimene Yesu amafuna:

MUSANAYAMBE, PEZERANITU ZINTHU ZOFUNA KUPEMBEDZERA:

Pezani zinthu zimene muyenera kupembedzera. Muyenera kuonetsetsa kuti zinthu zimene mukupemphelera zikhale zogwirizana ndi chikonzero cha Mulungu. Kupemphelera dziko lonse sikungopemphelera zina zilizonse zimene zapephedwa. Uku ndi kupembedzera kumene kumalunjika ku maiko a dziko lapansi.

KUPEMBEDZA MULUNGU (mpindi 10)

Timapezeka pamaso pa Mulungu kudzera mayamiko ndi matamando:

Lowani ku zipata zace ndi ciyamiko, Ndi ku mabwalo ace ndi cilemekezo:

Myamikeni; lilemekezeni dzina lace. (Masalmo 100:4)

Kupembedza kumabweretsani inu pamaso pa Mulungu ndipmo Mulungu amamva zopempha zanu. Muyenera kupembedza Mulungu chifukwa cha chimene iye ali komanso pa zimene iye wachita. Mu zopembedzera zanu mukueyenera kuzindikira chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi komanso muyenera kuthokoza Mulungu chifukwa cha mbali yanu mu chikonzero cha Mulungu. Wolembe Salimlo, Davide akufotokoza kuti tibwere pamaso pa Mulungu ndi maimbidwe. Mukhoza kuchita izi pakuyimba nyimbo za m’buku zimene zikugwirizana ndi cholinga cha Mulungu.

KUPEMBEDZERA DZIKO LONSE LAPANSI (mpindi 10)

MWA ZINTHU ZINA ZIMENE MUKHOZA KUPEMPHELERA NDI IZI:

- Njala yatsopano yauzimu pa dziko lonse lapansi.
- Mulungu adzutse gulu lamphamvu la opembedzera a dziko lonse.
- Kukula ndi ndikufarikira kwa mpingo dziko lonse lapansi.
- Mulungu adzutse atchitmo akholora- azibusa, aneneri, alariki, atumwi, aphunzitsi, ndi atsogoleri ena wamba amene akhoza kukwaniritsa kutumidwa kwakukulu (Mateyu 9:38: Luke 10:2).
- Umodzi pakati pa mipingo imene ilipo kale ndi pakati pa onse amene akutumikira.
- Chitsitsimutso ndi kukakamizika kulanditsa miyoyo ya anthu osapulumsidwa.
- Kugwiritsa ntchito kwa ndalama ndi zinthu zina zakuthupi zothandiza kufaritsa Uthenga Wabwino. Mukuyenera kupempha Mulungu kuti abweretse ndalama komanso adzutse anthu amene akhoza kuthandiza ntchito yofaritsa Uthenga Wabwino ndi ndalama zawo.
- Makomo otsekeka kuti atseguke ku Uthenga Wabwino (II Atesalonika 3:1)
- Mkamwa motseguka ndi cholinga choti tifaritse Uthenga Wabwino.
- Anthu omva uthenga akalandire Uthenga ndi mtima onse (Aroma: 15:30 31).
- Nkhani zikuluzikulu zimene zikhudza kufaritsa Uthenga Wabwino pa dziko lapansi.

- Atsogoleri andale ndi ma boma kuti mitima yao ikhale yotseguka ku ntchito yofaritsa Uthenga Wabwino komanso utumiki.
- Antchito amene akudzala mipingo yatsopano komanso amene akuchita utumiki.
- Okhulupirira onse amene akuvutika chifukwa chakudzipereka kwao kwa Khristu kapena chifukwa cha utumiki.
- Ntchito imene anthu omasulira Baibulo akugwira ntchito pa dziko lonse lapansi.
- Anthu onse amamene akuphunzitsa maphunzira a Baibulo, ndi ma Sukulu onse osula azibusa.
- Anthu onse ogwira ntchit a christu amene akugwira maiko ena.
- Atumiki amene akutimikira pakati anthu achikhalidwe china.
- Kuyenda kwa Mulungu pakati pa achinyamata chifukwa iwo ndi atsogole a amawa a mumpingo.
- Mavumbulutso a ndondomeko zothandiza kufikira midzi ndi maiko onse. Kupempha Mulungu kuti awonetsetse zimenezi kwa anthu onse amene akugwira ntchito yake mu zigawo zosiyana za dziko lapansi. Pemphelelani ma Bungwe amene akugwira ntchito yochita kafukufuku wa utumiki ndi ndondomeko za utumiki.
- Chitetezo kwa Satana pa onse amene akutumikira. Manganic ntchito zonse zolimbana ndi okhulupirira onse (Aroma 15:30-31; II Atesalonika 3:2).
- Kutu okhulupirira akhale ndi maonedwe a zinthu malingana ndi Baibulo komanso kuti achoke pongokhala owonenera ndi kuyamaba kuchitapo kanthu mu chikonzero cha Mulungu.
- Onse amane amagwira zintchito zimene si zauzimu koma ndi cholinga chifaritsa Uthenga Wabwino.
- Okhulupirira mene ndi ankhondo koma akugwira ntchito mu dzigawo zosiyanasiya za dziko lapansi. Anthu amenewa akhoza kukhala chida chabwino chofaritsira Uthenga Wabwino.
- Ntchito ya anthu onse amene amafaritsa mau a Mulungu kudzera pa wayilesi, kanema ndi zina zambiri.

- Ntchito ya anthu onse amene akuthandiza ngati achipatala komanso mu madera ena ndi ena achitukuko.
- Atumiki onse amene ndi oyendetsa ndege zimene zimanyamula katundu wa utumiki komanso atumiki ku zigawo zosiyanasiyana za dziko lapansi.
- Ntchito ya anthu onse amene akugwira ndi anthu othawa kwao pa dziko lonse lapansi.
- Kumanga mphamvu zonse za Satana zimene zikugwira ntchito mu zigawo zosiyanasiyana za maiko. Kupezeka kwa mphamvu zimenezi kukuonetseredwa mu buku la Danieli pamene akukamba za Karonga wa Ku Peresiya. Mphamvu zimenezi zimaonetsera chifukwa chake zigawo zina zimakhala zokonzeka kulandira Uthenga Wabwino kusiyana ndi zigawo zina. Mizimu ina imagwira ntchito mu zigawo zina zake kotero kuti ngati okhulupirira sangapembedzere, zimakhala zovuta kuti anthu atembenuke mtima muzigawo zimenezi.

KUPEMBEZERA CHIGAWO CHIMODZI CHA DZIKO LAPANSI (MPINDI 10)

Mapemphero anu akhazikike pa dziko kapena chigawo chimodzi cha dziko lapansi. Pali mabugwe angapo amene akhoza kupereka chidziwitso chokhudza chigawo cha dera linalake. Palinso magulu anthu amene akhoza kukuthandizani kuti mupemphere molunjika. Werengani chigawo cha zonjezera pohunzira.

Zina mwa zinthu zimene mukhoza kupemphelera mwa chindunji zokhudza dziko lina lilironse ndi izi:

- Zinthu zimene zikuchitika mu nthawi iemeneyo. Mukhoza kudziwa zinthu zimene zikuchitika kudzera kumvera nkhani kapena kuonera kumene pa kanema. Komanso mukhoza kufunsa anthu ena a chikhristu amene akugwira ntchito chigawo chiemecho.
- Mipingo ya dziko.
- Anthu onse amene akutimikira mdzikomo. Anthu amenewa akhoza kukhala odzala mipingo, aphunzitsi a sukulu za Abusa komanso amene akumasulira Baibulo.
- Okhulupirira onse a mdziko.

- Kumanga mphamvu za Satana zimene zimagwira ntchit mu dziko. Izi ndi mphamvu zimene zimalimbana ndi kufaritsa kwa Uthenga Wabwino kapena kuletsa kularikidwa kwa Uthenga Wabwino.
- Mu dziko lina lilironse, pamakhala magawo asanu ndi awiri amene amakhala ndi mphamvu pa kaganizidwe ka anthu komanso pa tsogolo la anthu mudziko. Madera amenewa ndi: makomo ndi mabanja, mpingo, maphunziro, zaluso ndi za msangulutso, zoulutsa mau, boma ndi ma businezi. Mukueyenera kupembedzera atsogoleri komanso moyo wauzimu mu madera amenewa.

KUPEMBEDZERA MABUNGWE OTUMIKIRA (mphindi 10)

Pakulumukizana ndi mabungwe amene akutumikira muzadziwa zinthu zimena amasowa zimene mukhoza kuzipemphelera. Lembetsani dzina lanu kuti mukhale munthu mmodzi amene adzilandira nkhani zokhudza mabungwe amenewa.

PEMBEDZERANI MAGULU ANTHU AMENE SANAFIKIRIDWE (mpindi 10)

Magulu asanu a anthu amene sanafikiriedwe ndi awa: Anthu Achibuda, Achihindu, Asilamu, aku China, ndi anthu mitundu ina ya kumudzi.

Pemphelerani njala yauzimu pakati pawo.

- Pemphelerani antchito kuti afaritse Uthenga kwa anthu amenewa.
- Pemphelerani ndondomeko zabwino zothandiza kufikira anthuwa.
- Pemphelerani iwo amene akutumikira kale pakati pa anthu amenewa.

MAPEMPHERO A ZOSOWA ZANU (mpindi 10)

Ganizirani za zosowa zanu malinga ndi zinthu zakuthupi. Kodi zosowa zanu zanu zikugwirizana bwanji ndi cholinga cha Mulungu pa dziko lapansi. Ngakhale zinthu zimene zimakhudza inu zimagwirizana ndi chikonzero cha Mulungu cha dziko lapansi.

Pitirizani kufunafuna Mulungu kuti mukwaniritse galo la cholinga chofuna kufikura dziko lonse ndi Uthenga Wabwino. Kodi mungazikonzeretse bwanji nokha ku ntchito imeneyi? Kodi

mungayambe bwanji kugwira ntchito imeneyi? Kodi mungapeze bwanji nthawi yanu komanso zachuma zanu zochulukana ndi cholinga choti mutumikire.

OLA LAKUPEMPHERA

Uku ndi kufotokera mwachidule mmene ola limodzi la kupemphera likuyenera kugawidwira:

1. Kuyamika Mulungu (mpindi 10)
2. Kupembedzera dziko lonse lapansi (mphindi 10)
3. Kupembedzera chigawo chimodzi cha dziko (mpindi 10)
4. Kupembedzera mabungwe otumikira kapena atumiki (mpindi 10)
5. Kupemphelera zinthu zimene mukuzisowa ngati munthu (mpindi 10)

KONZANI MLOZO WA MAPEMPHERO

Dongoloso la nokha la mapemphero likuthandizani kuti muchite kupembedzera kwa dziko lonse. Ena mwa malangizo pokonza mlozo umeneu ndi awa:

CHIGAWO CHOYAMBA: CHIKONZERO CHA MAPEMPHERO:

Chikonzero cha mapemphero mu gawo limeneli chichokere ku ola limodzi la kumbedzera dziko lonse. Ndipo onetserani mu mlozo mmene mupemphelere mu ola limeneli.

CHIGAWO CHACHIWIRI: DZIKO LONSE:

tangani zopemphelera za dziko lonse lapansi zimene zalembedwa mu chaputala chino ndi kuzilemba mu mlozo othandizira kupemphera. Mukhoza kuonjezera mapemphero ena amene dziko lapansi likufunika pamene Mulungu akuunikirani kapene kuvumbutsa kwa inu.

CHIGAWO CHACHITATU: MADERA OSIYASIYANA:

Pezani uthenga komanso mapu okhudza madera osiyasiyana ndipo muike mauthenga ikhudza madera amewa mu chigawo chimenechi. Mukhoza kuikanso nkhani zochikere mu nyuzi pepala zokhudza madera amenewa zimene zikufotokoza zinthu zochitika, makamaka zinthu zimene zimasokoneza kufaritsa Uthenga Wabwino mu dzikolo. Pemphelerani zinthu zimenezi.

Musaiwale kupephelera dziko lanu, mzinda wanu kapena mudzi wanu. Pezani mapu a dziko lanu ndipo muwaike muchigawo chimenechi.

Ngati mzinda wanu uli buku la ma namabala a phone, gwiritsani ntchito bukuli kuti mupephelere munthu wina aliyense mudzi mwanu. Pezani mndandanda wa maina atsogoleri onse a mdera lanu ndi cholinga choti mudziwapemphelera.

GAWO LACHINAYI: MABUNGWE A ATUMIKI KAPENA KUTI MAMISHONARE:

Mu gawo limeneli mukhoza kulemba mdandanda wa mamishonare amene mukufuna kupemphelera. Pezani nkhani zochokera mu ma nuzi pepa ndipo pemphelera zosowa zawo.

Ngati mpingo wanu uli ndi ma mishonare, pezani mdandanda wa maina awo ndi kuyamba kuwapemphelera. Pezani zinthu zina zokhudza mabugwe autumiki ndipo pemphelerani zosowa zawo. Pezaninso main a mipingo, mabugwe a chikhristu amemene akugwira ntchito mu dera lanu ndipo pemphelerani zosowa zawo.

GAWO LACHINAYI: MAGULU A ANTHU OSAFIKIRIDWA:

Lembani maina magulu a nthu amene sanafikiridwe mu gawo limeneli. Ndipo yambani kupeza mauthenga okhudza anthu amenewa. Ikani zimene mwapeza mu gawo limeneli mu mloza wa mapemphero.

GAWO LACHISANU NDI CHIMODZI: PEMPHELERANI ZOSOWA ZANU:

Lembani mdandanda wa zinthu izi pa pepala kuti zopembedzera zanu zisungike.

Tsiku Chosowa chanu Tsiku limene munalandira mayankho

Kulemba zinthu zopembedzera kukuthandizani kuti mulunjike pa zopemphelera zanu komanso kuti muzindikire pamene Mulungu wa kuyankhani.

PHUNZITSANI ANTHU ENA KUTI AKHALE OPEMBEDZERA A DZIKO LONSE:

Mukhoza kuphunzitsa anthu ena kuti akhale opembedzera a dziko lonse pogwiritsa ntchito ndondomeko izi:

1. Afotokozerani maonedwe a dziko malingana ndi Baibulo:

Choyamba fotokozerani kwa anthu maonedwe a dziko lapansi malingana ndi Baibulo. Pokhapokha munthu atamvetsetsetsa kaonedwe ka dziko malinga ndi Baibulo ndi pamene angathe kukhala opembedzera wa dziko lonse. Chaputala 10 chikufotokozerana mmene munthu afotokozere maone a dziko malinga ndi Baibulo.

2. Gwiritsani ntchito chaputala ichi kuti muphunzitse anthu zakupembedzera Kwa dziko lonse.

Choyamba werengani limodzi chaputala chimenechi. Kenako yambani kupemphelera malinga ndi ndondomeko zimene zaperekedwa mu chaputalachi.

3. Pangani gulu la anthu opembedzera a dziko lonse:

Kuthandizana kumene kumapezeka pa gulu kuthandiza kuti gululo likhale lodziepereka kupembedzera dziko lonse. Khazikitsani nthawi, malo komanso tsiku limene mudzikumana. Gulu limeneli likhoza kukumana ku nyumba ya munthu kapena ku kachisi kumene. Gwiritsani ntchito dongosolo lakapempheredwa limene laperekedwa mu buku ili komanso mu mlozo wakupembedzera umene mwapanga. Gwiritsani zinthu zina zoonjezera zimene zikupezeka mu gawo la zoonjezera pophunzira.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Kodi kukhala opembedzera wa dziko lonse kumatanthauza chani?

3. Kodi mungaphunzitse bwanji anthu ena kukhala opembedzera a dziko lonse lapansi.

4. Kodi munapanga malonjezano kuti mukhale opembedzera wa dziko lonse lapansi?

5. Kodi munakhazikitsa ndongosolo la nokha la kupembedzera?

6. Kodi kufunika kutatu kwa kupembedzera dziko lonse ndi kofunika bwanji malingana ndi mfundo zimene tafotokoza mu ndime imeneyi.

7. Fotokozani dongosolo la mapembedzedwe a dziko lonse malinga malingana ndi dziko lonse.

(Mayankho amafunso awa ali kumepeto kwa buku limeneli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Zinthu zolembedwa izi zikupezeka kudzera ma bungwe osiyanasiya amene ndi achikhristu ndipo zinthu izi zikhoza kukuthandizani pamene mukupembedzera dziko lonse. Mukhoza kupita pa makina a internet kuti muone mauthenga a tsopano.

1. Operation world: Ili ndi buku limene limapereka uthenga okhudza maiko osiyanasiyana komanso ndi zinthu zimene mukhoza kupemphelera.
2. Opembedzera a dziko lonse: amapereka mauthenga okhudza maiko osiyanasiyana ndi zofuna kupemphelera.
3. Joshua Project: amatsindika mapemphero pa anthu amene sanafikiridwe.
4. Lowani gulu lanthu limene cholinga chake ndi kupemphera.

CHAPUTALA 10

KUGAWANA NDI ENA MAONEDWE A DZIKO MALINGANA NDI BAIBULO:

ZOLINGA

Pamapeto paphunziro ili mukuyenera kukwanitsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsolera osaonera.
- Kuzindikira njira zinayi zogawanira ndi ena kaonedwe ka dziko malingana ndi Baibulo.
- Kugawana maonedwe a dziko malingana ndi Baibulo ndi okhulupirira ena.
- Kukhazikitsa komiti yofalaritsa Uthenga Wabwino.
- Khazikitsani gulu la dziko lonse lowerenga Baibulo.

VESI YOTSGOLERA:

Ndipo zimene wazimva Kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize Kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)

MAU OYAMBA

Monga taona kale, miyandamiyanda ya anthu ilibe maonedwe a dziko malinga ndi Baibulo. Chidwi cha anthu amenewa changokhazikika pa mabanja awo, midzi yawo, komanso mipingo yawo. Chifukwa chakuti samamvetsa chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi, iwo sametenga gawo pakukwaniritsa mbali yawo mu chikonzekero cha Mulungu. Chaputala ichi chifotokozerammene mungafotokozeramaonedwe a dziko malingana ndi Baibulo kwa anthu amenewa.

ANTHU OKHULUPIRIKA

Kuti kufotokozerakwanu kwa kaonedwe ka dziko malingana ndi Baibulo kakhale koyenera, mukuyenera kusankha anthu amene ndi okhulupirika kuti muwaphunzitse.

Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)

Mau oti okhulupirika amatanthauza, odalirika, odalirika, komanso ochitachita:

Siwina aliyense amene angalandire maonedwe a dziko malingana ndi Baibulo komanso siwina aliyense amene akhoza kukhala okhulupiririka ku zinthu zimenezi. Choncho, pamene mufuna kugawana masomphenya ndi anthu ena muyenera kusankha anthu amene ndi odalirika, ochitachita, komanso okhulupirika ku kuitana kwa Mulungu. Anthu amene mungagawane nawo masomphenya amenewa ayenera kukhala okonzeka kuphunzitsa anthu ena. Iyi ndi njira yokhayo imene kuchulukitsa ndi kubala kumabwelera.

ZA MAM'BAIBULO OSATI ZACHIKHALIDWE

Kumbukirani kuti pamene mukugawana ndi anthu ena zimene mwaphuzira, mukuyenera kudziwa kuti mwaitanidwa kuti mukagawane ndi anthu ena maonedwe a zinthu malingana ndi Baibulo osati maganizo anu malinga ndi chikhalidwe chanu.

Chikhalidwe ndi zinthu zimene munthu amaphunzira pa kachitidwe ka zinthu. Chikhalidwe chimakhudza chilankhulo ndi miyambo kapena kuti makhalidwe a anthu ndi mbali imodzi ya chikhalidwe.

Munthu amakhudzika ndi chikhalidwe chimene chamuzungulira. Anthu amaona kuti kachitidwe kawo ka zinthu ndiye koyenera. Koma mukuyenera kuzindikira kuti palibe chikhalidwe chimene ndi chabwino kuposa chinzake. Chifukwa cha ichi, simunaitanidwe kuti magawane ndi anthu chikhalidwe chanu kapena machitidwe anu a zinthu amene mumaona kuti ndi oyenera.

Pamene chikhalidwe chikusemphana ndi mau a Mulungu ndi pamene inuyo mukuyenera kuchitapo kanthu. Mukuyenera kuchitapo kanthu chifukwa ili limakhala kuti ndi ntchimo. Inu simunaitanidwe kuti mukafaritse chitukuko kwa anthu achikunja, koma mwaitanidwa kuti mukapululumutse moyo wao. Cholinga cha nsodzi sikusinthana Nyanja, koma ndi kugwira nsomba.

Chidwi chanu chiyenera kukhala pa ntchito imene mukuyenera kugwira: Kuphunzitsa amayi ndi abambo okhulupiririka:

DONGOSOLO

Izi ndi ndondomeko zimene zikuyenera kutsatidwa kiti mugawane ndi anthu ena maonedwe a dziko malingana ndi Baibulo:

1. Kukhala chitsanzo cha bwino cha masomphenya

2. Kufotokozerana anthu ena masomphenya anu.
3. Masomphenyawo akhale chinthu chimene muike chidwi chachikulu cha moyo wanu.
4. Mverani masomphenya.

Tiyeni tione dongosolo lonse mwandondomeko yake.

KHALANI CHITSANZO CHA MASOMPHENYA:

Choyamba inuyo mwina mukuyenera kuvomereza maonedwe a dziko malingana ndi Baibulo chifukwa ichi ndiye cholinga cha phunziro limeneli. Pamene mwazindikira za udindo wanu pa kutumidwa kwakukulu ndipo pamene mtima wanu ndi okhudzika ndi maiko a dziko lapansi, mukhoza kukhala chitsanzi cha masomphenya.

Ngati chitsanzo, mukhala munthu amene anthu amayang'anira pa inu mu mpingo ngakhale azanthu amene. Muyenera kuti iwo awone mtima wanu kapena kukhudzika kwanu pa ntchito ya Khristu komanso kudzipereka kwanu ku maiko a dziko lapansi. Kuophunzira kwa mphamvu sikumachitika ndi mau koma kumachitika powonetsera chitsanzo. izi tikuziona mu moyo ndi utumiki wa Khristu Yesu.

KUFOTOKOZERA ANTHU ENA MASOMPHENYA

Zina mwanjira zothandiza kufotokozerana anthu ena masomphenya ndi izi:

1. Gawanani masomphenya ndi anthu paokhapaokha. Gawanani ndi anthu phunziro limeneli kuna zinthu malingana ndi Baibulo. Ndi anthu amenewa, gawanani nawo chosowa chachikulu cha dziko lapansi komanso mufotokozerana udindo wao pakukwanitsa izi. Pempheperani limodzi ndi anthu amenewa pogwiritsa ntchito ndondomeko zimen zaperekedwa mu chaputala 9.
2. Apemphene abusa anu kuti mwakanthawi yochepa munthawi yachipembedzo, pakhale kuunikira mmene moyo wauzimu ukuyendera pa dziko lapansi, anthu amene sanafikiridwe ndi zimene mungachite kuthana ndi zinthu zolepheretsa.

3. Faritsani nkhani mu mpingo mwanu zokhudzana ndi maonedwe a zinthu malingana ndi dziko lapansi. Mukhoza kuchita izi kudzera mu zolembalemba zimene zimaikidwa mmakoma.
4. Khazikitsani kunyumba kwanu kapena ku tchalitchi malo amene anthu akhoza kupeza mauthenga osiyanasiyana. Mauthenga amenewa akhoza kukhala makalata ochokera kwa ma mishonare mabuku okhudza anthu amene sanafikiridwe komanso phunziro lino likhoza kukhala mbali imodzi ya mauthenga opezeka malo amene akhazikitsidwa.
5. Pemphani ma mishonare ena amene ali maiko akunja kuti agawane nanu zinthu zithunzi ndi zina zoonetsera zinthu zimene akuchita.
6. Chitanipo kanthu pakapempheredwe mu mpingo wanu pamene zopemphelera zikulembedwa, musaiwale kulemba zopembedzera za dziko lapansi.
7. Ngati muli pafupi ndi ndi Sukulu ya ukachenjede, pemphani ophunzira amene achokera maiko ena kuti agawane nanu zinthu zokhudza chikhalidwe chao.
8. Pangani komiti yofaritsa Uthenga Wabwino ngati mulibe komiti imeneyo mumpingo wanu. Gawo la zoonjezera pophunzira liri ndi ndondomeko zimene mungatsate kuti mupanga zinthu zimenezi:
9. Konzani misonkhani ndi cholinga chowazindikiritsa anth. Mukhoza kuchita izi mu mpingo mwanu kapena pakhomo panu. Itanani anthu ochokera ku mabungwe osiyanasiyana kuti adzalankhule kumkumano imeneu.
10. Pempani abusa anu kuti apereka buku *“la kukuza maonedwe a dziko malingana ndi Baibulo ku mpingo onse”* Ndipo phunzitsani anthu patchalitchi kapena ku nyumba.

MOYO WANU UKHAZIKIKE PA MASOMPHENYA:

Chidwi chanu chachikulu chikhazikike pa masomphenya muli nawo komanso pa amayi ndi abambo amene mukuwaphunzitsa. Ndondomeko zina zimene mukhoza kutsata ndi izi:

1. Pitirizani kuwerenga mabuku amene akukamba kwambiri za maonedwe a zinthu malingana ndi Baibulo komanso kutumikira.

2. Tengani gawo pa misonkhano yowona za kufalitsa uthenga Wabwino.
3. Khalani odziwa zinthu zimene zikuchitika pa dziko lapansi zimene zimalepheleretsa kufalikira kwa uthenga Wabwino ndipo pitirizani kupemphelera dziko lapansi.
4. Mudzilumikizana ndi anthu amene akutumikira zigawo zosiyanasiyana za dziko lapansi. Maumboni awo amathandiza kuti muchirimike.
5. Khazikitsani nthawi yosanthula Baibulo ndi cholinga choti mugawane ndi anthu ena. Gawo la zoonjezera pophunzira likuthandizani mmene mungachitire zinthu izi.

MVERANI MASOMPHENYA:

Sizokwanira kungokhala ndi kaonedwe ka zinthu malinga ndi ndi Baibulo, koma ndi zofunika kuti muyenera kuchitapo kanthu pa zimene mwaphunzira.

Koma pamene akatembenukira kwa Mulungu, cophimbaco cieotsedwa. Koma Ambuye ndiye Mzimuyo; ndipo pamene pali Mzimu wa Ambuye pali ufulu. (II Timoteo 3:16-17)


Mfundo ina iliyonse ya Baibulo ikuyenera kutithandiza kuti tikachite Utumiki Moyenera. Mwaphunzira mfundo zambira mu phunziro limeneli, koma chidziwitso chopanda kuchitapo kanthu chili ngati chikhulupiriro chopanda ntchito. Ngati mukungophunzira mfunmdo komanso palibe chimene mukuchita nazo mfundozi, mapeto ake ndi imfa yauzimu. Kulandira masomphenya sikokwanira, kufotokozero masomphenyawo sikokwaniranso ayi. Chofunika ndi chakuti amene akuphunzitsa ndi ophunzitsidwa akuyenera kumvera masomphenyawo.

Harvestime International Institute ili ndi maphuunziro amene akuthandizeni kuti mukwaniritse kuchita izi: phunziro limene limabwera patsogolo pa phunziro ili ndi *ukadaulo ophunzitsa*. Phunziro ili likuthandizani kuti mukwanits kugawana ndi ena molongosoka zimene mwaphunzira. “Ndongomeko zakuchulukukitsa” ndi phunziro limene likuthandizeni kuti muthe kuchulukitsa mphamvu zauzimu za anthu amene mwa aphunzitsa. Koma simukuyenera kudikira kuti muchite kumalizitsa maphunziro anu a Harvestime International Institute. Yambanipo kukwaniritse masomphenya malo amene muli. Zina mwa ndondomeko zimene mungatsate ndi izi:

1. Gawani Uthenga Wabwino kwa anthu amene ali mmudzi mwanu, kapena malo amene akuzungulirani.
2. Gwirani ntchito ndi mipingo imene ikupezeka mudera mwanu komanso ndi imemne ikupezeka maiko ena.
3. Pemphelelerani maiko onse a dziko lapansi.
4. Perekani thandizo ku mabugwe kudzera kumpingo kapena ku mabungwe ena. Kupereka kwa anthu amene akutumikira Uthenga Wabwino kukuyenera kutsindikidwa.
5. Fikirani kupyola malire a dera lanu. Konzani dongosolo la kufaritsa uthenga Wabwino mudera lanu kapena midziko lanu.

NDONDOMEKO YA KUPITILIRA

Iyi ndi ndondomeko yakubala malingana ndi Baibulo:



Choyamba mukuyenera kukhala chitsanzo chabwino cha masomphenya amene mwalandira, kenako gawanani ndi anthu ena masomphenya amenewa kudzera pokhala chitsanzo komanso kuphunzitsa. Chidwi chanu chachikulu chikhale pa maonedwe a dziko malingana ndi Baibulo. Pamene muyambe kuphunzitsa anthu ena kuti amvera masomphenya amenewa, mumakhala chitsanzo chabwino cha masomphenya amenewa kotero kuti masomphenyawa amapitilira.

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Kodi ndi mtundu wanji wa anthu amene mukuyenera kugawana nawo maonedwa a dziko lapansi malingana ndi Baibulo.

3. Tchulani ndondomeko zinayi zimene zikuyenera kutsatidwa pamene mukugawana ndi ena maonedwe a dziko lapansi malingana ndi Baibulo.

4. Kodi ndi zinthu ziti zimene mukuyenera kuchita pokwaniritsa masomphenya ofikira dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino. Ndi ndani amene mukuyenera kugawana naye masompenya amenewa? Ndi chiani chimene mungachite mu mpingo wanu? Ndi zinthu ziti zimene mungachite kumalo amene mumakhala?

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku limeneli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

KUPANGA KOMITI YOFALITSA UTHENGA WABWINO (EVANGELIZIMU)

Mu mphunziro limeneli, panaperekedwa ganizo lonena kuti pampingo pakhazikitsidwe komiti yowona zofaritsa Uthenga Wabwino. Kufaritsa Uthenga kapena kuti Komiti ya evangelizimu sikungoyenera kukhala komiti chabe ya pampingo, koma ikuyenera kukhala gawo lalikulu la mpingo. Cholinga chokhazikitsa Komiti ngati imeneyi ndi chakuti itsogolere mpingo kuti ukwaniritse cholinga chake. (Werengani chaputala 6 cha Mpingo pa dziko lapansi).

YAMBANI NDI ABUSA

Choyamba kumanani ndi abusa anu ndipo afokozereni masomphenya anu ofuna kuyambitsa komiti ya evangelizimu. Mwina ndi kutheka kuti akhoza kusangakha inuyo kuti mutsogolere komiti imeneyi. Ndi zofunika kuti muyambe kaye mwapeza chilorezo kuchokera kwa abusa anu.

UNIKIRANI MA POLOGALAMU AMENE AKUCHITIKA.

Kodi zinthu zili bwani pakadali pano mu mpingo wanu mumadera ofaritsa Uthnganga Wabwino? Ganizirani zinthu izi:

Ndondomeko:

Kodi mpingo wanu uli ndi ndondomeko ina iliyonse yolembedwa imene imakhudza kufaritsa Uthenga Wabwino. Kodi ngati zili choncho, kodi ndondomekoyo ndi yokwanira ndipo kodi ikugwirizana ndi zimene mpingo ukuchita?

Pemphero:

Kodi ndi kangati kamene mpingo wanu umapemphera pamodzi pa zinthu zosowa zogwirizana ndi kufaritsa Uthenga Wabwino. Kodi mpingo wanu unayamba wapemphelera atumiki nthawi yachipembedzo malingana ndi Mateyu 9:38.

Misonkhano ikulu ikulu:

Kodi mpingo wanu unayambapo wakonza msokhano waukulu omwe ndichilinga chofuna kufaritsa Uthenga Wabwino mu chaka changopitachi.

Maphunziro:

Kodi mpingo wanu umapereka maphunziro okhudzana ndi maonedwe a dziko malingana ndi Baibulo amene atsindika kufunika kofaritsa Uthenga Wabwino? Kodi mu li ndi maphunziro amene amakhudza magulu osiyanasiyana mu mpingo?

Kutengapo gawo:

Kodi ndi zinthu zokhudza kufalitsa uthenga Wabwino zimene mpingo wanu inatengapo mbali mbuyomu? Ndi zinthu ziti zimene mwapanga mdera lanu kapena mdiko lonse. Ndi zikonzero ziti zimene zinachita bwino ndipo ndi ziti zimene zinalephera.

Kodi ndi zinthu ziti zimene zimene zakhala zikutengapo mbali pakufaritsa Uthenga Wabwino? Mwachitsanzo, pali magulu awa: achinyamata, amayi, abambo, ndi magulu ena. Kodi ndi udindo wanji umene mabanja akutenga pofaritsa utheng Wawbino?

Thandizo:

Kodi ndi ma mishonare ati emene mpingo wanu ukuwapatsa thandizo? Kodi akupezekera kuti? Kodi ndi mlingo wanji wa ndalama kapena chithandizo chimene mumawapatsa?

Dongosolo la za chuma:

Muyenera kupanga chiganizo kuti ndi gawo lanji la ndalama mudongosolo la zachuma zimene ziperekedwe ku ntchito yofaritsa Uthenga Wabwino. Kuti mukwaniritse izi, malizitsani ziganizo zimene zili munsimuzi.

Zopereka zonse zimene mpingoo umatolera ndi izi K_____

Pa ndalama zimenezi, tinapereka ndalama zokwana K_____ ku ntchito yofaritsa Uthenga Wabwino?

Izi zikutanthauza kuti gawo lokwana _____ ya mu ndondomeko ya zachuma inaperekedwa ku ntchito yofaritsa uthenga Wabwino chaka chatha.

- Zinthu zofunika pa ntchito:

Zinthu zimene zikhoza kukhala: ndalama, anthu, zida ndi nyumba. kodi zinthu za mumpingo zikugwira bwanji ntchito mumpingo wanu.

KUPHUNZITSA MPINGO

Phunzitsani phunziriko la Kukuza maonedwe dziko malingana ndi Baibulo. Gwiritsani ntchito phunziro ili kuti muphunzitse izi kwa anthu.

KONZANI MSONKANO WA ZOKAMBIRANI

Konzani msonkhano umene a komiti ya evangelizimu mukambirane.

Udindo wa evangelizimu komiti:

Zina mwa ntchito za evangelizimu komiti ndi izi:

- Kukhala chitsanzo ku mpingo onse kudzera mu pemphero, kupereka ndi kutengapo gawo pa kufaritsa Uthenga Wabwino.
- Kutsogolera mapemphero a mpingo onse pa nkhani za evangelizimu kapena kufaritsa Uthenga Wabwino.
- Kukhazikitsa zolinga zofaritsira Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi komanso mu dera lanu.
- Kupanga chiganizo pa zinthu zimene ziyenera kugwiritsidwa ntchito pofuna kufaritsa uthenga
- Kufotokozera anthu zinthu zokhudza kufaritsa Uthenga Wabwino.
- Kukonza dongosolo la zachuma la chuma lokhudza kufaritsa Uthenga Wabwino ndi kukonza njira zimene zigwire ntchito popeza ndalama zimeneni. Komanso kuonetsera mmene ndalama zimenezi zigwilire ntchito.
- Kukoza mlozo wa dongosolo la mmne ntchito yofarita uthenga igwilire ntchito iyendera pachaka.
- Kukonza ndi kuphunzitsa anthu zokhudza kufaritsa Uthenga Wabwino.
- Kulimbikitsa ntchito yofaritsa Uthenga Wabwino kudzera mu pemphero, kupereka ndi kutenga mbali. Komitiyo ikuyeneranso kubweretsa maganizo amene akhoza kuthandiza.
- Kufufuza zinthu zimene mpingo ukhoza kuthandiza.

- Kulumikizana ndi mabungwe onse amene akufaritsa uthenga Wabwino.

KUKHAZIKITSA KOMITI YA EVANGELIZIMU:

Zina mwa zinthu zimene mukhoza kutsata pokhazikitsa komiti ya evangelizimu ndi izi:

- Abusa:

Abusa ali ndi ulamuliro opereka chitsogozo ku komiti. Izi zilo chomwecho chifukwa chakuti m'busa ndi amene amatsogolera mpingo. Amaperekanso uphungu kwa atsogoleri ena a mumpingo kuti akwaniritse maudindo awo.

Mlembi.

Ntchito ya mlembi ndi kusunga zinthu zolembedwa zokhudza zimene atumiki akuchita komanso ntchito zimene zikugwiridwa.

- Mkulu oyang'anira kupeza ndalama

Amatsogolera ntchito yopeza ndalama.

- Msungi chuma

Amakonza ndondomeko ya zachuma yokhudza kufaritsa uthenga Wabwino. Apatulutsa ndalama zopita ku ntchito zosiyanasiyana komanso zothandizira atumiki a Mulungu.

- Mkulu oyang'anira mapemphero.

Amatsogolera mpingo nkhani zopemembedzera zimene zokhudza kufalitsa uthenga Wabwino. Iye amalimbikitsa mpingo kupemphelera komanso mapemphero oyankhidwa.

- Mkulu oyang'anira zofaritsa Uthenga:

kozani mauthenga oti afalitsidwe kudzera ku nuzi pepala, wailesi, ndi njira zina zofaritsira mauthenga.

- Mkulu oyang'anira zophunzitsa.

Amakonza maphunziro ndi cholinga choti mpingo onse uphunzitsidwe mkhani zokhudza kufalitsa Uthenga Wabwino. Ndongomeko zamaphunziro zikuyenera kukhudza magulu onse

a anthu mu mpingo. Ngati pali ndalama zokuyenerezani, pezani ma buku osiyanasiyana okhudza kufaritsa Uthenga Wabwino.

- Mkulu oyang'anira za misonkhano:

Amakonza ndi kulimbikitsa misonkhano ikuluikulu.

- Mkulu oyang'anira za kufalitsa Uthenga mmadera.

Amakonza ndondomeko zokhudza kufaritsa uthenga mmadera. Ena mwa malo amene Uthenga Wabwino umalalikiridwa andi awa: mundende, khomo ndi khomo, komanso kufikira anthu amene angobadwa matsopano kumene ndi amene ayamba kumene mpingo.

- Mkulu oyang'anira kufaritsa Uthenga mdziko: Mkulu ameneyu ntchito yake ndi

CHITANI MKUMANO WA ZOKONZEKERA:

Komiti ya evangelizimu ikuyenera kukumana pafupi ndi pafupi ndi cholinga chofuna kukonza madongosolo a kufaritsa Uthenga Wabwino. Kuchokera nthawi imene mukukambirana komanso kupemphera, khazikitsani zinthu zimene mukufuna kuti mukwanitse pofaritsa Uthenga Wabwino. Kukhazikitsa zolinga kukuthandizani kuti mukwaniritse zolinga zimene mwakwaniritsazo. Kutu mudziwe zambira zokhudza izi, pezani phunziro la Haverstime International institute lotchedwa “management Objective” kapena kuti Kayendetsedwa ka zinthu.

Mukhazikitse Zolinga zokhudza:

- Mfundo:

Ngati mpingo wanu uli ndi mfundo zolembedwa zokhudza kufaritsa uthenga, unikirani mfundo zimenezi ngai zili zokwanira. Koma ngati mpingo wanu ulibe mfundozi, ndiye kuti mukuyenera kuti mulembe mfundozi. Mfundo zakufaritsa Uthenga Wabwino zikuyenera kufotokoza zolinga komanso zinthu zimene mukufuna kukwanitsa.

- Pemphero:

Yambani ndi kupemphera limodzi ngati a komiti. Bweretsani zonse zofuna kupemphelera zokhudza kufaritsa Uthenga Wabwino.

- Misonkhano ikuluikulu.

Pangani dongosolo la misonkhano ikuluikulu yobweretsa anthu onse pakamodzi. Pa misonkhano imeneyi, olankhula alankhule zokhudza kufaritsa Uthenga Wabwino.

- **Kuphunzitsa anthu**

Perekani maphunziro a Baubulo ndi cholinga choti anthu akhale ndi maonedwe a zinthu malingana ndi Baibulo.

Mukhoza kukhazikitsa dongolo la chaka chonse lophunzitsa limene mukhoza kuphunzitsa zinthu zokhudza mabungwe a atumiki.

Yambani kukhazikitsa nyumba yosungiramo mabuku imene mukhoza kusunghanitsa zinthu zimene zikhoza kuphunzitsa anthu.

Kutenga mbali:

Inikirani zimene mpingo wanu wakhala uchita mbuyo zokhudza kufaritsa Uthenga Wabwino. Yambani kupemphera ndi kukoza ndondomeko za mmene mungafaritsire Uthenga Wabwino.

Kodi ndi zinthu ziti zimene munalephera mbuyomu ndipo kodi mungapewa bwanji zinthu zimenezi mtsogolo.

Gulu lina lilironse la mumpingo litenga nawo mbali. Chimene mukuyenera kuchita ndi chakuti magulu onse akhale ndi owaimira pamene mukuchita zokambirana zokhudza kufaritsa Uthenga.

Onenetsetsani kuti mabanja akutenga nawo mbali pofaritsa Uthenga Wabwino pogwiritsa ntchito njira izi:

- * Banja linalilironse likhale ndi mapu a atumiki amene akufaritsa Uthenga madera ena ndipo mabanjawo ayenera kuyenera kupemphera atumiki amenewa.
- * Mabanja alandire atumiki amene akufaritsa Uthenga Wabwino.
- * Mabanja akhoza kupereka ndalama zamayendedwe kapena malo ogona kwa atumiki ofaritsa Uthenga Wabwino.
- * Kutolera mabuku okhudza atumiki a uthenga Wabwino.
- * Kukhala ndi malo mnyumba mwanu amene mungathe kusunga ndalama zothandiza anthu amene akufaritsa Uthenga Wabwino.
- * Makolo okhoza kulimbikitsa ana kuti atenga gawo pofalitsa Uthenga wabwino mdera lawo.

- **Chithandizo**

Wonjezerani chiwerengero cha atumiki amene mpingo wanu ukuthandiza kuti atumikire. Ganizirani zotumiza atumiki kuti **akatumikire madera ena amene ndi achikhalidwe china.**

- **Dongosolo la zachuma:**

Pangani dongosolo loti muonjezera ndalama zimene zimaperekedwa ku gawo lofalitsa Uthenga Wabwino:

Ngai munthu wina aliyensa angapereka _____ pa tsiku kwa atumiki ndiye kuti pachaka ndikhoza kupereka ndalama zokwana _____ ndekuti ngati pali anthu okwana _____ tikhoza kupeza ndalama zokwana _____ pachaka.

Mwachitsanzo, ngati mpingo wa anthu 200 wina aliyesne angapereke ndalama zokwana 10 cents patsiku, ndiye kuti mpingo umeneu ukhoza kupanga ndalama zokwana \$7,000 pachaka zimene zikhoza kupita ku gawo lofaritsa Uthenga Wabwino.

- Zinthu zofunika:

Bweretsani zinthu zonse zimene mpingo wanu uli nazo ndi cholinga choti mufaritse Uthenga Wabwino. Zinthu zimezi zikhoza kukhala: ndalama, dzida zoyimbira ndi zina zonse zimene zingathandize pofaritsa Uthenga Wabwino.

KUMANANI PAFUPI PAFUPI NGATI A EVANGELISM KOMITI:

Chitsanzo cha dongosolo limene mukhoza popanga mkumano wa komiti ndi ili:

1. Pemphero lotsegulira ndi kuwerenga kwa mau.
 2. Kuwerenga zinthu zimene zinakambidwa mu mkumano wapitao.
 3. Kufotokozera mmene zachuma zayendera.
 4. Kufotokozera mmene zinthu zikuyenera kuchokera kuzigawo.
 5. Zokambidwa kuchokera kwa mkulu oyang'anira zofaritsa Uthenga Wabwino.
 6. Zokambidwa zochokera kwa mkulu oyanga'anira kufaritsa Uthenga mdzik lonse.
- Zolengeza zapadera.
- Kupeza ndalama.
- Mkumamo waukulu wapachaka.
- Zinthu zina zing'ono zing'ono.
7. Zolankhula zomaliza kuchokera kwa abusa.
 8. Pemphero lotsekera.

LANKHULANI NDI MPINGO KOMANSO NDI ANTHU MDERA LANU:

Fotokozerani anthu ndi mpingo, zolinga, dongosolo ndi zinthu zimene mukufuna kuchita pogwiritsa ntchito zinthu izi.

- Wailesi, kanema, ndi nyuzi pepala.
- Ma posta oti amatidwe kunja ka mpingo.
- Mabuku ndi zinthu zina zomvera.

- Timabuku ting'onoting'ono.
- Zolengeza za mu mpingo.
- Makalata apadera olembedwa kupita kwa opembedza.

KUSANTHULA BAIBULO DIZKO LONSE

Kusanthula Baibulo kumathandiza kuti mukhale ndi maonedwe a zinthu malingana ndi Baibulo. Komasa izi zikuthandizani kuti mugawane ndi ena masompheny anu. Zina mwa zinthu zimene mukhoza kutsata posanthula Baibulo ndi izi:

Pamene mukusanthula Baibulo mukuyenera kufunsa mafunso awa.

- Kodi ndimeyi ikuonetsera bwanji chidwi cha Mulungu pa maiko a dziko lapansi?
- Kodi ndimeyi ikuonetsera chiani cha dziko lapansi?
- Kodi ndimeyi ikupereka uthenga ku dziko lapansi.
- Kodi ndime imeneyi ikuonetsa chiani zokhudza cholinga cha Mulungu pa dziko, pa mpingo kapena pa okhulupirira wina aliyense. Ndi zinthu ziti zimene ndime imeneyi ikufuna kuti ndi chite.

KUSANTHULA ANTHU MU BAIBULO.

Werenga nkhani zokhudza nthu a m'Baibulo. Pamene mukuwerenga nkhani zimenezi muyenera kufunsa mafunso awa:

- Kodi ndi ntchito iti imene Mulungu anapereka kwa munthu amane mukuwerenga?
- Kodi ntchito imeneyi ikukwaniritsa bwanji cholinga cha Mulungu pa dziko lapansi?
- Ndi ndi makhalidwe ati a anthu amenewa amene anapangits kuti anthu alephelere kukwaniritsa ntchito yawo imene Mulungu anawapatsa. (Chitsanzo chabwino ndi nkhani ya Abrahamu imene yaikidwa mu gawo la zoonjezera pophunzira)
- Kodi ndi chiani chimene munthu anachita pokwaniritsa zimene Mulungu anawaitanira?
- Chinawapangits ndi chiani kuti achite bwino.
- Kodi anthu amenewa analemphera bwanji?
- Kodi ndi chiani chimene mungaphunzire kuchokera kwa anthu amenewa.

KUSANTHULA BUKU LONSE

Werengani buku lonse la m'Baibulo ndi cholinga choti mupeza maonedwe a dziko malinga ndi Baibulo. Ngati mmene mwaonera mu phunziro lino, Buku lina lilironse la Baibulo likufotokoza choonadi chinachake chokhudza chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi. Pamene mukuwerenga mabuku amenewa, mudzifunse mafunso awa:

- Kodi cholinga cha buku limeneli ndi chiani malingana ndi chikonzero cha Mulungu? Kodi zinthu zimene zalembedwa mu buku iri zikugwirizana bwanji ndi cholinga ndi chikonzero cha Mulungu.
- Kodi anthu amene akuonekera kwambiri mu buku limeneri ndi ati? Santhulani anthu amenewa malingana ndi gawo limene anagwira mu chikonzero cha Mulungu.
- Ndi mavesi ati mu buku limeneli amene akulankhula za dziko lapansi komanso chikonzero cha Mulungu ndi zolinga zake.
- Kodi ndi zinthu ziti zimene zakukhudzani kwambiri zokhudza chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi? Ndipo ndi chiani chimene mungachite kuti mukwaniritse ntchito imeneyi.

CHAPUTALA 11

NDIPO CHIMALIRIZILO CHIDZABWERA

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziro ili, muyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba vesi yotsogolera osaonera.
- Kufotokozerana zinthu zikuluzikulu zimene zidzachitike chimaliziro chisanafike komanso mathero a chikonzero cha Mulungu.
- Kufotokozerana mwachidule zinthu zikuluzikulu zimene zidzachitike chimaliziro chisanafike komanso mathero a chikonzero ha Mulungu.

VESI YOTSOGOLERA

Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)

CHIYAMBI

Chaputala choyamba cha phunziro ili chinafotokozerana chiyambi cha dziko lapansi.

Kuchokera pamenepa, mwaona masomphenya a Mulungu mu mbiri yonse ya dziko komanso Chipangano Chakale ndi Chatsopano kufira nyengo ya mpingo mpaka lero.

Koma kodi Baibulo limaphunzitsa chiani zokhudza tsogolo la dziko? Yesu anakamba za chimariziro cha nthawi, koma kodi izi zimatanthauza chiani? Chaputala ichi chikuyankha mafunso amenewa komanso chikamba zinthu zochitika kumapeto kwa dziko ndi mathero a zinthu zonse.

CHINTHU CHACHIKULU.

Yesu anawalonjeza ophunzura izi:

M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali kutero, ndikadakuuzani inu; pakuti ndipita kukukonzerani inu malo. Ndipo ngati ndipita

kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso. (Yohane 14:2-3)

Yesu analonjeza kuti adzabweranso pa dziko lapansi kwa okhao amene ndi obadwa mwatsopano ndi cholinga choti adzawetengere kumalo amene awakonzera.

Nthawi yeniyeni sitimaidziwa, koma Yesu analankhula zinthu zikuluzikulu zimene zidzaonetsere kuti nthawi yayandikira.

Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu h mitundu yonse; ndipo pomwepo cidzafika cimariziro. (Mateyu 24:14)

Chinthu chachikulu chimene chidzachitike chimaliziro cha nthawi chisanafike ndi chakuti uthenga udzafarikira paliponse. Kodi ndi udindo wanji umene tiri nawo pofaritsa Uthenga umeneu?

Muphunziro lino taphunzira kuti ndi udindo wa mpingo komanso wa wina aliyense pokwaniritsa zinthu zimenezi. Ndipo taphunziranso kuti uthenga umene ukuyenera kufaritsidwa ndi uthenga wa Ufumu wa Mulungu. Koma kodi chimaliziro chimene Yesu amachikamba chija ndi chiti? Chimaliziro ndi mathero a dziko lapansi limene tikulidziwari. Ndi mapeto a chikonzera cha Mulungu pa maiko a dziko lapansi.

ZOLEMBEDWA ZAUNENERI

Mulungu sanaonetsera kanthu kena kalikonse kokhudza chimariziro cha nthawi. Iye sanapereke mndandanda wa zinthu mmene zikuyenera kuchitikira. Mau oti uneneri amathauza kulankhula zinthu zamtsogolo. Uneneri wa Baibulo uli magawo angapo:

1. Uthenga olankhulidwa kuchokera kwa Mulungu.
2. Kulosera zochitika mtsogolo malingana ndi chikonzera cha Mulungu.
3. Kutanthauzira kwa munthu zinthu zimene Mulungu amachita.

Maulosi akuluakulu okhudza tsogolo la dziko lapansi amapezela mu mabuku a Danieli ndi Chivumbulutso. Pali ndime zapadera ngati Mateyu 24 ndi I Atesalonika 4:13-18 zimapereka

chidziwitso chowonjezera. Kuchokera mu ndimene zimenezi, tikhoza kuphunzira zimene Mulungu wavumbulutsa zokhudza chimaliziro cha nthawi.[§]

ZIMENE ZABVUMBULUTSIDWA

Chidule cha zimene Mulungu waonetsera mumalemba zokhudza chimaliziro cha dziko lapansi.

KULARIKIDWA KWA UTHENGA WA UFUMU WA MULUNGU

Izi zikuyenera kukwaniritsidwa chimaliziro chisanafike (Mateyu 24:14)

MKWATURO

Pamene uthenga wa Ufumu wa Mulungu walalikidwa kwa anthu onse, Yesu adzabwera kudzatenga okhulupirira. pa I Atesalonika 4:13 ndi 18 akufotokoza mwatsatanetsatane mmene mkwatulo udzachitikire. Mau oti mkwaturo mu Baibulo mulibemo, koma tanthauzo la mau amenewa limapezeka: Kuchokera mu ndime imeneyi, tikuphunzira kuti:

- Yesu mwini adzabweranso (vesi 16)
- Padzakhala chiukitso cha okhulupiira amanene anafa (vesi 16).
- Kudzakhala mkwaturo umene ndi mchitidwe omuchotsa munthu kuchoka malo amadzi kupita malo ena. Okhulupirira amoyo dzatengedwa ali amoyo kumka nawo kumwamba (vesi 17).
- Padzakhala kuyanjana pakati pa okhulupirira amene anafa andi amene ali ndi moyo pa nthawi imene ambuye adzabwerenso kachiwiri. (vesi 17).
- Anthu ena amakhulupirira kuti mkwaturo udzachitika chizunzo chachikulu chisanafike. Chifukwa cha ichi, iwo amati okhulupirira sadzakumana ndi mazuzo pa dziko lapansi. Pamene ena amati mkwaturo udzachitika mkati mwa chizunzo. Enanso amati mkwaturo udzachitika kumapeto kwa chizunzo. koma ganizo limene ndi lodziwika bwimo lomwe ndi

[§] Chaputala 20 cha Phunziro la Haverstine International lotchedwa “Ukadaulo wakasanthulidwe ka Baibulo imapereka ndondomeko za kasanthuridwe ka Mabuku a Ulosi.

lakuti mkwaturo kwa okhulupirira udzachitika chizunzo chisanafike. Maganizo osiyana amabwera chifukwa chakamasuridwe kosiyana ka Baibulo. Koma nkhani yaikulu ndi yakuti palibe amene amadziwa za nthawi yeniyeniyo kupatula Mulungu Tate (Mateyu 24:36). Chinthu chimene chili chofunika kwambiri ndi kuzindikira kuti ndinu okhulupirira weniweni komanso kukhala okonzeka kupita ndi Yesu pamene adzabwera kudzatenga ake.

CHIZUNZO:

Anthu ena sadzakodwa powona Yesu akubwera:

Taonani, adza ndi mitambo; ndipo diso liri lonse lidzampenya iye, iwonso amene anampyoza; ndipo mafuko onse a pa dziko adzamlira iye. Terotu.

(Cibvumbulutso 1:7)

Chifukwa cha uchumo adzakumana ndi chizunzo chachikulu pa dziko. Izi zidzachitika okhulupirira atakwaturidwa kale.

- Chizunzo chidzachitika kwa miyezi makumi anayi ndi iwiri (Danieli 9:24-27)
- Iyi idzakhakhala nthawi yowawitsa kwambiri. Pakhala nyengo zingapo zowawitsa pa dziko lapansi, koma pali zinthu zingapo zimene zidzasiyanitse chizunzo ndi nthawi zimenezi:

Choyamba: chizunzo chidzachitika dziko lonse lapansi osati dera limodzi lokha ayi
(chivumbulutso 3:10)

Chachiwiri: anthu adzazondikira kuti chimariziro cha nthawi chayandikira
(Chivumbulutso 6:16)

Chachitatu: kukula kwa chizunzo kudzakhala kwakukulu kumenen sikunachitikepo
(Mateyu 24:4-14)

Pali magawo a chiweruzo cha Mulungu chimene chidzaperekedwe pa dziko lapansi nthawi ya chiweruzo. Izi zikufotokozeredwa mu buku la chivumbulutso ma chaputala a 6,8,9 ndi Mateyu 24:4-14. Chiweruzo chimenechi chikugwera anthu amayi ndi abambo onse amene anamkana Yesu.

MELENIYAMU:

Baibulo limkamba za dzaka 1000 zimene Yesu adzalamulire pa dziko lapansi chitatha chizunzo (Zakariya 14:9; Danieli 7:14) Mzinda wa Yerusalemu ndiy lidzakhale likulu la ulamuliro umeneu(Yesaya 2:3) Nyengo imeneyi idzatha pamene Satana adzaukire komaliza(Chivumbulutso 20:7-9) Koma Mulungu adzatumiza moto kuchokera kumwamba pofuna kuthana ndi onse otsutsana naye. Ndipo Satana adzaponyedwa mu Nyanja ya moto kwa moyo wake onse. (Chivumbulutso 20:10)

CHIWERUZO:

Onse amene anafa ali osakhulupirira adzaukitsidwa ndi cholinga choti aweruzidwe. Chifukwa chakuti sanalape machimo awo, iwo adzaponyedwa ku moto kwa moyo wao onse. (Chivumbulutso 20:12-15) okhulupirira eneeni amene analapa machimo awo ndi kuvomereza Yesu ngati mpulumutsi wao adzakhala moyo wao onse pamaso pa Mulungu kumwamba.

KUONONGEDWA KWA DZIKO LAPANSI:

Baibulo limafotokoza zakunongedwa kwa dziko lapansi ndi moto:

Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala; m'mene miyamba idzapita ndi cibumo cacikuru, ndi zam'mwamba zidzakanganuka ndi kurentha kwakukuru, ndipo dziko ndi nchito ziri momwemo zidzarenthedwa. (Petro 3:10)

Nthawi imene tikuidziwa sidzakhala onso ayi chifukwa tidzakhala muyaya pamaso pa Mulungu: Ndipo mngelo amene ndinamuona alikuimirira panyanja ndi pa mtunda, anakweza dzanja lace lamanja kuloza kumwamba, nalumbira kuchula iye amene ali ndi moyo ku nthawi za nthawi, amene analenga m'mwamba ndi zinthu ziri momwemo, ndi dziko lapansi ndi zinthu ziri momwemo, ndi nyanja ndi zinthu ziri momwemo kuti sipadzakhalanso nthawi: (Chivumbulutso 10:5-6)

KUKWANIRITSIDWA KWA CHOLINGA CHA MULUNGU;

Kumbukirani cholinga cha Mulungu chimene mwaphunzira kale?

Anatizindikiritsa ife cinsinsi ca cifuniro cace, monga kunamkomera ndi monga anatsimikiza mtima kale mwa iye, kuti pa tnakonzedwe a makwaniridwe a nyengozo, akasonkhanitse pamodzi zonse mwa Kristu, za kumwamba, ndi za padziko. (Aefeso 1:9-10)

Ndipo mngelo wacisanu ndi ciwiri anaomba, ndipo panakhala mau akulu m'Mwamba, ndi kunena, Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu, ndi wa Kristu wace: ndipo adzacita ufumu kufikira nthawi za nthawi. (Cibvumbulutso 11:15)

Ndipo colengedwa ciri conse ciri m'mwamba, ndi padziko, ndi pansi pa dziko, ndi m'nyanja, ndi zonse ziri momwemo, ndinazimva zirikunena, Kwa iye wakukhala pa mpando wacifumu, ndi kwa Mwanawankhosa zikhale ciyamiko, ndi ulemu, ndi ulemerero, ndi ufumu, kufikira nthawi za nthawi. (Cibvumbulutso 5:13)

PAMASO PA MPANDO WACHIFUMU

Mulungu adzalenga kumwamba ndi dziko lapansi latsopano. Zambiri za izi zikufotokozeredwa pa chivumbulutso 21 ndi 22. Anthu onse okhulupirira adzasonkhanitsidwa pamodzi ndi Mulungu owona mmodzi yekhayo.

Zitatha izi ndinapenya, taonani, khamu lalikuru, loti palibe munthu anakhozakuliwerenga, ocokera mwa mtundu uti wonse, ndi mafuko ndi anthu ndi manenedwe, akuimirira ku mpando wacifumu ndi pamaso pa Mwanawankhosa, atabvala zobvalazoyera, ndi makhwatha a kanjedza m'manja mwao; ndipo apfuula ndi mau akuru, nanena, Cipulumutso kwa Mulungu wathu wakukhala pa mpando wacifumu, ndi kwa Mwanawankhosa. Ndipo angelo onse anaimirira pozinga mpando wacifumu, ndi akulu, ndi zamoyozo zinai; ndipo anagwa nkhope yao pansu ku mpando wacifumu, nalambifa Mulungu, ndi kunena, Amen: Thamo ndi ulemerero, ndi nzeru, ndi ciyamiko, ndi ulemu, ndi cilimbiko, ndi mphamvu zikhale kwa Mulungu wathu kufikira nthawi za nthawi. Amen. (Cibvumbulutso 7:9-12)

Anthu onse, amayi ndi abambo amitundu yonse, zinenero zonse adzasonkhana pa mpando wachifumu wa Mulungu. Koma pamene tikuona chithunzithunzi cha chikondwewero kumwamba, tisayiwale kuti ndi okhao amene:

Pakuti, amene ali yense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.

(Aroma 10:13)

KOMA:

Ndipo iwo adzaitana bwanji pa iye amene sanamkhulupirira? ndipo adzakhulupirira bwanji iye amene sanamva za iye? ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? ndipo adzalalikira bwanji, ngati satumidwa? monganso kwalembedwa, Okometsetsa ndithu ali mapazi a iwo akulalikira Uthenga Wabwino wa zinthu zabwino. (Aroma 10:14-15)

Mwaphunzira mmene Baibulo limaonera dziko lapansi. Mwaliona dziko lapansi malinga ndi mmene Mulungu amalionera.

Tsopano kodi udindo wanu waukulu ndi uti?

MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera osaonera.

2. Kodi chinthu chachikulu chimene chiyenera kuchitika chimariziro chisanafike ndi chiani?

3. Kodi ndi mabuku ati awiri a m'babulo amene amafotokoza uthenga wambiri okhudza chimariziro cha dziko lapansi komanso pamathero pa chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi?

_____ ndi _____

4. Kodi ndi pati pamene timapeza tsatanitsatani wa mkwaturo?

5. Kodi ndi pati pamene timapeza zambiri zokhudza kumwamba ndi dziko lapansi latsopano?

6. Kodi ndi ma vesi ati amene amafotokoza mmene dziko lapansi ndi lakumwamba lidzaonongerredwe?

7. Fotokozerani mwachidule zinthu zimene zidzachitike kumapeto kumapeto kwa nthawi komanso pachimake pa chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi.

(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa bulu limeneri)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA:

1. Werengani zambiri zimene Mulungu anavumbulutsa zokhudza chimariziro cha nthawi:

- Werengani buku la Danieli ndi Chivumbulutso.
- Werengani Mateyu 24.
- Werengani I Atesalonika 4:13- 18 ndi II Petro 3:10.

2. Buku la Chivumbulutso limakamba za chimariziro cha nthawi komanso mapeto a chikonzero cha Mulungu pa dziko lapansi. Mu chaputala chapita, tinaona za dziko lapansi mu mau a Mulungu, koma sitinafike mu buku la Chivumbulutso.

Buku la chivumbulutso liri ndi zinthu ndime zina zokhudza chimariziro cha nthawi.

Ndipo ndime ziri munsimuzi zikupita ku maiko kapena mafuko a dziko lapansi.

- Yesu ndi Karonga wa mafumu a dziko lapansi 1:5.
- Kubweranso kwa Yesu Khristu 1:7.
- Malonjezano ku mafuko onse 2:26, 3:10.
- Kulalikira komaliza ndi kholora lomaliza la dziko lapansi 14:6-7, 15-19
- Mathero a dziko lapansi 10:5-6; 11:15; 13:8; 17:8
- Kufotokozera kwa kumwamba ndi dziko lapansi zatsopano ndi zinthu zochitika malo amenewa: 5:9-10,13; 7:9-11; 15:4, Chaputala 21 ndi 22(zikutchula mafuko a dziko lapansin 21:24,26; 22:2)

MAYANKHO AMAFUNSO ODZIYENSA NOKHA

CHAPUTALA 1

1. PACIYAMBI Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi. (Genesis 1:1)
2. Mulungu yekhayo weniweni wavumbulutsidwa mu Baibulo.
3. Zifukwa ziwiri zokhalira ndi khani zosiyana za chiyambi cha chilengedwe ndi izi: chifukwa chakuti anthu analibe chidziwitso cha zoonadi zake za chilengedwe komanso ena anasnkha kusakhulupirira za nkhani yoonadi ya chilengedwe ataimva.
4. Anthu ana samavomereza choonadi chake cha nkhani ya chilengedwe chifukwa chakuti iwo amadziwa kuti akatero ndiye kuti akuyenera kuvomereza kuti kuli Mulungu mmodzi. Ngati angavomereze kuti pali Mulungu mmodzi, ndiye kuti akuyenera kuvomerezanso ulamuliro wake pa iwo. Akueyeneranso kuvomereza mau ake ndi kuchitapo kanthu pa makhalidwe awo. Chifukwa chakuti anthu anthu samafuna kusintha makhalidwe awo, iwo amakana zimene Baibulo limafotokoza komanso kuti Mulungu alipo.
5. Pamene tikukamba za kukuza maonedwe a zinthu malingana ndi Baibulo ndiye kuti tikutanthauza kuti maganizo anthu akuyenera kukhazikika pa zimene Baibulo limafotokoza.
6. Onani mdandanda umene waperekedwa mu chaputala 1.
7. Munthu ndi osiyana ndi zolengedwa zonse zimene Mulungu analenga chifukwa chakuti Munthu analengedwa mu Chifanizo cha Mulungu komanso kuti ali ndi moyo wamuyaya. Iye ali ndi kuthekera kotha kulankula ndi anthu ana.
8. Werenga kufotokozeredwa mwachidule za kugwa kwa munthu mu chaputala 1.
9. Werenga zotsatira za kugwa kwa munthu mu chaputala 1.
10. Genesis 3:15.
11. Dziko lakuthupi ndi lauzimu.

CHAPUTALA 2

1. Ndipo Yehova anati, Taonani, anthu ali amodzi, ndipo onse ali naco cinenedwe cao cimodzi; ndipo ici ayamba kucita: ndipo tsopano palibe kanthu kakuletsedwa nao kamene akafuna kucita. Tiyeni, titsike, pomwepo tisokoneze cinenedwe cao, kuti wina asamvere cinenedwe ca mnzace. (Genesis 11:6-7)
2. Dziko linagawikana pakati pa anthu a zilankhulo sosiyanasiyana pa nsanja ya Babulo.
3. Anthu amene amalankhula chilankhulo chimodzi anabwera pamodzi. Izi zinapangitsa kuti pakhale anthu amitundu yosiyanasiyana.
4. Pamane mitundu ya anthu imakula, iwo amasamukira madera osiyanasiyana a dziko lapansi. Pakudutsa kwa nthawi, anthu amenewa anapanga maiko kapena kuti mafuko osiyanasiyana. Izi zinapangitsa kuti pakhale malire komanso malamuro osiyanasiyana pakati pa anthu osiyanasiyananso.

CHAPUTALA 3

1. Ndipo 7 anawatsegulira mitima yao, kuti adziwitse malembo; ndipo anati kwa iwo, 8 Kotero kwalembedwa, kuti Kristu amve zowawa, nauke kwa akufa tsiku lacityatu; ndi kuti kulalikiidwe m'dzina lace kulapa ndi 9 kukhululukidwa kwa macimo kwa 10 mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu. (Luka 24:45-47)
2. Chifunguro cholowa pena palipoonse nd Luka 24:45-47.
Mfundi ziwiri zikulu zikulu zoperekedwa mu chifungurochi ndi:
choyamba: “Khristu akuyenera kuzuzidwa ndi kuuka kwa kufa”
Chachiwiri: “kulapana ndi chikhululukidwa cha machimo zilarikidwe mu dzin lake”
3. Ndime ya m’baibulo imene imafotokoza cholinga cha Mulungu pa dziko lapansi ndi Aefeso 1:9-10 ndi 3:11.

4. Cholinga cha Mulungu chamuyaya ndi chakuti akabweretse anthu ochimwa onse kwa iye yekha kudzera mwa Yesu Khristu.
5. Munda wa kholora.

CHAPUTALA 4

1. Pakuti kuyambira kotulukira dzuwa kufikira kolowera kwace dzina langa lidzakhala lalikuru mwa amitundu; ndipo m'malo monse adzaperekera dzina langa cofukiza ndi copereka coona; pakuti dzina langa lidzakhala lalikuru mwa amitundu, ati Yehova wa makamu. (Malaki 1:11)
2. Uthenga waukulu ndi okhudza kukhudzika kwa Mulungu ndi chikonzero cha chichipulumutso cha Mulungu pa dziko lapansi.
3. Fananitsani kufotokoza kwanu ndi kufotokoza kumene kukupezeka pa chaputala 4.
4. Fananitsani kufotokoza kwanu ndi kufotokoza kumene kukupezeka pa chaputala 4.
5. Fananitsani kufotokoza kwanu ndi kufotokoza kumene kukupezeka pa chaputala 4.
6. Fananitsani kufotokoza kwanu ndi kufotokoza kumene kukupezeka pa chaputala 4.

CHAPUTALA 5

1. Ine ndalemekeza Inu pa dziko lapansi, m'mene ndinatsiriza nchito imene munandipatsa ndicite. (Yohane 17:4)
2. Chikonzero cha Mulungu chofuna kupulumutsa dziko lonse lapansi chinaonetseredwa ndi zolakhula za mngero, Mariya komanso simoyoni ndi anthu ena. Pakulengezedwa za kubadwa kwake, cholinga chofuna kuyanjanitsa anthu onse ndi Mulungu zimatchuridwa.
3. Fanananitsa kufotokozerana kwanu ndi zimene zakambidwa pa chaputala 5.
4. Fanananitsa kufotokozerana kwanu ndi zimene zakambidwa pa chaputala 5.
5. Ndi kudzera mu imfa ya Yesu pamtanda imene inamuyanjanitsa munthu ndi Mulungu amene ali olungama.

6. Iye anakwanitsa cholinga chimene anabwelera ku dziko lapansi chimene ndi kuyanjanitsa Mulungu amene ndi olungama ndi munthu ochimwa. Pakuchita zinthu izi chikonzero cha Mulungu chinakwaniritsidwa.

CHAPUTALA 6

1. Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezere ace a dziko. (Macitidwe 1:8)
2. Kutumidwa kwakulu ndi lamuro limene Yesu anapereka kwa ophunzira ake kuti akafaritse uthenga wabwino pa dziko lonse lapansi.
3. Ndime zitatu zonsezi zikhoza kugwiritsidwa ntchito: John 20:21-23; Acts 1:8; John 15:16; Luka 24:45-49; Marko 16:14-16; Mateyu 28:16-20.
4. Mpingo ukhoza kufotokozeredwa mu magawo awiri awa:

Mpingi wa dziko lonse: mpingo ndi gulu la anthu onse amene amakhulupilira Yesu Khristu. Ndi chiyanjano cha anthu okhulupirira amene anabadwanso mwatsopano ndipo amakhala moyo omvera Mulungu. Mau oti mpingo amatanthauza gulu la anthu amene ayitanidwa. Kotere mpingi ndi gulu la anthu amene ayitanidwa kuchokera ku ku fumu wa Satana ndi kulowa mu Ufumu wa Mulungu ndipo mpingo umapangidwa ndi anthu a mitundu, zikhalidwe ndi zilankhuro zosiyanasiyana.

Mpingo wa mdera: pa zolinga zofuna kuchitsa chiyanjano komanso ndi anthu ena, anthu ayenera kubwera pamodzi ndi anthu ena.

5. Mpingo unayamba pa tsiku la Pentekoste pa Machitidwe 2. Unabadwa pa chiwonetsero cha mphamvu ya Mulungu.
6. Mphamvu ya Mzimu Woyera.

7. Okhulupirira ayenera kukhala limodzi ngati abale ndi alongo apa banja limodzi. Iwo ayenera kutumikira ngati mmene thupi ligwilira ntchito limodzi, ndi Khristu ngati mutu wa thupi limeneli. Mulungu amapereka utsogoleri wapadera komanso mphatso zapadera mu mpingo ndi cholinga choti mpingo uthe kutumikira.
8. Mpingo uli ndi ntchito zambiri zimene zina mwa izo ndi izi: kupembedzera, kutimikira zosowa za munthu, ndi kuchita chiyanjano. Koma cholinga chenicheni cha mpingo ndi kufaritsa Uthenga Wabwino kapena kuti kukwaniritsa kutumidwa kwakukulu.
9. 1 Akorinto 15:1-11 amafotokoza nsanamira zikulu zikulu za Uthenga Wabwino. Uthenga waukulu ndiye Yesu Khristu, utumiki wake, imfa yake chifukwa cha machimo athu. Mwachidule tikhoza Kunena kuti Uthenga Wabwino ndi Yohane 3:16 ndi Yohane 14:1, Mateyu 11:28 ndi Aroma 10:9. Tanthauzo lake lalikulu ndi zonse zimene Yesu anaphunzitsa zokhudza ufumu wa Mulungu.

CHAPUTALA 7

1. Pomwepo ananena kwa ophunzira ace, Zotuta zicurukadi koma anchito ali owerengeka. (Mateyu 9:37)
2. Fananitsani zimene mwafotokoza ndi zimene zikupezeka pa chaputala 7.
3. Gulu la anthu kapena mtundu wa anthu ndi gulu limene lumakhala zinthu zofanana zimene zikhoza kukhala chilankhulo, chikhalidwe kapena malo amodzi okhala.
4. Gulu la anthu osafikiridwa ndi anthu amene pakati pawo palibe okhulupirira okwanira amene angathe kufaritsa Uthenga wabwino.
5. Anthu ofikiridwa ndi gulu la anthu amene amene pakati pawo pali okhulupirira okwana amene ali ndi zinthu zowayenereza kufaritsa uthenga Wabwino mdera lawo opanda kudalira gulu lo anthu ochokera kwina.
6. Magulu asanu amene sanafikiridwe ndi awa: Asilamu, Mahindu. Ma chinise, anthu a Chibuda ndi anthu amitundu yosiyanasiyana.

7. Dziko lotsekedwa ndi dziko limene silimalola anthu atumiki kuti alowe mudziko limeneli. Ndi dziko limene limakhala ndi malamuro oyendetsa chipembedzo cha anthu ake. Kumaiko ena ndi zoletsedwa kutembenuza anthu.
8. Chiganizo chimenechi ndi cholondola.

CHAPUTALA 8:

1. Inu simunandisankhe Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala cipatso, ndi kuti cipatso canu cikhale; kuti cimene ciri conse mukapempha Atate m'dzina langa akakupatseni inu. (Yohane 15:16)
2. Akhristu a dziko lonse lapansi ndi gulu la okhulupirira a dziko lapansi lonse amene amchokera ku zikhalidwe, zinenero komanso mipimngo yosiyanasiyana. Chinthu chimodzi chimene chimayanjanitsa anthu amenewa ndi kudzipereka kwao kofuna kukhala khristu wa dziku lonse.
3. Mpingo oyamba unafikira dziko lonse lapansi pogwiritsa ntchito ndondomeko ya kuchulukitsa imene yafotokozeredwa pa II Timoteyo 2:2. Nkhristu wina aliyense amabala zipatso komanso kuti khomo lina lilironse linali malo ofaritsira Uthenga Wabwino.
Funso limeneli likufunika kuti musainire ngati chizindikiro chodzipereka.

CHAPUTALA 9

1. Pakuti nyumba yanga idzachedwa nyumba yopemphereramo anthu onse. (Yesaya 56:7)
2. Opembedzera ndi mkhala pakati wa munthu wina. Timapembedzera maiko ena popemphelera maiko amenewa. Izi ndi zimene timatanthauza tikakamba za kupembedza kwa dziko lonse. Pamene tipambedzera, timakhala tikufunafuna Mulungu mmalo mwa anthu ena. Kapena kuti timatula zinthu zopempha mmalo mwa maiko.
3. Njira zophunzitsira opembedzera wa dziko lonse ndi izi:
Choyamba: fotokozeramaonedwe a zinthu malingana ndi Baibulo.

Chachiwiri: werengani chaputala 9, potsata ndondomeko zakupemphera, khazikitsani mlozo wakupemphera.

4. Ngati yankho lanu ndi inde, ndiye kuti mwakwanitsa zolinga za chaputala chimenechi.
5. Ngati yankho lanui ndi inde, ndiye kuti mwakwanitsa zolinga za chaputala chimenechi.
6. Kupembedzera kumapezeka m'Baibulo.

- Pemphero ndi chinthu chimene anthu onse amadalira.
- Kupemphelera dzikolonse kulibe malire.

7. Dongosolo la pemphero likuyenera kukhala ndi zinthu izi:

- Kuyamika Mulungu (mpindi 10)
- Kupembedzera dziko lonse lapansi (mpindi 10)
- Kupembedzera chigawo cha dziko lapansi (mpindi 10)
- Kupemphelera ma bugwe a ofaritsa mau kapema anthu otumidwa (mpindi 10)
- Pemphero kwa anthu amene sanafikiridwe (mpindi 10)
- Pemphero lapadera lokhudza zosowa zanu.

CHAPUTALA 10.

1. Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)
 2. Amayi ndi abambo onse okhulupirira.
 3. Kukhala chitsanzo cha masomphenya.
- Kufotokozera anthu ena masomphenya.
 - Masomphenyawo akhale chinthu chofunika kwambira pa moyo wanu.
 - Kumvera masomphenya.

4. Ndinu nokha amene mukhoza kuyankha funso limeneli ngati simunapange chiganizo choti mumvere masomphenya, pititirizani kufunafuna ambuye mpaka mutatero. Ichi ndiye cholinga chenicheni cha chaputala chimenechi komanso phunziro lonseri.

CHAPUTALA 11

1. Ndipo aneneri onama ambiri adzauka, nadzasokeretsaanthuambiri. (Mateyu 24:11)
2. Kufaritsa Uthenga Wabwino kwa anthu onse a dziko lapansi.
3. Buku la Chivumbulutso ndi Danieli.
4. I Atesalonika 4:13-18.
5. Chibvumbulutso chaputala 21 ndi 22.
6. II Petro 3:10.
7. Fananitsani kufotokozero kwanu mwachidule ndi zimene zalembedwa mu chaputala 11.